



Nkhondo Za Kudziwika

Nsewu waku Ufulu

Adrian Ebens

Nkhondo Za Kudziwika

Adrian Ebens

Copyright © 2018 Adrian Ebens
Losindikizidwanso kuchokera kuzolemba zam'mbuyomu

Duracell® ndiya Procter & Gamble Co. ndipo ndiyolembetsedwa ku Amereka ndi mayiko ena. Maumboni ku Duracell® mu nkhanayi cholinga chake ndi umboni, ndipo musatanthauzire kapena kukhuzana ndi Duracell® chipango, kapena kampani yake yayikulu, Procter & Gamble.

Baibulo logwiritsidwa ntchito m'Bukuli ndi Buku Lopatulika ndilo Mau a Mulungu.

Lotsindikitsidwa ku Australia ndi Maranatha Media
(Akudza Ambuye Ofalitsankhani)
Tatewachikondi.com
adrian@identitywars.org

Zamkati:

Gawo Loyamba. Maufumu Awiri - Kudziwika Kotayika

1. Mtengo wa Batire Lolimba..... 4
2. Kasupe Wa Moyo 11
3. Pafupi ndi Mtima wa Mulungu 20
4. Ufumu wa Banja..... 24
5. Vuto mu Banja 28
6. Gehena pa Dziko 34
7. Mnzere Wa Moyo Wakumwamba 43
8. Kufanaiza Ma Ufumu Awiri..... 50
9. Mtima Wa Babulo 55

Gawo Lachiwiri. Tsogolo Limodzi - Kudziwika Kubwezeretsedwa

10. Kudula Nsinga za Mtengo Wa Batire Lolimba 62
11. Kutsegula Zipata Za Kumwamba..... 71

Gawo La Chitatu-Ulendo Obwerera Ku Umwana

12. Moyo Oyendetsedwa Ndi Mtengo Wa Batire Lolimba 77
13. Makwerero Opita Kumwamba..... 82
14. Milungu Yofanana, Maina Osiyana..... 88
15. Mukuwerenga Bwanji?..... 96
16. Osakhalanso Kapolo 101
17. Kugwa Kwa Babulo 106

Bukuli ndi la ulemu kwa

Bambo anga okonedwa Abel,
omwe anandiphunzitsa kuima njo,
nthawi zonse kukhulupirika,
kumaliza chomwe wayamba,
ndi kusalolera chisalungamo.

Mai anga okonedwa Evelyn,
omwe anandiphunzitsa
ine kumalotabe, kudziwa kupanga zinthu,
kukonda chirengedwe,
ndi kukhala opereka.

Mchemwali wanga okonedwa Karen,
yemwe tagawana ulendo wa chibwana ndi ine
ndi nthawi zambiri kugwiritsa mwachangu nzeru zake
kupanga ine kuti ndiseke.

Gawo Loyamba. Maufumu Awiri

- Kudziwika Kotayika

1. Mtengo wa Batire Lolimba

Chipinda chinali chowunika mothima. Limodzi mwa makoma panali zikwangwani zingapo, chithunzi cha woyimba nyimbo za pop ndi china cha wamasewera wotchuka. Pambali pa nkhoma lina panali tebulo pomwe panali mabuku ndi makope aku sukulu ndipo pakati pa tebulo panali choyimbira chaching’ono koma champhamvu. Zowonadi chipindachi chinali cha wachinyamata woonesa zizindikiro za zikhumbo, kugwedezekagwedezeka ndi inde, wamaloto.

Munali nkhondo yayikulu m’mtima mwanga, nkhondo ya mathero, nthawi ya choonadi. “Sindinaganizire kuti ndingachite china chake mmene ndinachitira”. Ndinalingalira pamene ndinayang’anitsa pansi. Maganizo anga a ndekha anayetsedwa kwambiri. Nkhondo yinali yayikulu kwambiri moti ndinafunafuna chitonthozo kuchokera ku zikwangwani zomwe zinandithandiza nthawi zambiri kumbuyoku kuchotsa malingaliro anga kuchokera ku zokolola zomwe tsopano ndikututa.

Mpweya unadzadza ndi m’lingaliro wotsimidwa. Malingaliro anga amagwira zizindikiro zoti zimayenda mkhalidwe langa lotanganidwa: maphunziro, masewero, zomveka zinali zina zomwe zimandigwira, koma tsopano zimaoneka zopanda mphamvu kundithandiza. Mtambo wodwalitsa

unanditsikira ndi kuyamba kufinya m'lingaliro wanga wa zokhumba. Zinatsegula malo amphoto m'mtima ndi kuba chuma chawo, ndiyeno kupanga chipinda chopatulika cha zonse - **chiyembekezo**.

Ndinayankhula ndi amayi anga m'njira yoti ndinalonjeza ndekha sindizateronso. Uwu unali mtengo womaliza umene unandipanga kuzindikira kuti sim'mene ndimafuna kukhalira. Sindinazikonde ndekha, ndipo ndinafuna kusintha, koma zinaoneka zopanda chiyembekezo.

* * *

Kukhumudwa. Kukhumudwa ndi temberero limodzi lalikulu likusautsa anthu athu lero. Bungwe Lathanzi la Dziko lonse (WHO) likunena:

Kukhumudwa ndi chotsogolera chopangitsa kudwala ndi kulumala dziko lonse lapansi. Kuposa mazana atatu azikwi (300,000,000) a anthu tsopano akukhala ndi kukhumudwa, kuwonjeza kopitirira magawo khumi asanu ndi atatu pa zana limodzi (18%) pakati pa 2005 ndi 2015.¹

Yesani kumvetisa kuchuluka kwa vutoli mu chiwerengero chotsatirachi kuchokera 2011:

- Miliyoni limodzi (1,000,000) amazipha chaka chiri chonse. Imfa imodzi m'mphindi makumi anayi kapena kunena kuti zikwi zitatatu (3000) pa tsiku.
- Ali yense wa iwo wotenga moyo wake, pafupifupi makumi awiri (20) amayesa kupanga choncho. Ichi ndi zikwi makumi asanu ndi limodzi (60,000) pa tsiku.
- Pa dziko lonse, chiwerengero cha wozipha chikukula ndi makumi asanu ndi limodzi pa zana limodzi (60%) pa zaka makumi asanu zapitazi - makamaka mu mayiko wokwera.
- Makhumi asanu ndi limodzi pa zana limodzi (60%) pa wozipha onse zimachitika ku maiko a chimwenye (Asia). China, India ndi

¹ http://www.who.int/mental_health/management/depression/en/

Japan amawerengedwe pafupifupi makumi anai pazana limodzi (40%) pa wozipha onse, mogwirizani ndi WHO ²

Chikuchitika ndi chani pa dziko? Ndichani chikupangitsa kukhumudwa za moyo kuti mazanama a anthu akusankha kufa kusiyana ndi kuona tsiku lina?

Mu buku lotchedwa Sewero la Malingaliro (*The Mind Game*), Phillip Day akupereka vumbulutso ponena:

Mu nthawi zapita, achibale mubanja amabwera kwa wodwala wokhumudwa ndikumulimbikitsa ndi kukambirana mavuto ake. Lero, ndikuphwasuka kwa m'gwirizano wa banja, kusokonekera chipembezo, kusiyana kwa mabanja ambiri kwa lina ndi linzake ndi mayendedwe wotopetsa a moyo wa zaka mazana awiri makumi awiri ndi limodzi (21st century), wofufuza zosokoneza malingaliro (psychoanalysis) angotenga ntchito yolangiza yomwe amagwiritsa ntchito posamalira achibale kapena mtumiki mu dera lawo. Ndimakhulupirira kwambiri kuti izi zakhala ndi zotsatira zoipa pa anthu.³

Phillip Day akundandalika mfundo zitatu: (1) Kuphwasuka kwa mgwirizano wa banja; (2) Kusokonekera chipembezo; (3) Kusiyana kwa mabanja ambiri kwa lina ndi linzake chifukwa cha mayendedwe wotopetsa a moyo a mazana awiri makumi awiri ndi limodzi. Mfundo yayikulu ndi kuphwasuka kwa mgwirizao wa banja. David Van Biema kuthirira ndemanga pa phunziroli ananena motere:

Mubadwo wosiyana wina uli wonse wabwera, m'mene mazanamazana ali ndi chidzindikiro kwambiri cha zisoni zoyambirira. Ndi ana wosiyana banja. Iwo ali patsogolo chabe pa gulu losatha.⁴

Jim Conway mu buku lake *Adult Children of Legal and Emotional Divorce* akufotokoza momveka bwino za ululu ndi imfa avutika zikwizikwi amene

² <https://www.medicalnewstoday.com/articles/234219.php>

³ Phillip Day, Introduction-<http://www.campaignfortruth.com/Eclub/100702/depressioandsuicide.htm>

⁴ David Van Biema, "Learning to Live with a Past that Failed," *People*, May 29, 1989, p.79

amavutika ndi zotsatira za kuphwasuka kwa banja mwina mwamalamulo kapena maganizo. Mfundo imodzi yofunika kwambiri ya zochitikazi akuyifotokoza ndi kusatetezeka ndi mafunso wofunsiidwa pafupipafupi woti “Ndine ndani?” ndi “Ine ndine woyenera kukondedwa?”⁵

Mafunsowa akutitsogolera ku gwero lenireni la kugwidwa njakata kwa munthu - m’lingalira wa kufunika. Pali wina wosamala za ine? Ine ndiwoyera chiri yonse? Mafunsowa anakhazikika okha bwanji m’moyo wa munthu? Pofuna kuyankha funsoli tiyenera kubwerera ku chiyambi.

Mwadzidzi Eva anapezeka yekha mtengo woletsedwa. “Chifukwa chani Mulungu anatiretsa kudya ku mtengowu?” Anadabwa. Chipatso chinaoneka cholakalakika, chinamkodolera patsogolo. Mwadzidzi anamva mau kuchokera ku m’mtengomo. Satana, kuona mwai wake, anamyesa iye kuzera mu njoka; “Kodi Mulungu ananenadi, ‘Inu musadye kuchokera m’mitengo yonse ya m’mundamu?’”⁶ Satana akumnyengera kuti aziyankhulana ndiponso kuyika chikayiko mwa iye pa choonadi cha mau a Mulungu. Mukukambirana ndi mfundo zomveka, Eva anachepera kwa Satana. Kuwonjezera ku zida za chirendo za chinyengo ndi za mdima, ndikuti mpikisano ukhala ochepa woononga Eva akana woonetsa kufunitsitsa kwake potsegula pakamwa pake.

“Titha kudya chipatso cha m’mitengo m’munda, koma Mulungu anati, ‘Tisadya chipatso cha mtengo umene uli pakati pa munda, ndikuti tisaukhuze, kapena tizafa.’”⁷ Eva anavomereza vuto pobwereza mau amene Mulungu ananena, koma tsopano are m’vuto kwambiri. Chidwi chake, kuphatikizapo kutsegula vuto kwa Satana, zinamtsalira wosakonzeka ku maganizo ake amphamvu wotsatira, “Kufa simuzafadi.”⁸

Munapezekapo muzokambirana ndi wina mukucheza ndikuti inu mukumva kuti mukuyankhula bwino pamenepo kufikirira mnzanu wayankhula china chake mosiyana kwambiri? China chake simunayembekezere,

⁵ Jim Conway, *Adult Children of Legal or Emotional Divorce*, (Monarch Publications, 1990) p. 53

⁶ Genesis 3:1

⁷ Genesis 3:2, 3

⁸ Genesis 3:4

chokuzunguzani malingaliro ndikusiya kuganiza? Osati chimene ananena chinali chabwino kapena kuti chotsitsimutsa, koma kuti simunayembekezere kuchokera kwa iwo. Kuthekera kuyankhula kwao molimba mtima ndizoonekeratu kuti sizinakuchitikirenipo.

Satan, atawona kuti msampha wake wagwira anabweretsa chida chake chosakaza kuti apambane. “..... Pakuti Mulungu akudziwa kuti pamene mwadya maso anu adzatseguka ndipo mudzakhala ofanana ndi Mulungu, kudziwa zabwino ndi zoipa.”⁹

Mavesi wohepawa angakhale ngati akudusa ku katauni kakang’ono kaku midzi, kungophethira inu muwa sempha. Ganizo limene Satana anampatsa Eva linali ndi mbeu yomwe tsopano iri mliri kwa ana onse a Adamu - kulimbana kwa tanthauzo. Ganizo lomveka ngati lomasula koma lomwelo lopereka unyolo wa ukapolo wa munthu mu mavuto ndi mdima. Ikumveka ngati nkhanayi njaitali? Khalani ndi ine pamene tikumasulira ganizoli “*Inu simuzafadi,*” ndipo taonani pa chipatso chake ndi ntchito yake yopangisa mafunso wodandaula, “Kodi wina akusamala za ine?” ndikuti “Ndine woyenera kukondedwa?”

Ndikukumbukira ndiri ndi zaka zisanu ndi zitatu, mlongo wanga analandira chidole chimene chimatha kulira ndi kuseka komanso kumwa mkaka. Chimene umangochita ndikungoyikamo mabatire basi. Chimapereka maola ambiri achisangalalo kwa mlongo wanga. Ndimafuna kuchipereka kwa galu kuti achidye chifukwa pakapita kanthawi kulira kwake kunali kosatsangalatsa, koma ndinaganiza bwino chifukwa sindinafuno kumva mlongo wanga akulira kwa ola. Mwanayu amakhala ndi moyo pongoyikamo ma batire awiri basi, ichi ndi ndendende ganizo limene Satana amayesa kumubweretsa Eva. Eva, suyenera kudandaula za zomwe ali yense akunena, iwe uli ndi moyo mwa iwe wekha. Utha kupanga chokusangalatsa ndipo palibe vuto chifukwa uli ndi moyo mwa iwe wekha. Inu simuzafadi, ukamabweranso kuzadya za mtengowu kubwezeranso mphamvu m’abatirewo uzakhala bwino.

⁹ Genesis 3:5

Inu mungaganizire mwana wa miyeni khumi isanu ndi itatu akunena kwa makolo ake, “Ine ndikuganiza kuti nditha kukhala pa ndekha tsopano, ndimayakhula ndi wina wake m’ munda kumbuyo kwa nyumbaku ndipo akuti ndiri ndi mphamvu mkati mwanga yomwe ingandipatse moyo ndi zonse ndifuna, choncho zikomo chifukwa cha mathandizo anu, ndipo mwina tionana tsiku lina.” Izi ndi zenizeni zomwe zinachitikira Adamu ndi Eva m’ munda muja. Ganizoli *inu simuzafadi* linawononga malingaliro awo wodalira kotherathu pa Atate awo akumwamba. Ichi chinawononga maziko enieni a zomwe iwo anali monga anthu. Zinasokoneza malingaliro akudziwika kwawo ndiponso za mtengo / phindu lao ngati ana a Mulungu. Chifukwa chiyani Adamu ndi Eva akanangozindikira kulakwa kwao ndikubwerera ku udindo wodalira kwathunthu pa Atate awo akumwamba? Ndimafuna zikanakhala zophweka, koma zotsatira zomvomereza ganizo lakuti *inu simuzafadi* chifukwa muli ndi mphamvu mwa inu nokha, ngakhale kamphindi, zotsatira pomwepo zinalepheretsa iwo kuti abwerere ku mtendere woyamba wa chiyanjano ndi Mulungu. Tiyakhula zambiri za izi patsogolo, koma choyamba, tiyeni tibwerere ku mtengo watsoka uja.

Zindikirani langizo la Satana kuti pamene iwo adye chipatso, mwinamwake maso awo atsegukira ku chikhaliidwe chapamwamba. Kumasulira kwake pano n’ kwakuti sikukhala kokha ndi mphamvu mwa iwo okha, koma kuti chirengedwe chimakhala ndi zinthu za mphamvu, ndikuti mukangokhala nazo, zikhoza kukupangani inu kukhala ndi mphamvu kwambiri. Mwalandiredwa ku dziko la chuma.

Mu Genesis 3:4, 5, Satana ali mu ulaliki kuti apeze womutsatira ku ufumu wake watsopano. Iye anapereka ufumu umene ukulonjeza mphamvu ndi kukhutisidwa kwa onse amene angaulandire. Ufumuu ndiwokhazikika pakati pa mfundo ziwiri:

1. Nu muli ndi moyo mwa inu nokha kupanga inu kuzidalira kwenikweni kopanda kulumulidwa kapena wina kupindula pa inu.
2. Chirengedwe chatu chiri ndi anthu, zinthu, zoti mukakhala nazo kapena kugwirizana nazo, zingakupangeni amphamvu kwambiri, achidziwitso kwambiri ndi wokwanitsidwa kwambiri m’ moyo.

Kudzera m'mtengou wa chidziwitso, Satana amapereka kukhalako ndi mphamvu za ma batire, moyo wopanda kufuna wina wa kunja opeza phindu kapena kulamulidwa, choncho mutu wa ndimeyi - **Mtengo wa batire lolimba**. Satana akutiya kuti batire m'matupi lizakhala la mphamvu pamene titalira nzeru yake pa moyo.

Nchofunikira kukumbukira kuti pamene Adamu ndi Eva anadya chipatso cha mtengo, panalibe chakupha chachibadwidwe mwa ichi chimene chikanapanga iwo kukhala ndi mantha, ochimwa ndi opanduka. Baibulo limatiya kuti chipatso chinali chabwino kudya.¹⁰ Chakupha chinai mau amene Satana ananena kwa Eva. Chakupha ndi mfundo za ufumu wake. Anthu ena amafunsa, "Nchifukwa chani ndivutika pamene Adamu ndi Eva ndi amene anadya chipatso? Sindinadye kuchokera ku mtengo uja." Choono nchakuti nthawi zonse tichita pa tokha popanda Mulungu, timadya za mtengo uja mofanana m'mene Adamu ndi Eva anachitira chifukwa tinameza chakupha cha ufumu wa Satana. Zoono nzoti, tiphunzira kuti timadya kuchokera ku mtengou tsiku liri lonse ndipo zotsatira timavutika ndi zoopsa.

Lingaliro loti tingakhale ndi moyo popanda Mulungu sikunganeke kwachilendo kwa anthu ambiri, koma m'gawo likubwerali tiphunzira kuti kuganizaku nkwa kuzipha.

¹⁰ Genesis 3:6

2. Kasupe Wa Moyo

Linali tsiku lalitali ku ntchito. Tinali kumagawo akumapeto okonza dongosolo la ndalama - makamaka pafupifupi madongosolo makumi asanu ndi anayi kukhala limodzi. Inali ndondomeko yofuna kusamala, kukonza mwaluso kuti zokhumba ndi chiyembekezo cha mabwana kuti aliyense apezegawo lalikulu ku ndalama kuti zolinga zao zikwaniritsidwe. Malingaliro anga anayetsetsa pachabe kuwerengera zowerengera zonse m'mutu mwanga pamene mwadzidzidzi lamyalinalira. "Hello... Ndine Bambo wako, mwana wanga." Bambo anamveka ngati Nyumba yachi Fumu inali pa mapewapawo. "Chachitika nchani Bambo?" "Mayi ako achita ngozi ya galimoto." Mauwa anandimenya ngati nyundo yopunthira. Nthawi yomweyo ndinayamba kunjenjemera ndipo mtima wanga unagunda mowilikiza mkanthawi kochepe. Minofu yanga inalimba pamene thupi langa linalandira makhwala achirengedwe mthupi olimbitsa thupi. "Ngozi?" Pafupifupi ndinanong'ona pa lamyapoyesa kuti ndikhazikike. "Yayikulu bwanji?" "Ndiyaikulu kwambiri mwana wanga."

Pa nthawiyi ndinafunakuti ndilumphe kuzera pa lamyandi kukamira kwa bambo anga, koma analimaola khumi ndi awiri kuyenda pa galimoto ndipo ndinayenera kudikira mpaka m'mawa kuti ndikwere ndege. Pamene ndinasiyalyama, malingaliro anga amazungulira - chisoni, mantha ndi dzanzi zonse zinandimenyanthawiyimodzi. Nthawi yomweyo ndinakumbikira Yesu ndipo ndina gwada pa maondo anga ndi kulira mofula "Oo Yesu - chonde musalole kuti amwalire." Ndinatsegula Baibulo langa ndipo ndinapemphera ndikupemphera mpaka malingaliro abata unabwera

pa ine ndipo ndinamva pafupifupi mtendere. Maganizo anga anayendayenda ku zochitika wamba za moyo kufikira ndinamenyedwanso ndi; mantha, kupanda thandizo, ndi chisoni. Mobwereza bwereza ndinagwada pa maondo anga ndikupemphera ndikukangamira pa Yesu.

Mai anga ameyendetsa galimoto pa ulendo wao okaphunzitsa nyimbo. Anali pa msewu waukulu umene unali ndi njira ziwiri ndi munda wa mlingo khumi pakati pa misewu iwiri. Amadutsa galimoto yina pamene amadutsa phiri ndizimene amakumbukira. Galimoto yina imachokera mbali ina ndikutsokonekera kudutsa munda uja wa pakati pa misewu iwiri ndikugunda gamiloto ya amai anga mutu ndi mutu. Mphamvu ya kugundanaku inakankha injini ya galimoto ya mai anga kupyola choteteza moto, nthawi yomweyo kuponya chowongolera ku maso awo. Pa chifukwa chosadziwika, pa mphindi yomweyo mpando unaduka, ndikuthokoza unatero popanda kutero akanafera pompo. Pamene anafika nawo ku chipatala, anali ndi mikono yothyoka pamodzi ndi miyendo ndiponso mbali yonse yaku manzere ya nkhope inali yophwanyika.

Pamene amai anga amafika nawo m'chipatala, panali dokotala wina akuweruka atangomaliza ntchito tsikulo. Atangoona mai anga, anayambanso kugwira ntchito. Anagwiranso ntchito maola asanu ndi atatu kupulumutsa moyo wa mai anga, kenako atayetsetsa kwambiri anatsitsimuka. Sinditha kupeza mau wothokoza dokotalayo; mpaka tsopano zimabweretsa misonzi. Iye anagwira ntchito maola khumi asanu ndi limodzi molumikiza osapuma naganizanso kuwayimbira bambo anga lanya 3 koloko m'mamawa kuwadziwitsa kuti mai anga ali m'ululu woopsa koma atsitsimuka. Ndiri woyamikabe, chisanzo chowala cha luso, mphamvu ndi chifundo cha anthu a chipatala.

Patapita masiku wochepe ine ndi mkazi wanga tinali mu chipinda cha chisamaliro chapadera m'chipatala ndi mai anga. Ndinali wokondwa kwambiri kuona iwo ali moyo. Madokotolo anali wodabwa kuona m'mene amachirira. Tinauzidwa kuti sadzayimbanso piyano komanso kuyenda. Chinali chokhumudwitsa kwambiri, komabe analibe ndi ife, ndipo ndinali wothokoza. Lorelle mkazi wanga amayang'ana zimene a chipatala amaleMBERERA za amai anga ndipo zinampasa chidwi kuti ndione. Zinaonetsa poyera m'maganizo awo kuti titaya amai anga, ndipo mwadzidzidzi ziwalo

zawo zinagwirizana ndipo anatsitsimuka. Panalibe mbiri yotsonyeza m'mene zinachitikira, koma ndinadziwa kuti Atate anga, gwero la moyo, anatuma Mwana Wao kuwatsitsimutsa. Ndikuthokoza chifukwa cha mphamvu ya Yesu yopereka moyo. Lero, Amai anga akuyenda ndikuti nthawi zina pamene akuyimba piyano, ndimamva malingaliro akuya achiyamiko kwa Yesu chifukwa mai anga anali pa imfa yoonekeratu.

Ziri zonse tingamvetsetsa za gwero la moyo, Baibulo silikutisiya wokayika. Tikuwerenga zotsatira za Yesu mu Akolose:

Pakuti mwa Iye, zinalengedwa zonse za m'mwamba, ndi za padziko, zooneka ndi zosaonekazo, kapena mipando yacifumu, kapena maufumu, kapena maukulu, kapena maulamuliro; zinthu zonse zinalendedwa mwa iye ndi kwa iye. Ndipo iye ali woyamba wa zonse, **ndipo zonse zigwirizana pamodzi mwa Iye.** Akolose 1:16, 17

Chiri chonse tingaone kapena kuzindikira, ndiponso zinthu sitingazione, zinapangidwa ndikusamalidwa ndi Yesu Kristu.¹¹ Zindikirani mosamala mau omaliza a vesi 17. Ndipo **mwa Iye** zonse zigwirizana pamodzi. Malemba akutiiza momveka bwino kuti mphavu ya moyo yimene imachokera kwa Mwana wa Mulungu yongwira chirengedwe chonse pamodzi. Mtumwi Paulo akunena mwa njira ina m'buku la Machitidwe.

Mulungu amene analenga dziko lapansi ndi zonse ziri momwemo, Iyeyo, ndiye mwini kumwamba ndi dziko lapansi, sakhala m'nyumba zakacisi zomangidwa ndi manja; satumikidwa ndi manja a anthu, monga wosowa kanthu, popeza **iyeyo mwini apatsa zonse moyo ndi mpweya ndi zinthu zonse;** ndipo ndi mmodzi analenga mitundu yonse ya anthu, kuti akhaleponse pa khope ya dziko lapansi, **atapangiratu nyengo zao, ndi malekezero a pokhala pao;** kuti afunefune Mulungu, kapena akamfufuze ndi kumpeza, **ngakhale sakhala patari ndi yense wa ife;** pakuti mwa iye tikhala ndi moyo ndi kuyendayenda, ndi kupeza mkhalidwe wathu; monga enanso a

¹¹ “Koma ndine yani, ndi anthu anga ndiwo ayani, kuti tidzakhoza kupereka mwaifulu motere? Popeza zonse zifuma ku dzanja lanu.” 1 Mbiri 29:14

kuyimba anu ati, Pakuti ifenso tiri mbadwa zace. **Macitidwe**
17:24 - 28

Tikuona Mulungu amene amakhuzidwa kwambiri ndi miyoyo yathu. Paulo akuyamba ndi chinthunzi chachikulu kenako akufika pansu momwe tikhala ndi moyo ndi momwe tikhala.

1. Iye anakhazikitsa nthawi ndi malo mtundu uli wonse.
2. Iye sali kutali kwawina aliyense wa ife.
3. Kenako pomaliza Paulo akufotokoza nkhani yeniyeni kunena kuti mwa Iye ife tikhala ndi moyo ndikuyendayenda ndikukhalako.

Ngati mwa Iye tikhala ndi moyo ndiyeno mfundo yapafupi yomveka yotiuza ife ndiyoti popanda Iye sitingakhale ndi moyo. Monga oyimira Mulungu, Yesu, Mwana wa Mulungu, anati “... popanda ine palibe mungachite.”¹² Chonde zindikirani kuti izi zikutanthauza kuti ife palibe chinthu tingachite mwathupi, mwamaganizo kapena kuuzimu popanda Iye. Ife kwathunthu ndi kotheratu timadalira pa Mulungu ndi Mwana Wake pa chiri chonse, monga ngati mwana amadalira pa makolo ake.

Ndiroleni ndipereke fanizo pa mfundoyi chifukwa zochitika zake ndizakuya kwambiri. Ganizirani za chiwalo chodabwitsa cha mtima. Chimagwira ngati pompe kufalitsa magazi m’matupi athu onse, popanda kupuma, kwa zaka zaka. Chodabwitsa za mtima ndichoti kugunda kwa mtima zikuoneka kuti suthandizidwa ndi china chake kunjwa kwake. Mtima umafinyika ndi kumasuka kapena kuti kumagunda popanda kuthandizidwa ndi ubongo. Uli ndi dongosolo lozilamulira pa iwo wokha. Monga buku la kafukufuku likufotokoza: “Dongosolo loyenda ndilopangidwa ndi minofu yapaderadera yimapanga ndi kugawa magetsi amene amathandizira minofu ya mtima yigunde.”¹³ Minofuyi zoonadi ndi yapadera chifukwa yimapanga magetsi amene sachokera ku ubongo. Ndizodabwitsa zedi poti palibe mu bukumo pamene akufotokoza m’mene minofuyo imapangira magetsi kuti

¹² Yohane 15:5

¹³ Gerard Tortora and Nicholas Anagnostakos, *Principles of Anatomy and Physiology*, (Harper and Row Publishers, New York, 1984) p. 463.

mtima ugunde. Zikutchedwa kuti ndizapadera ndikuti ndi pa izo zokha, koma zimapanga bwanji, ndikuti mphamvuyi imachoka kuti?

Pano ndi pamene msewu ukugawika. Baibulo likutiiza ife kuti mphamvuyi imabwera mwachindunji kuchokera kwa Mulungu, “Mwa Iye tikhala ndi moyo.” Macitidwe 17:28. Koma Satana akutiiza ife kuti ndi wachibadwidwe mwa ife, ndi mbali imodzi yophweka ya ndondomeko ya moyo kuti timapeza mwa ife tokha, “Kufa simudzafadi.” Genesis 3:4. Ichi ndiye chikhazikitso. Ichi ndi china kapena chinzake. Pali Akristu ambiri amayesa kutenga msewu wapakati pa nkhanayi ndikunena “Inde, Mulungu analenga chirichonse, koma ziri ngati koloko yowayinda. Iye anayiyamba ndikuyisiya kuti yiziyenda.” Monga ngati Mulungu anapanga Batire lolimba ndikulikhazika mkati mwathu. Baibulo siriphunzinsa ganizoli. Ife tiri wolumikizana kwathunthu ndi Iye ndi kudalira kotherathu pa Iye kanthawi kali konse ka mphindi ka ola liri lonse la tsiku liri lonse. Mulungu mwachangu, modziwa, mwachikondi amatipatsa magetsi kusunga mitima yathu yizigunda. Pali china chake chenicheni chomwe chingatipange ife monga ngati anthu kwenikweni wovutika, koma tichinena patsogolopa. Choonadi ndi choti tiyenera kupeza poyera zenizeni za nkhanayi tsopano. Mwina ife tikhulupirere “Mwa Iye tikhala ndi moyo ndi kuyendayenda, ndi kupeza mkhalidwe wathu” kapena “Kufa sitizafadi.” Palibe malo apakatikati.

Monga zingakhale zovuta kwa ena ambiri a ife, tangochita ndi kukhalako kwa zakuthupi la umunthu. Tsopano tione mbali ya maganizo ndi uzimu. Taonani mavesi wotsatirawa:

Kuti itonthozeke mitima yao, nalumikizike pamodzi iwo m'cikondi, kufikira cuma conse ca cidzalo ca cidziwitso, kuti akazindikire iwo cinsinsi ca Mulungu, ndiye Kristu, **amene zolemera zonse za nzeru ndi cidziwitso zibisala mwa Iye.** Akolose 2:2, 3.

Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti; Taona ndaitana ndi kumchula dzina lace, Bezaleli, mwana wa Uri, mwana wa Huri, wa pfuko la Yuda; ndipo **ndamdadzadza ndi mzimu wa Mulungu, ndi luso, ndi nzeru, ndi cidziwitso, ndi m'ntchito ziri zonse,** kulingirira ntchito zaluso, kucita ndi golidi ndi siliva

ndi mkuwa, ndi kuzokota miyala yoikika, ndi kuzokota mtengo, kuchita ntchito ziri zonse. Eksodo 31:1 - 5

Baibulo likuulula Mulungu monga gwero la nzeru zonse ndi chidziwitso. Akolose 2:2, 3 akubetchera lingaliro kuti ife monga mwa umunthu tingayambitse nzeru ndi chidziwitso. Nzeru zonse ndi chidziwitsi chonse zimachokera kwa Mulungu kuzera mwa Kristu Mwana Wake. Chinsanzo chikuonetsedwa mu Eksodo 31:1-5. Pano tikuona Mulungu akupereka kwa munthu nzeru ndi kumvetsetsa mu ntchito za manja. Ndi zotsangalatsa kuti nthawi zambiri kunena kwa anthu amene awonetsa kuthekera kwambiri ndi luso monga “wopatsidwa mphatso.” Zoadi iwo ali, opatsidwa mphatso ndi Mulungu.

Tiyeni tizitengere tokha pakati pa zoimbaimba. Omvera akhala ndi chidwi pamene ntsikana wa luso akuthamangitsira dzala zake pamwamba ndi pansa pa piyano imene yaima mwachikoka pa nsanja. Iye akupanga piyano kuyimba kwenikweni - kukhuza kwa dzanja la mbuye. Kenako akufika pa chiindeinde, ndipo ife kulingalira kuti chimalidziro chafika. Timafuna kuti apitirire - koma nyimbo ikutha ndipo khamu liyamba kukuwa mwachitsangalalo, mantha ndi kukongola ndi chisomo kuphatikizika ndi chilakolako ndi mwamphamvu. Ntsikana anawerama ndi kupuma fungo lachiyamiko ndipo anachokapo pa nsanja.

Tiyeni tiwonjezere pang’ono, chifukwa pali chinthu china chotsangalatsa za choonekachi. Nthawi zonse china chake chikachitika chonchi omvera azifula kuti “Alemekezeke Mulungu kumene kwachokera madalitso” kapena china chake chofananirako. Chitsangalalo chizipita kwa Mulungu amene wapereka luso ndi nzeru ndi kuthekera. Mtima woyimba piyano uzitsefukira ndi chikondi ndi chiyamiko kwa Mulungu chifukwa cha mphatso Iye wampatsa kugwiritsa ntchito, koma zimenezi sizichitika chitika. Tikapanga choncho mooni, ife sitinga sekerere pamene tapambana kapena kukhumudwa pamene talephera chifukwa kuthekera kupanga chinthu sizichokera kwa ife, ndipo ngati sizichokera kwa ife, ndiyeno sitingatenge chiyamiko pamene tapambana kapena kumva kukhumudwa pamene talephera.

Pano pagona temberero la Mtengo wa batire lolimba. Taganizirani za ufulu wa parachuti cha moto m'mlengalenga.¹⁴ Malingaliro a ufulu tikhala nako tikapambana, kukhulupirira kuti ife ndife tayambitsa kupambana kumene kuyerekeza ndi kusangalala kwa kukwera mtundu wautali pamwamba pa dziko kuchitira umboni zooneka zodabwitsa kuchokera m'mwamba. Koma tikakwera kwambiri, kusowa kwa mphweya opuma ndikupangisa ife kusatsitsimuka kapena kuti palachuti yisowa moto ndikulephera kugwira ntchito ndikutigwetsa pansi. Tikakwera m'mwamba ndi bodza lakuti tiri ndi mphamvu mkati mwathu, pamwambanso kuthamanga kwa zotsatira pamenepo tikugwa pansi. Palibe kuthawa temberero la Mtengo wa batire lolimba. Ukangoti walawa chipatso chake chilakolako chija chokwera nchosaleretseka, ndipo zotsatira zomaliza nzosalephereka. Sikuti ndi mwa ngozi kuti "nkhwera yimatsogolera kupanga kulumala ku dziko lonse lapansi."¹⁵

Chipatso cha Mtengo wa batire lolimba chimapangitsa chilakolako chokwera m'mwamba mosayenera ife. Tikamadya kwambiri chipatsochi, kwambirinsu chilakolako chokwera ndipo pamwambanso ndithu tizagwa. Mwalandira kale kumenyedwa kungati? Mungaonjezerenso kulandira kungati? Izi nzofunikira kuziganizira.

Tiyeni tipite pa gawo lina. Taona zochitika za kudalira ku thupi ndi m'maganizo, nanga bwanji kudalira kwa uzimu ndi khalidwe. Iyi ndi nkhani yovutirapo, choncho mangani malamba, kukhoza kukhala kuyenda kovuta.

Baibulo limanena kuti **"Mulungu ndi chikondi."** 1 Yohane 4:8. Izi zikutiuza kuti Mulungu ndi gwero la chikondi. Limanenanso kuti Mulungu monga Mulungu wa chiyembekezo. Aroma 15:13. Ganizoli linatambasulidwa kwambiri mu Agalatiya:

¹⁴ Palachuti yondetsedwa ndi injini imene oyendetsa amaibereka kumbuyo. Nthawi zambiri amakonda kugwiritsa ntchito pa masewero koma monga mayendedwe chifukwa chimayenda mtundu ndithu wautali m'mlengalenga monga ngati ndege. Oyendetsa amakhala munthu m'modzi nthawi zambiri. Zambiri onani. Wikipedia: Powered Paragliding yotchenso Paramotor.

¹⁵ http://www.who.int/mental_health/management/depression/en/

Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiro, cifatso, ciletso; pokana zimenezi palibe lamulo. Agalatiya 5:22, 23

Mauwa ndi wokhuza kwambiri. Tiyeni tiwasanthule mwaka mphindi. Zikhumbo zonsezi zikuchokera pokhala ndi Mzimu wa Mulungu. Zikungothanthauza kuti popanda Mzimu wa Mulungu sungakhale chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo ndi zina. Ndimaganizira za choonadichi m’Baibulo tsiku lina pamene ndimayenda malo a chisangalalo m’mphepete mwa nyanja. Kunali kwa bata ndi mtendere. Mwadzidzi ndinaona mai wina akukankha mwana wake ntsikana pa lende. Onse amaseka ndipo mwachionekere amasangalala limodzi. Chikondi chimene maiyu amakumana nacho kwa mwana wake chinauziridwa ndi Mulungu. Ganizo lokhala wokonda ndi wachifundo ndi chifatso kwa mwana wake sizinayambike m’mtima mwa mai, koma m’mtima wa Mulungu, ndipo chinapatsidwa kwa mai uja amene anasankha kuchiwonetsera, ndi kukhala chikondi cha mai. Malingaliri kwenikweni si chikondi cha mai konse, koma chikondi cha Mulungu choonetsedwa kudzera mwa mai. Chikondi chija chinakhala mbali ya mai chifukwa iye anayanka ku Mzimu wa Mulungu ndi kuchionetsera. Malingaliri woonadi, palibe chinthu ngati chikondi cha mai cha ana kapena chikondi cha pakati pa mwamuna ndi mkazi wake. Kodi chikumveka chopambana? Chabwino umu ndimene Baibulo likuphunzitsira.

Ndakhala ndikupereka mfundoyi nthawi zambiri pamene ndimalalikira kapena kuyankhula pa misokhano ndipo ndizotsangalatsa kuona m’mene omvera amalabadira. Nkhope za anthu ena zimaonetsa monga ngati ndakhuza maziko enieni a mtundu wa anthu. Mwa mazana mazana a nyimbo za chikondi zimene zakhala zikuyimbidwa zikwi zikwi za malonjezano akunenedwa pa maukwati kuti “Ine ndimakukonda ndipo ndiza kukonda iwe mpaka muyaya,” palibe limodzi mwa malonjezano limene lingasungidwe popanda Mulungu kutsanulira chikondi chake mkati mwa miyoyo ya wina wa aliyense wa ife. Tirole chochitika cha chikondi m’palachuti kufotokoza kuti tirole chikondi m’mitima mwathu. Chifukwa chani ambiri amaperewera ku chikondi ndi kugwa pansi? Anthu amene amakhulupirira kuti chikondi chimayambika mwa miyoyo yathu patokha nthawi zambiri angadzuke m’mawa ndi kumva kusakonda okonedwa wao.

Amayamba kukayika ngati ubalewu ndiwoona kwa iwo tsopano ndipo nthawi zambiri amayamba kufuna wina wake kuti abwezeretsetso kumverereku. Chiphatso cha ngongole ya Mtengo wa batire lolimba chafika pa mapeto ndipo tsopano ndi nthawi ybweza ngongole.

Nanga bwanji kwa mwamuna woona amene amatanthauzadi zenizeni za malumbiro a chikondi mpaka myaya ndipo kenako mwadzidzidzi wapeza mkazi wina amene wakopeka naye. Iye mwina sanafune kumva m'njirayi koma iye "sangachitire mwina." Chikondi chatsokonekera ndi kutsirira, ndipo pali chikayiko cha umphumphu wake. Iye kenako ayamba kubwerera m'mbuyo kwa okonedwa wake chifukwa cha malingaliro okulakwa kumene anapanga komwe kukumlepheretsa iye kukhulupirira kuti iye anga kondedwebe. Iye amaganiza kuti angasamalire kuyenda kwa chikondi kuchokera m'mtima mwake, koma parachuti chake chalephera kuuluka ndipo chikugwa pansu kuchokera kumere anachiulutsa, ndipo ukwati wake watha. Kodi ndi nzodabwitsa kupeza chimwemwe mu ukwati chikulemphereka kwa anthu ambiri?

Chifukwa cha iwo amene akumva kuti ukwati wao sulinso woyenera tsopano, kumbukirani kuti chikondi chimayambira kokha m'mtima wa Mulungu ndipo mwa ufulu chimapezeka kwa iwo akuchipempha kwa Iye. Ngati inu mukumva kuti mwataya chikondi chija cha okonedwa wanu, pemphani Mulungu kuti akubwezeretseni. Iye azalola, chifukwa walonjeza.

Ndipo cimene ciri conse mukafunse m'dzina langa, ndidzacicita, kuti Atate alemekzedwe mwa Mwana. Ngati mudzapempha kanthu m'dzina langa, ndidzacicita. Yohane 14:13, 14

3. Pafupi ndi Mtima wa Mulungu

Timathamanga kwambiri ndi galimoto potsetsereka pa msewu waukulu. Matenda a uchembere anayamba a Lorelle mkazi wanga. Sitinafune kuti zitisokonekere, ndiye tinathamangira ku chipatala. Kanali koyamba ndipo wosangalala, posachedwa tikhala ndi mwana wathu woyamba. Tinakwera ku chipinda chochirira mosabvuta ndipo namwino anationa kamodzi nati, “Mukuoneka okondwa kwambiri, muyenera kupita kukayenda.” Chabwino, izi zinachepetsa chisangalalo chathu. Patapita mphindi makumi anayi ndi asanu tinabweranso ndipo tsopano Lorelle samamwetuliranso. Mphindi zina makumi atatu tinafika pakati pa ululu wa matenda a ubereki. Inde, palibe mau ena kufotokoza ichi, ululu, ululu waukulu. Tinayesa kukumbukira njira zonse za maphunziro a kalasi la okonzekera kubereka koma zinali zovuta kukhazikika. Ululu wa misempha unali wothamanga kwambiri motsatanatsatana. Potsiriza patapita maola khumi ndi limodzi, tinalandira mwana wathu woyamba wamwamuna, Mikayeli.

Pali chithunzi chosangalatsa kwambiri cha Lorelle ndi ine atangobereka kumene. Ichi nchodabwitsa mwamtheradi. Iye anakhala apo wooneka mokondwera ndi wowala monga ngati inali ntchito ya tsiku limodzi, ndipo ine ndimango gwedezeka kupita patsogolo ndi pambuyo muka mphepo kooneka ngati ine ndinali pafupi kugwa. Ndinakhala ndi ulemu kwambiri watsopano kwa achembere tsiku lija. Ndiyenera kukuuzani azimai kuti kuona mkazi wako akubereka ndi ntchito yovuta kwambiri.

Mukamamaliza kuseka, ndikhala nditamaliza mfundo yanga. Maganizo wovuta kuona amene umamkonda ali mu ululu ndi zosaneneka. Kwa ife

azibambo, nthawi zambiri timakhala ndi zothetsera mavuto, koma sindinakhale ndi mayankho pa nthawiyi ndipo zinandipweteka. Ndinango pemphera, “Mulungu, ndikudziwa kuti pali chifukwa pa ululu oneswu, koma tsopano sindikutha kuwona.” Zedi ndinali wokondwa kwambiri pamene izi zinatha.

Pamene ndinamugwira mwana kwa nthawi yoyamba, inali nthawi yam’yaya. Ndinamuyang’ana m’maso mwake, ndipo anandiyang’ananso, ndipo zinali zodabwitsa. Pamene ndinapitiriza kumuyang’ana mu maso mozizwa ndi modabwa, ndinagwidwa ndi malingaliro akuya a mantha. Ndinadziwa kuti mwana wanga ali ndi makhalidwe wofanana ndi makhalidwe anga, makhalidwe ovutitsa kwa olamulira, makhalidwe aja okokedwera kukupanduka, kulekana koposa kumvera. Pambuyo pa zonsezi, ndinadabwa, kodi azakhala m’nzanga? Kodi wina azabwera pakati pathu ndikutirekanitsa? Ndinangopemphera nthawi yomweyo, “Oo, wokonedwa Atate akumwamba, musalole chiri chonse kubwera pakati pa mwana wanga ndi ine. Tikhale pafupi limodzi nthawi zone, ndipo ndikupemphera kuti azandidziwe kuti ndine ndani ndikukhala m’nzanga.” Mwamphamvu pempherolo limakhalabe ndi ine. Nthawi zambiri ndimalimva, ndipo ndimapempherabe kukhulupirira kuti Mulungu azakwaniritsa kuti zizakhala zenizeni.

Patapita zaka zinayi ndinali ndi nthawi ya chete tsiku la Sabata kuyenda ndi kuyankhula ndi Ambuye, kutali ndi zogonthetsa ndi chipikitipikiti cha moyo. Ndimaganizira za Atate anga aku Mwamba ndi chikondi Chawo kwa ine ndi m’mene chiriri cha mtengo wapatali. Mwadzidzidzi, malingaliro anga anabwerera ku kubadwa kwa mwana wanga ndipo ndinakhalanso ndi chirakolako chachikulu chosasiyana ndi iye ndi kuti moona azandidziwadi ine. Malingalirowa atadutsa ndipo mwa bata ndinamva mau akayaziyazi mukati mwa malingaliro anga, anati, “Ndim’mene ndimamvera za iwe.” Sindinadziwe choti ndichite kuseka kapena kulira, ndinapeza zovuta kwambiri kuzilandira. “Koma Ambuye,” ndinati, “Mumandidziwa m’mene ine ndiriri, mumadziwa zimene ndachita ndi kunena zinthu zambiri zolakwa,” ndinapitiriza kumenyana. Ndinadabwitsika kwambiri ndi ine ndekha. Ndine munthu amene ndinamulandira Kristu ngati Mpulumutsi wake ndikukhulupirira kuti machimo anga anakhululukidwa, koma pamene Mulungu wabwera pafupi chonchi ndi ine ndikundiiza m’mene Iye

amamvera za ine, ndinavutika kuzilandira. Kenako ndinangolira kwambiri “Oo Zikomo, zikomo chifukwa mumandikonda ndikuti zikomo chifukwa cha zonse zimene m’mandichitira ine. Ndimakukondani Inu kwambiri.” Ndinazindikira kuti Atate anga Kumwamba amandikonda kwambiri ndikuti Iwo safuna china chiri chonse chibwere pakati pathu. Zimamupweteka Iye kuganizira kuti tingasiyane ife, ndipo Iye amapanga chiri chonse kuti tisasiyane.

Mchochitikachi cha mwai wodabwitsa wokhala mbali ya ufumu wa Mulungu zinaululidwa kwa ine pa mtima wanga. Zitangochitika izi ndinatsogozedwa ku mau mu Baibulo amene ananditsegula maso ndikundipanga ine kulemekeza Mulungu koposa. Ndipemphero langa kuti lemba lofunikali litenthetsa m’mtima mwanu ndi kusakusiyani inu. Pano pali dzenera looneka bwino la ufumu wa Mulungu:

Kodi mpheta zisanu sizigulidwa timakobiri tiwiri? ndipo palibe imodzi ya izo iiwalika pamaso pa Mulungu; komatu ngakhale matsitsi onse a pamutu panu awerengedwa. Musaopa, muposa mtengo wace wa mpheta zambiri. Luka 12:6, 7

Yesu akufotokoza za mfundo za ufumu Wake. M’mavesiwa tiri ndi chilinganizo chimene chimapanga anthu kukhala ofunikira mu ufumu uja. Kodi ndi chiyani chimaapanga iwo kuwerengedwa, ndi chiyani chimaapanga iwo woyenera chinachake, ndi chiyani chimaapanga iwo amtengo wapatali? Ngati nkhaninyi ndi yosafunikira kwa inu, ndiyetu lembali siritanthauza chiri chonse, koma sindinapeze winawake amene salimbana ndi nkhani zoziyenereza yekha.

Yesu akunena za mtengo wa mpheta zisanu m’mawu a anthu. M’malingaliro a dziko lapansi mphetazi ziri ndi mtengo wotsika. Yesu kenako akuyerekeza ndikuti, “Palibe imodzi ya izo imayiwaliidwa ndi Mulungu.” Pano kusiyantsa ndikoti chifukwa Mulungu amakumbukira mpheta, ziri za mtengo wapatali mu ufumu wa Mulungu. Yesu akupitiriza mfundoyi poyerekeza momwe Mulungu amaganizira za ife potiyerekeza ndi mpheta, “matsitsi onse a pamutu panu awerengedwa.” Ngati izi siziri “zoonza mtima, pafupi ndi umunthu”, ndiyeno ndi chiyani? Kenako akubwera mau osangalatsa: “Musaopa; muposa mtengo wace wa mpheta zambiri.”

Mungaone momwe kuyenera ndi kufunikira kumapezekera mu ufumu wa Mulungu? Zingobwera pongodzindikira kuti Mulungu mwa chikondi amatiganizira mosalekeza. Ife motsimikizika tiri mu malingaliro Ake. Iye amatipatsa moyo, kupanga mitima yathu kugunda, mwachangu amatsanulira chikondi Chake m'miyoyo yathu kuti ife tizisangalala ndi moyo; ndipo amatipatsa zochuluka mphatso, maluso, ndi kuthekera kwa kukhutitsidwa, chisangalalo ndi kutumikira ena. Pano pali chinsinsi cha ufumu wa Mulungu, chinsinsi cha kufunikira. Ichi ndi mfungulo wotsegulira ufumu wa ukapolo wa uchabechabe ndi nkhawa. Kodi muli ndi mtima wokhulupirira ichi? Pamene tiri pa mfundoyi, kodi mumadziwa momwe Mulungu amaganizira za inu? Mvetserani ku ichi...

Inu, Yehova wanga, zodabwisa zanu mudazicita nzambiri,
Ndipo zolingirira zanu za pa ife; Palibe wina wozifotokozer
Inu; Ndikazisimba ndi kuzichula, Zindicurukira kuziwerenga.
Masalimo 40:5

Ngati mtengo wathu umatsimikizika ndi maganizo a chikondi chimene Mulungu ali nacho kwa ife, ndiyeno lembali likutiiza ife kuti ndife a mtengo, chifukwa zikunena ndondomeko Zake ndi malingaliro kwa ife ndi woposa kuti angalengezedwe kapena kuwerengedwa. Zikumveka bwanji kukhala wa mtengo? Koma zingakhale za bwino kokha mu chikhulupiriro chathu mu choonadi kuti Mulungu amatikonda kopitirira mlingo, kusawerengera momwe tiri abwino kapena oipa. Nkhaniyi ndiyodabwitsa ndipo ndiri wothokoza chikuwa cha ichi. Choncho nthawi zonse mukama yetsedwa kuti mukayikire kuyenera kwanu, mungoona pa mpheta ndi kukhulupirira!

4. Ufumu wa Banja

Ndi tsiku lofunda ndi la chinyezi. Mzimu wa chikondwerero ukufalikira m'chipinda. Fungo lokoma likuuluka kuchokera ku chipinda chophikira kulonjeza kuti kuli zakudya zakoma. Kuseka kukumveka kuchokera ku nkhani zakale zikunenedwa. Mphatso zikusinthanitsidwa m'chisangalalo chodabwitsa chophatikiza ndi chikondi. Ana akusangalala ndi Agogo a akazi pamene Agogo a amuna akutiiza m'mene takulira ndikutalika. Izi nthawi zonse zimachitika pamene tapita kukaona Agogo athu. Inali nthawi ya banja, nthawi yotsimikizira kumene umachokera, nthawi yolumikizanso ndi omwe umaakonda, kugawana mphatso; nthawi ya mtengo wapatali ndi yofunikira kukhala pamodzi.

Palibe chinthu chovuta kwambiri kuposa malingaliro a m'gwirizano m'banja wotiteteza ife ku zotirekanitsa monga nkhwana ndi uchabechabe. Banja angakhale malo amene ungalandiridwe momwe uliri, kukhala iwe popanda chokuyenereza, m'mene ungakhulukidwe pa zophophonya ndipo kungogawana chisangalalo cha moyo limodzi.

Yesu akutsegula chithunzi chofunikira kwambiri cha ufumu wa Mulungu pamene anatiphunzitsa ife m'mene tingapempherere. Yesu anati, "Umu, ndim'mene mungapempherere: 'Atate Athu muli kumwamba.....'" Yesu sananene kuti popemphera 'ziti, "Wokondedwa Mulungu," kapena "Wopatulika Wolemekezeka," kapena "Wokondedwa Mfumu," ngati mfundo yathu yoyambira, koma "Atate athu."

UFUMU WA MULUNGU NDI BANJA

Ichi chikuoneka choonekeratu kwaena, koma zochitika za ufumu wa banja zotsatira nzofunikira kwambiri. Tiona zochitikazi m’magawo akubwerawa. Nthawi yoyamba imene Atate anayakhula ku mtundu wa anthu mu **Mateyu 3:17**: **“Uyu ndiye Mwana wanga wokonedwa, mwa Iyeyu ndikondwera.”** Kuchokera pachiyambi cha nthawi kufikira ubatizo wa Yesu, Mulungu amayankhulana ndi ife kuzera mwa Mwana Wake. M’chidzalo chonse cha kutengera umulungu Wake, Yesu anali Yehova amene atsegula Nyanja Yofira, Iye anali Yehova amene anabangula pa Phiri la Sinayi ndipo Iye anali Yehova amene anatsogolera Yoswa mu Dziko la Lonjezano. **1 Akorinto 10:1 - 4 (Pakuti sindifuna, kuti mukhale osadziwa, abale, kuti makolo athu onse anali pansu pa mtambo, naoloka nyanja onse; 2 nabatizidwa onse kwa Mose, mumtambo, ndi m’nyanja, 3 nadya onse cakudya cauzimu cimodzimodzi; 4 namwa onse cakumwa cauzimu cimodzimodzi; pakuti anamwa mwa thanthwe lauzimu lakuwatsata; koma thanthwero ndiye Kristu).** Pa nthawi ya ubatizo wa Kristu, Mwana wa Mulungu anakhala **Emanueli - Mulungu nafe** - ngati m’modzi wa ife. Choncho tsopano **Atate** akuyankhula kwa nthawi yoyamba ndipo wau Ake ali ofunikira kwambiri (m’mene aliri nthawi zonse), chifukwa pompano Mulungu akuyala khalidwe lenireni la ufumu Wake. “Uyu ndiye Mwana wanga wokonedwa, mwa Iyeyu ndikondwera.” Pali njira zambiri zimene Mulungu akanamutchulira Mwana Wake, monga, “Uyu ndi Mlengi wa kumwamba ndi dziko lapansi; mumvereni Iye.” kapena “Uyu ndi Mfumu yanu, mumvereni Iye,” koma Mulungu akumutchula **kudziwika** kwa Mwana Wake mu njira ya banja kusiyana ndi mu njira ya mfumu kapena olamulira. Tikafufuza malembawa, tikuona zotsatirazi:

1. Uyu ndiye Mwana Wanga

= Kudziwika

2. Amene Ine ndimukonda; Mwa Iyeyu Ine ndikondwera

= **Mtengo**

Mu Ufumu wa Mulungu, kufunikira ndi kuyenera zimatsimikizika ndi ubale wathu kwa Iye. Izi ndi zosiyana kwambiri ndi mu ufumu wa Satana m’mene kufunikira ndi kuyenera zimatsimikizika ndi kuchita mopambana ndi

zomwe wapeza, kuweruzidwa ndi ife eni ndinso ena atizungulira. Mu Ufumu wa Mulungu, Iye ndi Atate wathu ndipo ife ndife ana Ake. Ichi ndiye kudziwika kwathu. Timadziwika ndi amene tiri kwa mwini wake osati zomwe ife tichita. Chifukwa choti Mulungu amatikonda ife monga ana ndikutsanulira madalitso pa ife mopitirira, amaganizira za ife nthawi zonse, ndipo amafuna kukhala pafupi ndi ife, zimatipasa ife malingaliro wa mtengo wosaneneka. “Musaope, chifukwa mulioyenera kuposa mpheta zambiri.”

Mu ufumu wa Mulungu kudziwika kwathu ndi mtengo nzokhalitsa monga Mulungu Mwini - wosatha ndi wosasintha. Kusawerengera kupambana kapena kulephera, ubale umakhalabe osasintha ndipo kuyenera kwathu ndi kotetezedwa. Mu ufumu wa Satana kuyenera kwathu kuli kotetezedwa monga ngati katundu pa msika zitachitika pa tsiku la Sepitembala 11, 2001 - osakhazikika kwambiri, osatetezeka ndipo nthawi yina iri yonse kupasuka. Tingatsimikizire kuti nthawi zonse tizipambana? Tingatsimikize kuti anthu wotizungulira, kwa omwe ife timafuna chirimbikitsa ndi chithandizo, nthawi zonse angamasangalale ndi khama lathu? Nkhomwe! Kwa iwo amene ali ndi makutu amve, kuti wanzeru anamanga nyumba yake pa thanthwe kusiyana ndi pa mchenga.

Kuti titeteze kudziwika kwathu ndi kupulumutsa ife kuchoka mu kulowa mu moyo osimidwa, kulefuka, uchabechabe ndi imfa, Mulungu wamanga linga mu mtima wa ufumu Wake lamulo lomwe lizateteza maubale. Amachita ndi mitundu iwiri ya maubale: Ubale pakati pa ife ndi Atate Athu akumwamba, ndi ubale pakati pa wina wa ife ngati abale ndi alongo mu ufumu wa Mulungu. Ndi chifukwa chake Yesu anati:

Ndipo Yesu anati kwa iye, Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi nzeru zako zonse, Ili ndilo lamulo lalikuru ndi loyamba. Ndipo laciwiri lolingana nalo ndili, Uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini. Pa malamulo awa awiri mpokolowekapo cilamulo conse ndi aneneri. Mateyu 22: 37-40

Malamulo awiri akuluwa anapangidwa kuti ateteze kudziwika kwathu ndi mtengo / phindu ngati ana a Mulungu. Malamulo awiriwa ndi, zoona, chidule cha Malamulo Khumi. Kodi munayamba mwaganizirapo za

Malamulo Khumi ngati chinthu chofunika kwambiri pokupewetsani inu kukutaya kwa kuyenera kwanu? Mukati mwa ufumu wa Mulungu Malamulo Khumi amamveka mu nkhani ya maubale. Ngati inu mungadule maubalewa, mukuwononga kudziwika kwanu, ndipo pamene mwawononga kudziwika kwanu, imfa yikufuna kukumbatirani inu. Palibe kusinthasintham' malemba a Mulungu kuti mphoto ya uchimo ndi imfa. Uchimo (chimene Baibulo limafotokoza monga kuswa lamulo mu 1 Yohane 3:4 - Yense wakuchita cimo acitanso kusayeruzika; ndipo cimo ndilo kusayeruzika) limawononga kudziwika kwathu ndi mtengo. Pamene kudziwika ndi mtengo zapita, moyo umafuna imfa. Ndendende ndi chifukwa chake nkhwana ndi kuzipha ziri mavuto aakulu pa anthu lero. Yankho ndi losavuta - uchimo. Kodi inu mungaone chifukwa Mulungu amadana ndi tchimo kwambiri? Tchimo ndi lolanda kudziwika kwathu ndi mtengo ngati ana a Mulungu, ndipo Mulungu ndiotsimikiza kuliwononga.

Mofulumira tipange mwachidule zimene taona:

1. Ufumu wa Mulungu ndi banja.
2. Mulungu ndi Atate Wathu ndipo ife ndi ana Ake.
3. Kudziwika kwathu ndi mtengo monga pa yekha zimakhazikika pa ubale wathu kwa Mulungu.
4. Ufumu wa Mulungu ndi ufumu wapa chibale wokhazikika pa maubale pakati pa ife ndi Mulungu ndi pakati pa wina ndi mnzake.
5. Maubalewa amatetetedwa ndi Malamulo Khumi.
6. Kuswa Malamulo ndi kuwononga kudziwika kwathu ndi mtengo wathu.

5. Vuto mu Banja

Ndikananena pongomuona pa nkhope yake kuti anavutika ndi zoopsa zinamchitikira. Maso ake anamupereka ngakhale amayetsetsa kukhala ngati ali bwino. Ine ndinamfunsa “Zonse ziri bwino?”

“Mkazi wanga ndi ine tasiyana,” iye anayankha mopwetekedwa. “Ine sindinayembekezere kuti zingachitike,” ananena, monong’oneza bondo. Tinakambirana za mavuto amene amakumana nawo kenako mofulumira “Ine ndikusamala kusaona ana - zikundipweteka ine.” Ndimamuona akuvutika kuzigwira pamodzi, ndipo ndithu ndinamva kupweteka kwake. Ndinafunitsitsa kuti ndimuthandidze. Ndemanga yake yomalirza inali “Sindikuona njira yoti ndiyende kapena kumene ndikupita.”

Okhawa amene anapatukanapo ndi kusudzulanapo angamvetsetse maganizo mu mauwa. Mantha, mkwiyo, ndi chisoni zimene amamva amene samafuna kupatukana ndi kusudzulidwa nthawi zambiri zimayerekezedwa ndi kuferedwa.¹⁶ Kuwononga kwenikweni kwa kusudzulidwa kutanthauza kuposa kungogawana katundu, zikutanthauza kukonzanso kudziwika kwako konse.¹⁷

¹⁶ Nelly Zola and Renata Singers, *The Stories from the Land of Divorce*, (Pan Mcmillan, Sydney, 1995) p 2;

¹⁷ Ibid

Wovutika kwambiri, kwenikweni, ndi ana. Maganizo wononga osiyanasina amene amadusa mwa an samachitika nthawi yokhayo yolekana makolo koma kufikira moyo wao onse, sungawerengere modzadza.

Jim Conway anafufuza mazana aachikulire amene anali ana a wosudzulidwa, maganizo osiyanasiyana amene iwo amamva anafotokozedwa motere:

Osasangalala - makumi asanu ndi awiri ndi mphambu ziwiri pa zana limodzi (72%)

Omva opanda mphamvu - makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zisanu pa zana limodzi (65%)

Omva kusungulumwa - makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu limodzi pa zana limodzi (61%)

Amantha - makumi asanu ndi mphambu ziwiri pa zana limodzi (52%)

Amkwiyo - makumi asanu pa zana limodzi (50%)

Omva kusiyidwa - makumi anayi ndi mphambi zisanu ndi zitatu pa zana limodzi (48%)

Omva kukanidwa - makumi anayi pa zana limodzi (40%)

Omva achabechabe - makumi atatu pa zana limodzi (30%)

Ana okhuzidwa ndi kusudzulidwa amasiya achikulire nkhani zotsatirazi:

Mowirikiza kufunafuna kumvomerezeka - makumi asanu nd mphambu zisanu ndi zitatu pa zana limodzi (58%)

Kutsekereza zina zakale lawo - makumi asanu ndi mphambu zinayi pa zana limodzi (54%)

Odziweruza okha mokhwima kwambiri - makumi asanu ndi mphambu zitatu pa zana limodzi (53%)

Kuzitenga okha mozama kwimbiri - makamu anayi nd mphambu zisanu ndi ziwiri pa zana limodzi (47%)

Kuchita mopitiriza pa zinthu zomwe iwo sangathe kuzilamulira - makumi anayi nd mphambu ziwiri pa zana limodzi (42%)

Okhalabe ndi mavuto ndi maubale - makumi anayi pa zana limodzi (40%)¹⁸

Kodi nzodabwitsa kuti Mulungu akunena, “Ndidana nako kuleka!” Malaki 2:16. Mosasamala kuti zikuchitka bwanji, kapena ndani akuleka mnzake, kutaya ubale wa banja chiri chowononga mbali zonse. Palibe opindula pamene ubale wa banja wasweka. Komabe ndim’mene zinachitikira ku mwamba. Banja la Mulungu linang’ambika pakati ndi vuto pamene mwana Wake wolengedwa woyamba anaukira Iye.

Baibulo likuti mu Cibvumbulutso 12:7, “Ndipo munali nkhoodom’mwamba.” Pamene ife tikuwerenga vesiri tingayetsedwe kuganiza kuti nkhoodoyi ndi pakati pa mafumu awiri ndi maufumu ao, koma nkhoodoyi ndikung’ambika kwa banja la Mulungu. Kodi mungaganizire inu pamene Mulungu poyamba anapanga Lusifala anamgwira mwachikondi mwana wake watsopano? Mulungu anagawana mtima wake weni weni ndi moyo ndi m’ngeloyu. Sanamuonetsera kanthu koma chikondi ndi kumpasa iye mwai wotumikira pa udindo waukulu kwambiri mu boma la Banja Lake. Koma tsopano mwanayu wa Iye ali akulavula mau a mkwiyo ndi kupanduka. Kuyenda mu mithunzi ya chinyengo ndi mabodza, iye anasokoneza malingaliro a ana ena ambiri a Mulungu. Mungaganizire inu za chisoni? Lusifala, analengedwa mwangwiro, tsopano wadzadzidwa ndi udanani ndi kupha. Iye anatsimikizika kuwononga Mwana wam’yaya wa Mulungu, chifukwa Yesu anaulula kuti Satana anali wakupha kuyambira pa chiyambi mu Yohane 8:44 – “... Iyeyu anali wambapanda kuyambira paciyambi...” Zenizeni za izi zinaonekera pa Mtanda wa Kalivali; pamene Satana anayembekezera kuthana ndi Yesu.

Angamvetsetse ndani kutaya kumene Mulungu anamva za mwana Wake Lusifala. Tiri ndi kubwereza kuchokera ku mtima wa Mulungu mu nkhani ya Davide ndi Abisolomu.

Ndipo mfumuyo inagwidwa cisoni, nikwera ku cipinda cosanja pa cipataco, nilira misozi; niyenda, nitero, Mwana wanga

¹⁸ Conway, p 31

Abisalomu; mwana wanga! Mwenzi nditakufera ine,
Abisalomu, mwana wanga, mwana wanga! 2 Samueli 18:33

Abisalomu, mwana wamwamuna wokongola ndi wooneka bwino wa Davide, anafuna kupha atate ake ndi kutenga ufumu wake, koma atsirikali a Davide anagonjetsa mphamvu za mwana wake ndipo Abisalomu anaphedwa mu nkhondo. M'malo mosangalala pa kupambanako Davide analira chifukwa chotaya mwana wake opanduka. Palibe wopindula pamene mabanja agawika pakati.

Nkofunikira kukumbukira kuti mu ufumu wa Mulungu kudziwika ndi mtengo wa munthu za mangiriridwa pa ubale wao kwa Mulungu Mulengi, Atate athu akumwamba. Pamene Lusifala anatuluka mu ubale uja, iye anazipha m'maganizo ndi m'malingaliro ndi kutsegula mazenera wosayembekezereka amalingaliro a mdima. Lusifala asanapanduke, mukadamufunsa iye – “Iwe ndiwe ndani?” akadayankha modekha ndi chitsimikizo ndi chidaliro, “Ine ndine mwana wa Mulungu, ndipo Iye amandikonda ine.” Lusifala atangokana Atate ake, ngati mukanamufunsa iye funso lomwero, “Iwe ndiwe ndani Lusifala?” iye akanati chani? Iye sanalinso ndi kudziwika, anakuwononga. Kulikonse kudziwika kumene iye angafune kupanga kwa iye yekha kuyambira nthawi ija mpaka mtsogolo, sangateronso, sangadzadzisenso kuperewera ndi malingaliro wotayika amene iye anamchitikira kuchokera ku kusweka kwa ubale weniweni ndi Atate ake akumwamba. Nthawi zambiri ankafuna ngati abwezeretsenso chomwe iye anachitaya, koma kunyada kwake sikunamulole iye kutero. Kuonjezera apo, mukati mwenimweni mwa iye akana khulupirira kuti iye angakhululukidwe pambuyo posayamika kwake mopanda manyazi ndi kupanduka poyera. Lusifala, tsopano Satana, kuthanthauzakuti ‘wotsutsa’, wayima payekha. Palibe wina womugwira iye, popanda kholo lotembenukirako, ndi popanda malo wotchedwa kwawo. Satana tsopano akuoneka ndi mtima wonse wachabechabe: osatetezeka, mantha, wopanda kanthu, nsanje, kunyada, kudzilungamitsa, kudzitukumula, chiwawa, mkwiyo, ndi mzimu wolamulira.

Satana sadziwe njira yoti ayende tsopano. Iye anayenera kudzifotokozanso kuti iye ndani ndi mwinamwake kuphimba kupanda kanthu kuja, uchabechabe uja, kusakhalakonso kuja kumene iye amazimva mkati. Monga

mwana wina aliyense amene amazimva wosayenera, Satana amanyamula zizindikiro zonse za kusatetezeka, mantha, misala ndi wofuna kwambiri kuvomerezeka kuchokera kwa winawake ali yense angamupeze. Iye amalakalaka chidwi, ndikuti akwanitse kusayenera kuja, khalidwe lake lopotoka lakulakalaka kuti azipembezidwa, kulemekezedwa ndi kukonedwa - china chiri chonse chochosa kupweteka, kusungulumwa ndi uchabechabe - chiri chonse. Mkhaliidwe wachisoniu modabwitsa ukuonekera mu nyimbo kuchokera m'sewero lotchedwa Mzinda wa Angelo:

Vesi 1

Tayani nthawi yanu yonse kudikira mwai wina uja
Chifukwa kupuma kuja kungapange bwino
Kuli nthawi zonse chifukwa china chosamvera bwino mokwanira
Ndipo nchovuta pakutha kwa tsiku
Ine ndikufuna zododometsa zina kapena chotuluka chokongola
Kukumbukira kukuchokera m'mitsempha mwanga
Ndiloleni ine ndikhale opanda, O ndi kusalemera ndi mwina
Ine ndipeza mtendere wina usiku uno

Vesi 2

Ndatopa ndi muzere woongoka, ndikuli konse utembenukira
Kuli miimba ndi akuba pa mbuyo pako
Mkuntho ukupotozokabe, iwe ukumangabe pa mabodza
Zimene iwe ukupanga chifukwa cha zonse zomwe ukusowa
Sichikusintha chiri chonse, kuthawa nthawi yomalidza
Nkophweka kukhulupirira m'misala yokomayi
O kukhumudwaku kwaulemerero kumene kumandibweretsa pamaondo
anga.

Popeza Satana anakana ubale ngati maziko a kuyenera, iye sakanakhazikitsa ufumu wake pa ubale. Panali njira imodzi yotsalira kwa iye. Adziwike ndi zimene akupanga m'malo mwa kwamwini wake akuchoka. Ufumuu siungagwire ngati aliyense angavomereze kuti moyo wonse, nzeru, ndi chikondi chimachokera kwa Atate. Choncho Satana anapanga mfundo yoti

‘mphamvu nzochokera mkati,’ ndikuti amuchepse Mulungu ku mphamvu basi yimene singakhale ndi ubale payekha. Mphamvu yimene ungayigwiritse ntchito ndi kusaigwiritsa molakwika m’mene ufunira. Ufumu wa Satana ndi ufumu wa mphamvu ndi kuchitachita ndi kufuna chitsangalalo. Phata lake ndikuti sayankha kwa wina ali yense, ndi kusamalira okhawo amene azakhala ofunika kwa inu.

Ufumu wathedwa, zoonza, chifukwa mphamvu ya moyo woyisamalira yikuchokera kwa oilengena ndipo tsiku lina chikumbu mtima cha kukana Iye chizawononga moyo wa onse mwaliuma akana kumvomereza kudziwika kwao ngati ana a Mulungu. Wathedwa chifukwa palibe china chingachotse kupweteka ndi kutaya chomwe chabwera kuchokera ku kukana kudziwika kuja. Pano tikuphunzira choona cha mwambi woti, “Kulibe mpumulo kwa ochimwa.”

Ngati tingabwerere ku Munda wa Edeni mu nkhanayi, ife tiona kuti kunjira Satana akuoneka wochenjera waluso ndi wochenjera pamene iye akufuna kulepheretsa kuthamangitsidwa kuchokera kumwamba. Komabe mkati muli mtima wodzadza ndi uchabechabe ndi kusatetezeka kumene kukulimbana kuti kupange kudziwika kwina kwatsopano ndikuti athawe phompho lomwe likukula lopanda chiyembekezo.

6. Gehena pa Dziko

Ichi chiyenera kukhala chimodzi cha zochitika zowawitsa mu moyo. Mwina zinatenga zaka, koma patapita nthawi inu mwakhala ndi ubwenzi wolimba kwenikweni ndi winawake. Wina wake amene inu mwayamba kumkondwa kwenikweni kutaya naye nthawi. Mwadzidzi inu mwadzindikira kuti bwenzi lanu likuchita zinthu mwachirendo. Mukuyesa kusalabadira ndi kuziiza nokha kuti mukungoganizira zinthu ndipo kuti palibe nkhani yeniyeni. Koma maumboni akunka nachuluka pamene nthawi ikupita, ndipo pomaliza mukumilizidwa kuti m'mfunse m'nzanu chimene chikuchitika. Mutataya nthawi yomwe ikuoneka ngati chaka kuti mudutse zoonekeratu ngati khoma la mwala, mukupeza kuti wina wake amamukopa m'nzanu uja kutsutsana ndi inu, chimene chimapangitsa kutanthauzira zochitika zanu mwa njira imene yakusiyani inu wodabwa.

Ndithudi kulingalira kuzapambana ndipo mwamsanga mungathetse kusamvetsetsanaku, koma si choncho! Pamene inu mukufuna kupereka malongosoledwe wololera inu kenako mopanda manyazi mukudzudzulidwa kuti mukuyesa kupeza chozitchinjirizira. Pa nthawiyi amodzi mwa maganizo akhoza kukufikirani: kupweteka, ululu, mkwiyo kapenanso ngakhale kuwonongedwa kuti m'nzanu angakhulupirire motsavuta winawake popanda kunena liwu kwa inu, ngakhale kuti akukhalireni kumbuyo! Kukhala chete kwanu kukupereka chizindikiro kwa mnzanu kuti amanena zoono ndipo zonse zimene amanena za inu zinali zoono. Kuyankhulanso ndikungowonjezera chipongwe kuululu!

Mwina pamene mwawerenga ndime ziwirizi, chikumbumtima chopweteka chakubwererani chotsimikizira za zenizeni za zochitikazi mobwerezabwereza chiyambire nthawi pa dziko la pansi pano. Ngakhale pamene ndikulembamu ndikukumbukira zomwe zinandichitikira ine, ndikuyima ndikufunsanso, “Chifukwa chani?”

Ndikunena zoonza ambiri a ife tiri ndi zipsera kuchokera kukukanidwa kotere, ndipo ndikulingalira izi mwa njira yina pang’ono zingatithandize kumvetsa momwe Mulungu anamvera pamene Adamu ndi Eva anadya chipatso chochokera ku Mtengo wa Chidziwitso. Ndi chimodzi cha zinsinsi zazikulu kwambiri za moyo kuti mau a wachilendo angalekanitse abwenzi enieni.

Ndakhala ndikuganzira Mulungu akuyang’anitsitsa mwana wake wamkazi Eva pamene iye anapezeka yekha pakati pa munda, kenako mwadzidzi wayamba kukambirana ndi “wachirendo.” Pa nthawi yonse imene Mulungu anali nayo mwapadera ndi Eva, kumuwonetsa iye chikondi Chake chochuluka, iye akanamamatira ku chitetezero ndi chikondi cha Atate ake akumwamba kapena kulandira mau a Satana kupyolera mwa njoka? Nchifukwa chiyani Mulungu sanalowerere ndikutumiza m’ngelo ndikuletsa chodula ubale wao? Ndikulingalira kuti pali mafunso ambiri woti ayankhindwe pa nthawi. Pamene sitiri ndi nthawi kapena malo ambiri woti tiyankhe onsewa, ndipo nzoona ena sangayankhidwe mokwanira kufikira titazonana ndi Iye maso ndi maso, koma yankho lapakatikati ndi chikondi.

Chikondi chimapereka mwai wosankha chingakhale pamene chisankho chizapweteka kwambiri wopereka chisankho. Ngati Mulungu anali ndi chizolowezi cholowerera nthawi zonse ana ake akamalunjika ku njira yolakwika, ndiyeno zenizeni nzoti iwo sakanakhalanso ndi ufulu wa chisankho. Pali nthawi yolangiza ndi yakukonza, komanso pamabwera nthawi pamene kukhala chete kwa wopereka chisankho amatsimikizira mawu onse woti “Ine ndimakukonda iwe.” Analankhula, chifukwa chikondi chopanda chisankho sichikondi konse. Izi ndi zenizeni kuti makolo onse amabvutika nacho pamene achita ndi ana awo. Malangizo onse ataperekedwa ana athu nkusankha kutsutsana nafe, timawaletsa iwo kutsatichitira ululu wokanidwa? Kapena timakhala chete ndi kulira,

kuwavomeredza chisankho chawo chotikana? Ndichisankho chobvuta kwa kholo lilonse.

Mulungu, mu chobvala cha chikondi, mwachete anamuona Eva, mwana Wake wamtengo wapatali, akukhala chida chomuwongera mwana Wake wokonedwa Adamu. Pa nthawiye nkuti mulingo wa kupweteka m' mtima wa Mulungu kunali kosaneneka. Kodi kupwetekaku kwa kutayika kwa mwana Wake wamkazi kungapangitse Iye kulowererapo kupulumutsa Adamu? AYI. Chikondi cha umulungu chimalira kwambiri ndi kudikira mwachete, kutsimikizira kupitirira funso kuti zoonadi Iye ndi Mulungu wa ufulu ndi ufulu wosankha. Iye alola Adamu kusankha yekha. Tikamanena za mayeso, chonde tisalole lingaliro lolakwika kuti Mulungu amayang'ana mosasamala zochitika za yeso kuchokera kuchitetezo cha kumwamba kuwona ngati Adamu ndi Eva anali nazo zowayenereza kukhala chiwalo cha gulu la kumwamba. Mulungu nayenso amayesedwa chimodzimodzi monga Adamu ndi Eva pa nthawiye. Chifukwa Mulungu amadziwa kuti ngati Adamu ndi Eva angagwe, ndiye kuti agwiritsa chikole chimene anatsimikizira dziko lisanalengedwe kupereka moyo wa Mwana Wake – Yesu Khristu.¹⁹ Khristu atha kuwonetsa iwo m'mene Atate Wake aliri; Iye atha kutenga kupalamula kwawo pa Iye yekha ndikulola kupalamulako kuwononge moyo Wake kusiyana kuti miyoyo yawo yiwonongeke. Zonsezi Mulungu amadziwa bwino lomwe pamene Iye amayang'ana Eva ndipo kenako Adamu akusankha kustusta Iye. Kodi ndi chikondi chanji chinali m'kukhala chete? Chiwonetsero cha chikondichi chizachotsa nthawi zonse lingaliro la bodza kuti Mulungu anasunthika ndi chidwi cha yekha pochita ndi makolo athu oyamba.

Tinakambirana m'chaputala choyamba nzeru imene Adamu ndi Eva anayikumbatira pamene iwo anadya kuchokera ku mtengo uja ndipo tinakambirananso m'chapitala chapitachi za zomvetsa chisoni m' mtima zimene zinamtsogolera Satana kupeka ganizo loti tikhoza kukhala ndi moyo popanda Mulungu ndi kupanga kudziwika kwa ife eni ndi zomwe ife tapeza. Ingakhale pamene chipatso chimagayidwa m' mimba mwa Adamu ndi Eva, mtambo wosakhala bwino wa uchabechabe ndi wopalamula pang'ono ndi pang'ono umazinga manganizo awo, kusekera kukonedwa kuja, kutsangala

¹⁹ 1 Petro 1:20; Chibumbulutso 13:8

ndi ubale mwachimwemwe pakati pa Mulungu ndi munthu. Temberelo la Batire lolimba la mtengo linayama kugwira nthito yake yoipisa, ndipo pa nthawi yochepa Adamu ndi Eva anazunguliridwa ndikutsutsika ndi mantha. Iwo, pamodzi ndi Satana ndi angelo ake, m'maganizo ndi malingaliro anazipha. Iwo anataya kudziwika ndi kufunikira kwawo, ndipo panalibe akanachita kuti azibwezeretse. Iwo sakanatha kuzibwezeretsa kukukondana ndi Mulungu. Iwo anapwanya ubale ndipo ndi Mulungu yekha amene angaubwezeretse. Fundoyi njachidziwikire yokha ngakhale m'mene ife timaonetsera mu zochitika zathu zomwe. Ngati wina waphwanya ubale ndi ife, mphamvu yobwezeretsa ubale uja yimakhala ndi mbali imene sinalakwiridwe; mbali yolakwira agonja ku ulamuliro mu ubale.

Pa nthawiyi nkwabwino kukumbukira pa zimene tinaona m'chaputala chachiwiri. Mulungu ndi gwero kapena kuti chiyambi cha moyo, nzeru ndi chimwemwe. Adamu ndi Eva azidula okha kuchokera ku gwero pokhulupirira bodza loti iwo akhala ndi zonsezi mwa iwo okha. Mphamvu zawo zoganiza sizingagwiridwensomo mosadzikonda kapena kuti moyenera. Maganizo awo ali wogwirizana kwa thunthu ndi Satana. Iwo alibenso kuthekera kovumbula mabodza Satana akuwawuza. Satana wayamba kuwadzadza iwo ziphunzinsomo zonse zonyenga zokhuza khalidwe la Mulungu. Pa nthawi yomweyo Satana akuwawuza Adamu ndi Eva kuti iwo ndi woipa. Satana akuyetsetsabe kutikhotesera ku gehena powononga malingaliro athu za kudziwika kwathu, ndipo iye akupanga ichi potiwuza ife mabodza za Mulungu ndi mabodza a ifenso. Tikango khulupirira ife mabodza za Mulungu ndi a ifenso, ife sitingathenso kulungamitsidwa kwa Mulungu. Njira yokhayo kuti tibwezeresedwe mu ubale wanthu ndi Mulungu ndipodziwa moona khalidwe Lake momwe linawululidwira mwa Mwana Wake.

Mlendo walekanisa mabwenzi abwino. Mulungu akubwera kuwayendera ndikuitana Adamu ndi Eva, koma mau iwo amawamva wokometsetsa m'chirengedwe tsopano akuwapatsa iwo kubitsala m'mantha ndi mosimidwa. Mfundo za Satana zagwira ntchito yake.

Lingalirani mukubwera kuchoka ku ntchito tsiku lina, mokondwera kuyembekezera mwambo okondwa mwakhazikitsa ndi mwana wanu. Madzulo alionse mwana wanu akubwera akuthamanga kutuluka khomo la

kutsogolo la nyumba akuyimba, “Abambo, Abambo,” kenako akuziponya m’manja mwanu mwachifundo kukumbatirana. Pamene mukuyandikira ku nyumba inu mukupeza kuti mwana wanu wokondwedwa sanabwere kuzakupatsani moni. Mosamvetsa, mukulowa khomo la kutsogolo ndipo mukumva mapazi a mwana wanu akuthamangira mwamantha m’ munda kukabisala. China chake chaphwanya ubale. Pamene panali chikondi, tsopano pali mantha. Palibe bambo weniweni amasangalala ana ake akamamuthawa akamva mau ake. Zimapweteka. Ndichisoni chimene tchimo limatipanga ife kuchita mantha kwa wachikondi choposa, wopasa, woleza, wokonda ufulu Munthu m’chilengedwe.

Mulungu wagwidwa njakata. Iye ayandikira bwanji Adamu ndi Eva tsopano pamene akumvetsera mau a wina? Liwu liri lonse anga lankhule tsopano litanthauzidwa m’kuwala koipa. Iwo akudziwa kuti ngopalamula, koma tsopano alibe chitetezo kapena woyenera kumvomereza kuti iwo ngolakwa, atamvomereza maganizo wonyenga za Mulungu, amene ali gwero la moyo ndi nzeru. Akulamulidwa ndi mzimu wopalamula ndi wosatetedwa iwo akhala amwano. Iwo ataya mphamvu zolingalira moona mtima.

Ine ndimazizwa pa chikondi cha Mulungu anachisonyeza m’kuleza mtima. Mulungu akuitana Adamu “Uli kuti?” osati chifukwa Iye sanadziwe koma kuti amulole Adamu awone nkhani. Malingaliro ako ali kuti Adamu? Chachitika ndi chani za kudziwika kwako? Chakuthupi nthawi zonse chimayimira chakuuzimu, ndipo kubisala kwa Adamu ndi Eva ku thupi momveka kumasonyeza kubisala kumene kunali m’ malingaliro awo. Aziveka okha m’chinyengo kupewa kukumana ndi chowonadi chikuoneka chochititsa mantha. Mulungu akuyesa kuwathandiza kuwona vuto ndikuti Iye angawabweretsere dalitso lothetsera vuto lawo.

Adamu anayankha funsolo pomuuzza Mulungu kuti Iye anali ndi mantha chifukwa anali maliseche. Kuululako nkosekesa malingana ndi malemba apa **Genesis 2:25. “Onse awiri ndipo anali a maliseche, mwamuna ndi mkazi wake, ndipo analibe manyazi.”** Adamu anali wamaliseche asanadye chipatso koma sanachite manyazi. Kumasulira pano nkoti Adamu tsopano ali maliseche. Liwu lachi Hebere (buwsh) limatanthauzanso kuti kusokonezeka, manyazi, ndi kukhumudwa. Adamu anadzadzidwa ndi kusokonezeka, kupalamula ndi kukhumudwa. Iye anali wosokonezeka za

zimene anali ndipo anamva kupalamula za zimene anachita. Mulungu tsopano akufuna kuyika chala Chake pa ululu wamphamvu mwa Adamu. “Wakuuza ndani kuti uli wamaliseche? Wadya chipatso cha mtengo ndinakulamulira kuti usadye?” Mulungu sakumufunsa Adamu, “Wadziwa bwanji kuti uli maliseche?” Iye akufunsa Adamu “Wakuuza ndani kuti uli maliseche?” Mulungu akulozera Adamu kwa amene anatsogolera mabodza iye anauzidwa. Mwa mau ena “Amene akupangitsa iwe kundithawa ndani?” “Ndani wabwera pakati pa iwe ndi Ine?”

Adamu akulankhulidwa mwachindunji, “Kodi wadya za mtengo uja, umene ndinakuuza iwe kuti usadye?” Iri ndi funso lophweka lofuna yankho lophweka inde kapena ayi. Tsopano poti m’malingaliro a Adamu chithunzi cha Mulungu chiri monga ngati wodzikonda ndi wobwezera ndipo iye monga ngati wopusa ndi wachabechabe, iye akuphatikiza ziwiri ndi ziwiri pamodzi m’malingaliro ake akupeza makhumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zinayi. Adamu akukhulupirira ngati akanena kuti inde, iye alangidwa mwaukali chifukwa tsopano monama akukhulupirira Mulungu ndi wobwezera. Iye akanena kuti ayi, akukhulupirira iye alangidwa kawiri, koyamba chifukwa chakudya kuchokera ku mtengo ndipo kachiwiri chifukwa chonama. Kukhulupirira palibe njira yopulumukira, Adamu akufuna kuziteteza ndi kuzilungamitsa yekha.

“Mkazi amene Inu munandipatsa ine, ameneyo anandipatsa ine za mtengo, ndipo ndinadya,” iye akuneneza. Mwamuna akuonekerathu ngopalamula koma iye akupereka mlandu kwa Eva ndi motheradi kwa Mulungu. Inu mungaganizire mantha a Eva pa mwamuna amene posakhalitsa pambuyopa analonjeza akumana ndi iye m’china chiri chonse chingaabwerere, koma pa vuto loyamba wagwa kale pansu pa nkhope pake. Tchimo siringapange wopambana amene angazipereke yekha wosazikonda kuthandiza ena. Nthawi zonse nzotsatira mwa mwamuna aliyense kwa iye yekha.

Sitikufuna tiphonye ndondomeko ikuchitika pano. Zochitika za Adamu zikuwongoledwa ndi kupalamula ndi kusatetezeka kwake, kuphatikizana ndi lingaliro lonyenga la khalidwe la Mulungu, zonse zolimbikitsidwa kwambiri ndi kunyada. Tsopano poti sakudziwonanso yekha monga mwana wa Mulungu, iye ayenera kukumbatira nzeru yoti “Ngati sindiziyimira ndekha, palibenso wina atha!” Akuganiza chonchi chifukwa akukhulupirira kuti

alibeno bambo. Pano pali kusweka mtima kwa tchimo: Mulungu awonetsa bwanji Adamu kuti ali ndi chithunzi chonyenga cha Atate ake ndikuti sali wachabechabe ndi wopusa? Adamu angapasidwe bwanji kuunikira koono kwa makhalidwe ake pamene wataya mphamvu yakulingalira moyenera? Mulungu ndi gwero lokhalo la nzeru zoono ndipo Adamu wazichotsa yekha ku gwerolo. Ndipo ngakhalebe Adamu akulingalira, lingaliro lake lingamasulidwe bwanji kukupalamula kophatikizana ndi kunyada kumene kukukana mwaukali china chiri chonse chofanana choonadi? Adamu sangasamalire Mulungu akumuuzira iye kuti ngolakwa, ngakhale zitachitidwa mwachikondi chifukwa cha iye mwini, chifukwa kusatetezeka kwake kukulamulira lingaliro lake.

Ndipemphero langa loona mtima kuti muone kuti pamene Adamu ndi Eva atangozisiyanitsa okha kwa Mulungu, anali otayika wopanda chiyembekezo choti angatengedwenso. Iwo anali wolamulidwa kwathunthu ndi mzimu wa Satana. M'mitima yawo munagonera mbeu yomwe kenako yitsogolera ana awo kuphatikana ndi angelo woipa m'mugwirizano wosachiritsika woyesa kupha Mwana wa Mulungu m'Yerusalemu. Ngakhale sizinawonetsedwe mokwanira, mitima yawo simafuna kuchita chiri chonse chokhuzana ndi Mulungu kapena ufumu Wake; osadzindikira ichi iwo ankadana ndi Iye kwenikweni.

Pa nthawiyo mwina mungayetsedwe, “Dikirani, inu mwazitengera patali. Ine ndikuzindikira kuti iwo anali ndi vuto, koma kunena kuti ankadana kwenikweni ndi Mulungu ndi kusinjirira zinthu.” Poyankha ndinganene kuti tiyenera kukumbukira kosalekeza kuti ubwino wonse, chikondi ndi nzeru zimachokera kwa Mulungu. Siziya mbira m'mitima ya anthu. Ngati tingayiwale fundo yofunikirayi sitingawerenge nkhanayi moonadi ndiponso sitingazimvetse tokha moonadi. Baibulo limanena momveka bwino pa fundoyi. Yang'anani mavesi atsaturawa:

Cifukwa cisamaliro ca thupi cidana ndi Mulungu; pakuti sicigonja ku cilamulo ca Mulungu, pakuti sicikhoza kutero.
Aroma 8:7

Monga kwalembedwa, Palibe mmodzi wolungama, inde palibe mmodzi; palibe mmodzi wakudziwitsa, Palibe m'modzi wakulondola Mulungu; Aroma 3:10, 11

Mtima ndiwo wonyenga koposa, ndi wosaciritsika, ndani angathe kuudziwa? Yeremiya 17:9

Baibulo limalengeza kuti mitima yathu m'chikhalidwe chathu, yimadana kapena kuti yiri pa nkondo ndi Mulungu. M'chikhalidwe chake, malingaliro athu ali opanduka, samagonjera ku malamulo a Mulungu, ndikosatheka kwa malingaliro athu kutulukamo m'chikhalidwechi. Ndapeza ine mu zochitika zanga, ndi m'zochitika za anthu ambiri amene ndagawana nawo izi, kuti pali mzimu wokaniza kwambiri ku choonadi. Mzimuu wokaniza ku mfundo yakuti khalidwe la munthu limadana kwathunthu ndi Mulungu, ndi kukaniza kunabwerezeka kwenikweni kumene Adamu anaonetsera kwa Mulungu, pamene ananeza Eva ndi Mulungu m'malo motenga udindo wa kulephera kwake. Kusatetezeka kwa Adamu ndi cholowa chathu ndipo sitingachite choonadi kuposa m'mene anachitira. Ngati mukupeza kuti mukukana nokha fundoyi, muzifunse nokha chifukwa chiyani mukutero? Ngati inu muli otetezedwa mwa inu nokha ndiye kuti ziganzozozi nzoti sizingakhuzeni konse. Kusatetezeka ndi uchabechabe wa Adamu ndi cholowa chathu. Ndichokhacho chimene angatipatse osati chinanso.

Ngati tingakumbatire zenizeni kuti khalidwe la munthu ndi la nkhanza kwa Mulungu, ndiyeno muli mothandizika kwenikweni. Mu nkhanzi ya ndondomeko ya Mulungu kutipulumutsa ife, muli ufulu kwambiri mukudzindikira kuti sitingachite chiri chonse chabwino. Mungasiye kuyesa. Mukhoza kusiya kuziguguda nokha pamene khalidwe lituphuka ndikumanya wina m'maganizo kapena mthupi, koma ndikufulumira mwa ine ndekha; tisunge izi ku gawo la patsolo.

Kubwerera pambuyo kwa Adamu ndi Eva, titha kuona kuti kuphwanya chotchinga pakati pa iwo ndi Mulungu itha kukhala ntchito yayikulu. Kuchira kwawo, ndi kuchira kwa ana awo, kuyenera kufuna zinthu zingapo:

1. Njira yomupatsira munthu nzeru kudzindikira m'khalidwe wawo wosachiritsika, pamodzi ndi njira kwa iwo kuwakopa m'malangizo olondola popanda kuphwanya ufulu wawo wosankha.
2. Njira yowaonetsera kuti iwo anali ndi kudzindikira kolakwika za khalidwe la Mulungu ndi ufumu ndi mwinamwake kuwaonetsera iwo kuti Iye amawakonda kwenikweni ndi m'mene Iye aliri kwenikweni.
3. Njira yowachotsera kupalamula ndi kusatetezeka ndi kuwabwezeretsera kudziwika kwawo koona ndi mtengo / phindu monga ana a Mulungu.
4. Njira yobwezeretsa lingaliro la cholinga chawo, chifukwa chawo cha kukhalako kapena tsogolo lawo.
5. Zonse ziri pamwambapa zimafuna nthawi. Adamu ndi Eva anapinyolitsa moyo wawo, ndipo amafunika dongosolo la moyo wothandizira kuwapasa nthawi yosankha chisankho.
6. Pamene akupanga zonse, Mulungu ayenera kukhalabe ndi m'lingaliro la chilungamo. Iye sanganyalanyaze kupanduka kwawo ndikunena kuti ziri bwino. Pamene Mulungu m'chifundo Chake sakulola zotsatira zonse za chisankho chawo kugwera pa iwo, Adamu ndi Eva ayenera kumvetsa chotsatira cha chisankho chawo kuti ayambe kuyamikira zolakwa za zimene anachita.

Pali nfundo yofunikira kwambiri ife tifuna kupanga pano. Mulungu sanadzidzimutsidwe. Atate ndi Mwana Wake anatsimikizika kale chimene angachite ngati angafike apa. Dongosolo linayikidwa kale m'malo – dongosolo lomveka bwino kukumana ndi m'khalidwe wosachiritsikau.

7. Mnzere Wa Moyo Wakumwamba

Mwakhama kuti afotokoze maonekedwe a chikondi cha umunthu kotherathu, a Herene anatulukira nkhani ya Admetus ndi Alcestis.²⁰ Mtumwi Paulo akutsimikizira ku nkhanayi mu buku la Aroma.

Pakuti ndi cibvuto munthu adzafera wina wolungama; pakuti kapena wina adzalimbika mtima kufera munthu wabwino.
Aroma 5:7

Mfumu Admetus anali wotchuka ndi kuchereza kwake ndi chilungamo, ndipo anakonedwa m’ufumu wake wonse. Mulungu Apollo anathamangitsidwa kuchokera ku phiri la Olympus ndi abambo ake Jupiter ndipo anauzidwa kuti asiye umulungu wake ndi kukhala munthu ndikutumikira munthu ngati kapolo. Atabwera ku dziko lapansi, mfumu Admetus anam’peza iye ngati wopemphapempha wosauka ndipo

anamumvera chisoni. Anamudyetsa iye ndikumupanga mbutsa wankhosa zake ndikumutenga ngati mwana wake. Patapita miyezi khumi ndi iwiri Apollo anasinthanso kubwerera ku umulungu wake ndipo anathokoza Admetus chifukwa chomuthandiza ndipo anamuza iye “Ngati ungazafune thandizo langa m’tsogolo uzangondifunsa.”

Patapita nthawi Apollo anabwerera kwa Admetus kuzamuza kuti Hades, mulungu wa kumidima, posachedwa azafunsa moyo wake. Apollo anati anapangana ndi mkazi wake Persephone, mkazi wa Hades, kuti ngati

²⁰ <https://en.wikipedia.org/wiki/Admetus>

pangapezeke wina kufa m'malo mwa iye sanayenera kufa. Admetus anapita kwa makolo ake kuwapempha kuti alowe m'malo mwake. Iwo anati, "Timakukonda mwana wathu, ndiwe munthu wabwino ndi wachifundo, koma timakonda moyo wathu kwambiri koposa. Sitingakufere iwe." Mfumu inayenda m'ufumu wake wonse kuti apeze wina woti angalole kumufera koma sanampeze m'modzi. Admetus anangobvomereza za tsoka lake ndipo pa nthawi ya mkazi wake, Alcestis, analirira kwa Apollo, "Wokonedwa Apollo, mwamudalitsa mwamuna wanga ndi kuchulukitsira kutchuka kwake ndi mwai kupinda ka khumi mu ufumu wathu wonse. Admetus ndi munthu wabwino kwambiri, ndipo anthu ake akumufuna kwambiri, moti ayeneradi kukhala ndi moyo! Ine ndifa m'malo mwake, kuti akhale ndi moyo." Ndipo anatero. Dziko lonse linalirira mkazi wabwino wa mfumu yabwino, amene anakonedwa kwambiri ndi anthu ake ndimene anafa kuti mfumu yake ikhale moyo. Ndipo atawonekera pamaso pa Persephone anamumvera chisoni iye, nauzidwa atha kukhalanso ndi moyo ngati mphoto ya kukhulupirika kwake kwa mwamuna wake. Ndipo kunali pamene Admetus ndi Alcestis amachuluka zaka, nkuti Apollonso amawapasa mphoto iwo chifukwa cha kukhulupirika kwawo, mpaka kenako Imfa inabwera kwa iwo atakalamba, anali wokonzekera iye.

"Ichi," anafuula anzeru achi Herene, "Ndi maonekedwe aakulu kwambiri a chikondi chimene chiripo – kuti munthu ataya moyo wake chifukwa cha abwenzi!" Anthu ambiri amalumikiza nkhanayi ndi mawu a Yesu pamene Iye anati:

Palibe munthu ali naco cikondi coposa ici, cakuti munthu ataya moyo wace cifukwa ca abwenzi ace. Yohane 15:13

Komabe ichi sikuya ndi kukwera kwa chikondi cha Mulungu, koma chabe mau akunena malire a chikondi cha munthu. Mtumwi akusiyanyitsa nkhanayi ya munthu ya malire a chikondi cha munthu ndipo akutiya ife:

Pakuti ndi cibvuto munthu adzafera wina wolungama; pakuti kapena wina adzalimbika mtima kufera munthu wabwino. Koma Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cake ca mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife cikhalire ocimwa, Kristu adatifera ife. Ndipo tsono popeza

tinayesedwa olungama ndi mwazi wace, makamaka ndithu tidzapulumuka mkwiyo wa Mulungu mwa Iyeyo. Pakuti ngati, pokhala ife adani ace, tinayanjanitsidwa ndi Mulungu mwa imfa ya Mwana wace, makamaka ndithu, popeza ife tayanjanitsidwa, tidzapulumuka ndi moyo wace. Aroma 5:7–10

Mulungu anaulula kuya kwa chikondi Chake polola Mwana Wake kuvulazidwa ndi zolakwa zathu ndi kutunduzidwa ndi mphulupulu zathu. Anapereka Mwana Wake chifukwa ca adani Ake, amene anadana ndi kumunyoza Iye, kuchokera mu chikondi Chake chachikulu ndi chifunda chapa iwo. Ichi si umunthu koma chikondi cha umulungu.²¹

Munthu asanalengedwe, Atate ndi Mwana Wake anali muzokambirana zozama zimene m’Baibulo limatcha uphungu wa mtendere.²² Pa nthawi ija, dongosolo linayikidwa kuti chizachitika ndi chiyani ngati munthu azasankha kutsutsana Nawo. Tsopano inali nthawi yochita. Ndani angayerekeze kuvutika kwa Mulungu? Kodi alola Mwana Wake kulowa m’ malo mwa Adamu ndi Eva ndi kulipira dipo la zotsatira za chisankho chawo? Alola Mwana Wake kutenga pa Iye yekha uchabechabe wao ndi kupanda chiyembekedzo kutengera ku manda? Alola Mwana Wake kuvutika kotaya kudziwika ndikutaya Umwana Wake chimene chipangitsa kunena mau kuchokera m’mtima Mwake, “Chifukwa chani Inu mwandisiya Ine?”

M’mene ndikulemba mauwa, mwana wakhala mwamtendere moyang’anana nane. Ndikayang’ana nkhope yake yokongola ndikumva lingaliro la chimwemwe ndi chikondi zotuluka m’mtima mwanga chifukwa cha iye. Ndiyeno ndikuyesa kulingalira kuziyika m’ malo mwa Mulungu, kulola mwana wanga kuzitengera yekha chilango cha imfa cha gulu la anthu amene tsopano akudana nane ndi zinthu zanga zonse. Ndikuulula kuti malingaliro anga amangotseka maganizowo. Singalolenso kuganiza malingalirowo. Ndikudziwa kuti ngakhale ganizolo ndilopweteka kwambiri ndipo kuchita nalo ndikhoza kugwa! Maganizo anga akubwerera kwa Mulungu ndi njakata

²¹ Zambiri onani bukuli *The World That Turned The World Upside Down* lolembedwa ndi Robert Wieland <http://fatheroflove.info/download/view/863>;

²² Zekariya 6:13

Yake ndipo ndimamva dzanzi. Ndimamva lingaliro lakuya kwambiri la chiyamiko kwa Iye polola kuti zichitike, podziwa kuti ine ndine m' modzi wa anthuwo amene, pokhala adani a Mulungu, apatsidwa moyo kupyolera m'nsembe yolowa m'malo ya Mwana wa Mulungu. Ganizoli nthawi zonse limandipanga kuyima ndi kupembeza Iye mu kuyamika chifukwa cha chikondi chake ndi nsembe yopanda malire.

Ndine wodabwa kuti Mwana wa Mulungu, amene anabwera kukhala Yesu munthu, analola kuchitira ife ichi. Baibulo limatiuza ife kuti Mulungu amadziwa chimalidziro kuchokera pa chiyambi, ndipo Atate anagawana chidziwitsochi ndi Mwana Wake. Tchimo litangowononga chirengedwe, Iye anadziwa ndendende kumene zimapita. Kristu anatha kuona chimene chimamudikirira pamene anabwera pa dziko lapansi: kukanidwa, kumenyedwa, kunyogodoledwa, kudedwa, kutukwanidwa ndi kulumbira, maliseche ndi mdima pa mtanda, uchabechabe wa miyoyo yankhanikhani kuunjikidwa pa Iye, ndi unyinji wakupalamula ndi chisoni cha mazanamazanasa a mibadwomibadwo. Iye anaona zonsezi komabe Mwana wa Mulungu anati, "Kucita cikondwero canu kundikonda, Mulungu wanga; Ndipo malamulo anu ali m'kati mwamtima mwanga"²³ Mwana wa Mulungu sanavomere monyinyirika kubwera, koma m'malo mwake, Iye anakhumba kuchita ichi. Mtima Wake, monga mtima wa Atate Ake, akulakalaka kubwezeretsa ana Ake ku chidzalo cha chimwemwe kukhala tsogolo lawo. Kodi Mulungu wa mtundu wanji ameneyu? Iye tizamuyerekezera ndi ndani ndipo ndi mau anji wokwanira womutamanda Iye?

Tinaona m'chaputala chapitachi kuti Adamu ndi Eva amafunika dongosolo la moyo wotheadizira ndi luso lozindikira choonadi kuchokera ku zolakwa zao; amafunika thandizo kuti aone choonadi za Mulungu ndikudzindikira, kubvumbula ndi kukana mabodza amene Satana amauza iwo. Iwo amafunika kalodzera wamakhalidwe kuwathandiza kudzikindikira kumpoto koono kwa uzimu.

²³ Masalmo 40:8

Zinthu zonsezi zikhoza kupatsidwa kudzera / kupyolera ku mphatso ya Mwana wa Mulungu ku dziko lapansi. Izi zinanenedwa kwa Adamu ndi Eva mu Genesis 3:15. Polankhula mwachindunji kwa Satana motere:

Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace. Genesis 3:15

Vesiri ndilodzadza ndi malonjezo ndi chiyembekezo. Mulungu anati ayika udani pakati pa Satana ndi mkazi. Pamene Mulungu akunena za mkazi, Iye akunena kwa onse abadwe mwa mkazi, mwa mau ena kwa mtundu wonse wa anthu. Liwu loti udani likutanthauza kuti mdani.²⁴ Mulungu ayika china chake m'mtima wa banja la munthu chodana ndi zoipa ndi kukhumba chabwino ndi choonadi. Pali chifukwa chimodzi chokha Mulungu akutha kuchita ichi, ndichifukwa choti Mwana Wake ayanjanitsa banja la munthu kudzera mu moyo ndi imfa Yake pamene ali pa dziko la pansi. Ichi ndicho tandauzo lake la udani kukhalapo pakati pa Mbeu ya mkazi ndi mbeu kapena kuti ana a Satana. Paulo, mu buku la Aroma, akutanthauza za udaniu wa zoipa monga chisomo kapena mphamvu m'vesiri lotsatirali:

Koma mphatso yaulere siilingana ndi kulakwa. Pakuti ngati ambiriwo anafa cifukwa ca kulakwa kwa m'modziyo, makamaka ndithu cisomo ca Mulungu, ndi mphatso yaulere zakucokera ndi munthu mmodziyo Yesu Kristu, zinacurukira anthu ambiri. Aroma 5:15

Luso losankha chomwe chiri cholondola limachokera ku udani umene Mulungu anayika mu mtima kudzera ku mphatso ya Mwana Wake. Mphatso yomweyonso imaperekanso mphatso yofunikira kwambiri ya moyo.²⁵ Paulo akunena za mfundoyi m'chaputala chomwencho cha Aroma:

²⁴ Vines Expository Dictionary-Enmity

²⁵ Pamene tikunena za moyo pano, tikunena za moyo obwereka, osati moyo wa m'yaya. Mulungu wapereka kwa munthu aliyense pa dziko lino moyo wosankha kapena kukana choonadi za Mulungu ndi ufumu Wake.

Chifukwa cace, monga mwa kulakwa kumodzi kutsutsa kunafikira anthu onse; comweconso mwa cilungamitso cimodzi cilungamo ca moyo cinafikira anthu onse. Aroma 5:18

Ichi ndi choonadi chosaneneka chomwe chingabweretse mtendere ndi chimwemwe choposa muyeso. Mfundo iri pamwambapa ikutanthauza kuti mpweya uli onse mupuma (Kaya mukukhulupirira mwa Mwana wa Mulungu ndi nsembe Yake kapena ayi) ukuchokera mwachindunji kuchokera kwa Yesu Kristu. Ndi moyo Wake umene ukupangitsa mtima wanu kugunda ndi kupangitsa inu kupuma ndi kusunga inu ndi moyo. Zintchito zonse zimene ife timati sizaufulu ku mbali yathu zedi nzaufulu ku mbali ya Mulungu. Iye ndi mtima wa choonadi chimene chimati:

...kuti afunefune Mulungu, kapena akamfunefune ndi kumpeza, ngakhale sakhala patari ndi yense wa ife; pakuti mwa iye tikhala ndi moyo ndi kuyendayenda, ndi kupeza mkhalidwe wathu; Macitidwe a Atumwi 17:27, 28a

Mulungu sali kutali kwa wina aliyense wa ife timachirikizika ndi moyo wa Yesu Kristu ndi ukoma / makhalidwe Ake okhalapakati chifukwa chathu kudzera mu imfa Yake pa mtanda. Ngati inu mukumva kuti Mulungu ali kutali choonadi nchoti Iye salikutali ndi inu. Inu muyenera kungomva ku gunda mtima wanu kuti mudziwe kuti Iye sanakusiyeni.

Wonjezerani ku izi mfundo yoti Mulungu amaika m' mitima yathu khumbo lochita chabwino ndi khumbo lokana choipa, kenako moona tiri ndi zambiri zothokozerera. Taganizirani nthawi zimene inu mwayesedwa kuchita china chake cholakwika ndipo kenako mwaganiza bwino ndi kusachita. Iyi inali mphatso Mulungu wakupasani inu, udani wotsutsana ndi choipa. Palibe kanthu kuti mumakhulupirira mwa Mulungu kapena ayi, munapatsidwabe mphatsoyi kudzera mwa Yesu pamene mwasankha kuyigwiritsa ntchito. Timauzidwa m'malemba kuti Mulungu amagwesa mvula pa abwino ndi woipa.²⁶ Taganizirani pamene nthawi zambiri Satana waika maganizo woipa m'malingaliro a winawake kukuchitirani inu kapena kutenga zinthu zanu, ndipo udani unaikidwa m' mitima ndi Mulungu analimbikitsa kusachita choncho. Inde tiribe ndi chisankho kukana kulimbikitsidwa kuja ndi

²⁶ Mateyo 5:48

kupitiriza kupanga choipa, koma ngati udani uja panalibe wina wa ife akanatha kusiya kuchita choipa chimene chayikidwa m'malingaliro.

Atate wodabwitsa kupanga zonsezi chifukwa chathu. Ife ndife mtundu wa anthu amene tinatayika kwathunthu ndi kutengedwa ukapolo mu njira zoipa za Satana. Tapitira kotherathu pozithandiza tokha, wothedwa ku mavuto ndi kuchiwonongeko chotherathu. Koma Atate wathu wakumwamba wachifundo anakana kutinyanya ife. Anatipatsa ife chinthu cha mtengo wapatali kwambiri chimene ali nacho – Mwana Wake. Yesu azakhala nthawi zonse m'modzi wa banja la munthu ndipo m'modzi wa ife. Iyi ndi nsembe imene izakhala pakatikati pa mutu wa maphunziro ndi kulingalira kwa muyaya.

Pamene mukuganiza za zinthu izi, mukumva bwanji za zonse zimene Mulungu wakuchitirani inu? Mzimu Wake akukokerani inu tsopano kumulandira Iye ndi kukhulupirira choonadi za Iye. Amafuna kuti mudziwe amakukondani inu modziperekadi ndipo akupatsani chiri chonse kuti akubwezeni. Ine sindingakane chikondi cha mtunduu, chikundikakamiza modabwitsa kwambiri.

8. Kufanaiza Ma Ufumu Awiri

Tisanapite patsogolo zitithandiza tichite kaye mwachidule maufumu awiri wosiyana kwambiri amene panopa ali pa dziko; ufumu wosatha wa Mulungu ndi ufumu wa Satana, awiriwa anaperekedwa kwa Adamu ndi Eva mu Munda wa Edeni. Titaganizira kwa kanthawi pang’ono chimene chimathandauzira ufumu, pali zinthu zitatu zofunika kuziona:

1. **Boma:** Dongosolo limene ufumu umalamulidwira. Mwachisanzo, demokalase kapena kupondereza.
1. **Ndalama:** Dongosolo la mtengo limene nzika mu ufumu angasinthanitsire katundu wao.
2. **Unzika:** Njira yodziwira m’mene wina angakhalire chiwalo cha ufumuo.

Tingasiyanitse maufumu awiriwa mu njirayi:

	Ufumu wa Mulungu	Ufumu wa Satana
Boma	Banja	Wamphamvu
Ndalama	Chikondi / Chifundo / Ufulu Wosanka / Chikhulupiriro mwa Mulungu	Mphamvu / chuma kapena katundu / chikakamizo / Kuzikhulupirira
Unzika	Mwana wa Mulungu	Kutakata / Kupambana

Boma la Mulungu nlokhazikika pa dongosolo la ubale. Mkulu wa boma ndi Atate. Ubale pakati pa mtogoleri ndi nzika zake ngwapafupi ndi wapamtima. Pamene ufumu wa Satana umadalira kukhala ndi mphamvu. Amene ali ndi mphamvu ndi amene amalamulira. Ngakhale m'demokakase, amene ali ndi mphamvu kulengeza uthenga wao ndi kuwakopa mwamphamvu ovota akhala wolamulira.

Ufumu wa Mulungu umagwira ntchito mu mphamvu za ubale wake. Chikondi ndi ndalama ya kumwamba. Nzika nzotetezeka mu chikondi cha Atate wao ndipo sayeneranso kutsimikizira kufunikira kwao kapena phindu lao. Iwo angasangalalirane wina ndi mnzake pa gulu lao mosavuta popanda kampeni ku mphasa. Kuphunzira kumudziwa Mulungu ndi chimwemwe chopambana kwambiri ndi khumbo²⁷, ndipo chifukwa chidziwitso cha Mulungu ndi nzeru ndi khalidwe nzopanda malire, ntchito yotsangalalay siizatha. Pazakhala nthawi zonse china chake chophunzira za Iye. Nzika zake zikuphunzira za Iye kuchokera kwa Iye mwini kapena kudzera ku zinthu zimene Iye anazirenga. Choncho poyang'anirana wina ndi mnzake ndi kuphunzira makhaliidwe ndi chirengedwe ndi mbalinso ya chisangalalo yokhala m'ufumuu. Popeza zamvomerezeka momveka bwino kuti chiri chonse chimachokera kwa Atate, cirengedwe chonse chimapembeza Iye ndi chisangalalo choyamika ndi chithokozi.²⁸

Kuyerekeza ndi uwu, ufumu wa Satana umagwira ntchito m'chuma kapena katundu. Kufunika kumabwera kuchokera ku zomwe tapambana, choncho kudzikundikira chuma nkofunika kuti tikhale apatali. Chumachi chikhoza kukhala katundu, maganizo, kapena ubale. Nyumba ikakula, zinthu zambirinso zokhala nazo, ukhalanso ofunikira kwambiri. Maphunziro akakwera, udindo ukwera pa ntchito uli nayo, kufunika ukhalanso. Anthu amene umagwirizana nawo ndi ofunikira kwambiri chifukwa munthu akhoza kukhala wodalirika kwambiri pa ntchito yako. Ufumu wa Satana umakhulupirira kuti anthu ali ndi mphamvu mkati mwao, choncho kukhala ndi anthu ena zikhoza kukupanga kukhala wamphamvu kwambiri. Maubale ndi anthu chakhala chida chimene chimatipindulitsa kwambiri. Ichi chimapangitsa kufuna kulamulira anthu ena ofunikira kwambiri. Kukhala


²⁷ Afilipi 3:9, 10

²⁸ Chibvumbulutso 14:6, 7; Chibvumbulutso 4:1-9

wabwino ndi ochezeka ndi zofala. Ichi chimagwiritsidwa ndi amalonda nthawi zonse. Kuchita zinthu zazikulu kukhoza kupanga athu kukutsatirani, ndipo zikaléphereka mutha kugwiritsa mphamvu, kuwanenera zoipa ndi kuopseza kuti mulamulire anthu ndi kuteteza chikhulupiro chao pa inu. Nchifukwa chake ma ubale ambiri ndiodzadza ndi ululu ndi chisoni lero, chifukwa anthu nthawi zambiri agwirizana kuchulukitsa kufunikira kwao ndi phindu lao.

Kusiyana kwina kumene taona ndi unzika. Mu ufumu wa Mulungu m'mawerengedwa nzika pongokhala mwana wa Mulungu. Mosasamala zochitika kapena mavuto a moyo mfundoyi siisinha. Unzika wanu ndiwotetezedwa mu ubale wanu kwa Mulungu ngati Atate wanu. M'ufumu wa Satana m'mawerengedwa nzika pochita kapena posachita kanthu. Zonse kupambana ndi ulesi zikupasani inu unzika ndi inu mukalunjika kuchita ndi kupanga chinachake. M'ufumuu mukadzuka m'mamawa uli wonse ndikuganiza choti mukwaniritse tsikulo m'mamva bwino za in nokha. Ngati anthu akukupingapinga khama lanu kuti mukwaniritse, m'makhumudwa ndi kukwiya. Ngati mwafika pa mapeto a tsiku ndi kumva kuti simunakwaniritse zambiri, m'mamva kuperewera mwinanso kutaya mtima kapena kulimbika kwambiri. Moyo ndi mkombero wozungulira pa kunyada ndi uchabechabe / kuperewera. Pamene mwakwaniritse m'makhala onyada ndipo pamene mwalephera m'mamva kuperewera. Moyo pakati pa kupambana ndi kulephera zimapangisa kutsimikiza kuti m'kwaniritse, kapena mantha kuti zimene mwapeza zizatayika. Uwu ndi Mkombero wosatha mpaka mtafa kapena kusintha maufumu.


Maganizo a Mkombero m'Ufumu wa Satana



Uwu ndi mkombero wazotsatira zosavuta zokhulupirira kuti tiri ndi mphamvu mwa ife tokha. Ngati ife timazipasa mphamvu tokha ndiye kuti ife sitidalira pa wina ndi kupeza phindu / mtengo kuchokera kwa wina. Tiyenera kukulitsa ndi kupanga phindu la ife eni. Kupambana kuli konse kumatitsimikizira ife ndipo kulephera kuli konse kumatsogolera kukusakhalakonso.

Ndikukumbukira mkangano m’mtima mwanga pa nthawi yanga yoyamba kuchita ulaliki. Ndimamva kudalitsika pamene ndinaalodzera anthu ku choonadi cha m’Baibulo, koma pamene ndinayima pa khomo kuwapatsa moni anthu ali pa m’nzere ndimafuna kuti andiuze kuti ndinachita bwino, ndikunditsimikizira pa chimene ndinachita. Ine ndikalalikirira bwino mtima wanga umafunanso kuyamikidwa kwambiri. Ndimadziwa kuti sibwino kuganiza mwa njirayi, choncho pakanthawi pamene anthu akandiuza kuti ndinayankhula bwino, ndimati “Zikomo Mulungu, musayamike ine”, koma nthawi zambiri sizimaoneka bwino ndipo nthawi zina anthu amamva ngati ndawakankha kutali. Pamene tadzindikira kuti zinthu zonse zabwino zimachokera kwa Mulungu ndikuti timalemekezeka ndi Iye pa mbali pa chiri chonse timachita, ndiyeno mfulu kupambana ndi kulephera popanda kukhumudwa za kumva kuperevera ndi kumva kufuna chitsimikizo kapena kuyamikidwa kuchokera kwa ena.

Maganizo a Mkombero m’Ufumu wa Mulungu



Nkofunikira kukumbukira kuti ziwalo za ufumu wa Mulungu sapeza ulemere wao kuchokera ku zomwe akwaniritsa, iwo amakwaniritsabe. Chooni chake ndi choti iwo ali ndi kuthekera kukwaniritsa zambiri chifukwa ngati alephera sayenera kuyang’anana ndi mantha a kuperevera

kwao. Iwo amakonedwabe, ndi anabe a Mulungu osasamala kaya apambana kapena alephera. Ufumu wa Mulungu umakupatsani njira yabwino kukwaniritsa kuthekera kokwana popanda kusiya maubale anu m'mansanza ndi ulemu wanu kuonongedwa.

Mwachidule tatambasula makhalidwe a maufumu awiriwa. Kwina konseko mu bukuli tifufuza m'mene maufumu awiriwa akulira m'nzeru za mbiri ya munthu ndi kulimbana kumene nthawi zambiri timakumananako tikamakhala pakati pa awiriwa. Ma ufumu onsewa amapereka ufulu, onse amalonjeza zambiri, koma ndi ufumu uti uzakusiyirani malingaliro akuya atanthauzo ndi kuyenera kumene nkosagwedezeke.

9. Mtima Wa Babulo

“Tinalakwisa pati ife?” Bambo wosweka mtima analira pamene amalimbana kuti amvetse zoonza za zomwe amakumananazo tsopano. “Tinali ndi banja labwino ndipo akudziwa kuti timamukonda iye” akupitiriza bambo pamene movutika akufunafuna malongosoledwe ena zifukwa zomwe mwana wao m’nyamata wangomangidwa ndi makhwala ozunguza bongo, kuba ndi kupha.

Kulira kosweka mtimaku kwakhala kukunenedwa nthawi zambiri kuposa m’mene timaganizira; makolo kukhala ndi manyazi ndi ululu za mwana amene wagwa mu moyo wopanduka ndi wa zoipa. Gwero la kulira mosweka mtima zikhoza kufufuzidwa kuchokera kwa makolo athu oyamba ndi tsoka la mwana wao oyamba Kaini. Makolo azadziwa chimwemwe Adamu ndi Eva anachimva pamene anagwira koyamba khanda Kaini m’manja mwao. Mphatso ya chikondi chao tsopano yinali yao kuyigwira ndi kusangalala. Pamene Eva anam’gwira mwana watsopano wa mtengo wapatali, analira mwachimwemwe, “Ndalandira munthu, Ambuye!”²⁹ Eva anakhulupirira kuti Kaini akhala Mbeu yolonjezedwa yonenedwa m’Genesis 3:15 imene ibweretse machiritso ndi madalitso ku mitundu yonse. Zikanangokhala zoonza, chifukwa zowawa zoonza kwa Eva zinali zoti mbiri ya Kaini ibweretsa mavuto, chiongeko ndi imfa ku anthu ochuluka. Kaini anakhala mutu wa mtundu wa wopembedza amene mkhalidwe wa zochitika za uzimu nza iwo eni. Mtundu wa anthuwa uli wochulukirapo pa chierengero cha dziko, mtundu wa anthu amene Baibulo kenako analitcha Babulo. M’chaputalachi

²⁹ Kuwerenga kwenikweni kwa Genesis 4:1

tifufuza mzimu umene ukutsogolera mtunduu wa anthu ndi m'mene umakhuzira inu ndi ine.

“Abambo, nchifukwa chani tiyenera kupha nkhusa yosalakwa?” Kupha kwa nkhusa kunakonzedwa ndi kunayikidwa kwa banja la munthu kuti zionetsere khalidwe la munthu kwa Kristu motero afune kulapa. Choncho chikubvumbulutsa mtengo umene Mulungu anali olola kupereka kuti ife tione chikhalidwe chathu, ndipo kudzera ku chikoka cha Mzimu, kupempha chikhululukiro. Mphatso yodabwitsa yaperekedwa chifukwa cha chipulumutso chathu. Unali mwambo olodzera mwachindunji ku masautso a Kristu pa nthawi ya nsembe. Zinalodzeranso kutsogolo pamene Kristu adzabwere ku dziko la pansu kuulula Atate. Imalodzeranso kumbuyo ku manyazi za zimene munthu wachita kwa Kristu kuchokera pamene anagwa m'Edeni. Zinali chikumbutso cha chithonhozo za chikondi chodabwitsa cha Mulungu komanso pa nthawi yomweyo chikumbutso chopweteka cha munthu kusathokoza ndi dyera. Kutenga nawo mbali mu utumikiu utha nthawi zonse kupangitsa maganizo wosakanikira. Kuyang'anitsa pa nkhope ya nkhusa yosalakwa ndi kuyang'anitsa ululu wachete zikhoza kuonetsa mwa mphamvu kudzikonda ndi kuzipereka. Kwa onse amene amayang'ana pa nkhope ya Nkhosa yoona ya Mulungu, chiyembekezo nthawi zonse chisakanikira ndi moyo wa ululu umene umabwera pomvetsa mkhalidwe wa munthu umachita kwa Kristu. Mkhalidwe wa munthu kuyankha ku mtanda ndi mwina kulembanso chiyambi cha munthu pokana kuti kugwaku kunachitika poyambapo, kapena kuyika kufuna imfa pa Mulungu ngati chinachake Iye amafuna kukwanitsa m'kwiyo Wake potsutsa tchimo. Mu zochitika zambiri mtanda umasandulika kuchokera ku kuunika ku mdima, kapena kuonetsedwa moipa ngati chizindikiro cha chiyembekezo pamene moonadi kuyimira chizindikiro cha chinyengo chimene nchoyambitsa kudziwa.

Patapita zaka zambiri akuona makolo ake akupha nkhusa ndikuonanso m'maso mwao misonzi ndi chisoni kuphatikizapo ndi chiyembekezo, kuleza ndi chidaliro mu Mbeu yobwera, Kaini anaganiza kuti iye sapiriranso kufunika kwa kudzichepetsa ndi kulapa. Poganzira pa kulephera kwa munthu kumene nkhusa yophedwa ikubvumbula, Kaini anasankha osakumbukira chikondi chakuya cha Mulungu m'mphatsoyi. Kwa Kaini, nkhusa inangolimbikitsa kusatetezeka kwake, mbali ya ukulu iye

analandirakuchokera kwa atate ake amene analandira kuchokera kwa Satana. Kwa Kaini nkhusa imangomuza kuti iye ndiwosavomerezeka kwa Mulungu m'kuyenera kwa iye yekha ndipo kuti khalidwe lake ndilosagwirizana ndi Mulungu. Mwachionekere Satana amamulimbitsa Kaini ndi ganizo lochotsa kupereka nsembe ya nkhusa m'chipembezo, motero dikukonzanso ubale wake kwa Mulungu pochotsa kufunikira kwa kulapa ndi ntchito zake.

Baibulo likutiya ife kuti Kaini anabweretsa nsembe ya zipatso kwa Mulungu.³⁰ Tikuzidwanso kuti Kaini anali mulimi olima chakudya ngati mbali imodzi ya ntchito yake. Nsembe ya Kaini inali chizindikiro cha khama lake kupeza ulemu wa Mulungu ndi ntchito za manja ake. Iye anasintha mapembezodwe kuchokera ku kuzichepetsa muchikhulupiriro kunka ku kuzionetsera monyada, kuchokera ku ubale wokhulupirira kwapamtima kukungokondweretsa. Chipembezo chotere chimanyalanyaza mfundo yoti tiribe mphamvu yokambirana kusintha zinthu ndi Mulungu; tiribe moyo wa ife tokha opumirapo ndikukumana ndi Mulungu pa mfundo za ife tokha. Mwachisoni Kaini anaiwala ichi. Satana anamulonjeza iye ufulu wozimasula yekha kuchokera ku kukhudzidwa ku tchimo ndi nkhusa, koma pochotsa nkhusa chipembedzo cha Kaini chinasintha kuchokera ku ubale wachikhulupiriro ndi Mulungu woona kunka ku miyambo yochitachita kwa mulungu wolingalira yekha. M'kusinthaku Kaini anakumbatira choopsa cha Mtengo wa batire lolimba, iye anauluka pamwamba mu ntchito zake zimene poyamba anakumana ndi malingaliro wosangalatsa a ufulu umene pakanthawi pang'ono afika pamalire ndipo nkugwa pansu.

M'chaputala chachisanu tinaona zina za zipatso za maganizo zimene zabwera kuchokera maubale a mabanja osweka. Mwachidule:

- Mowirikiza kufunafuna kuvomerezeka
- Kuziweruza wokha mokhwima kwambiri
- Kupanga maganizo opitirira m'lingo pa zinthu zoti iwo alibe ulamuliro – mwachinsazo, nthawi zambiri iwo ali olamulira kwambiri.

³⁰ Genesis 4:3

- Ali ndi vuto ndi maubale.³¹

Pamene Kaini anachoka pa dongosolo la Mulungu loikika kumupulumutsa iye, iye anakhala kutali ndi Mulungu; ubale wa banja lake unaswekerathu. Mtundau unabukitsa malawi a kusatetezeka kwake; Mzimu wa Mulungu sukanamukhazikanso bata ku mantha ake kapena kumuthandiza kutsutsa mabodza a Satana. Uchabechabe/kuperewera kunangowonjezera, ndipo malingaliro a manyazi anachuluka. Monga Satana, Kaini akanalimbana popanda phindu kubwezeretsa malingaliro a ubale wake wosweka ndi Mulungu. Ngakhale Iye akanayetsetsa molimbika bwanji sakanachotsa malingaliro akuya a kuperewera kwake mpakana iye abwerere kwa Mulungu, ufumu Wake, ndi dongosolo Lake.

Maganizo achipwirikiti a Kaini potsachedwapa aphulika. Zinachitika pa nthawi yoyikika ya nsembe, pamene Kaini ndi m'bale wake Abelo anabwera kupembedza Mulungu. Mulungu analandira nsembe ya Abele ndi moto wopsereza, koma anasiya ya Kaini osayikhudza. Ndi chomwecho basi chomwe chinam'kwiyitsa Kaini. Tchimo n'losathandiza kwambiri. Kaini sakutsatira malangizo ndipo kenako akukhumudwa monyansa pamene iye sizinamuyendere.

Taganizirani mwapita ku sitolo / msika kukapeza zophikira mkate. Inu mukufunsa ogulitsa m'sitolomo m'mene mungachitire, ndipo iye akukupatsani zofunikirazo kupita nazo ku nyumba. Zonse zikuyenda bwino ndithu kufikira mwanunkhiza fungo la chotupitsa ndipo mwaganiza kuti musayike ndikuti zikhala bwino popanda chotupitsacho. Mwaika mophikira m'uvuni pang'ono ndi pang'ono kenako mwachisoni kwambiri muli ndi mkate wosafufuma. Tsopano, zingakhale zomveka kuthamangira mwam'kwiyo kwa wogulitsa m'sitolo ndi kumukalipira chifukwa cholephera kuphika mkate? Sichoncho! Umu ndimene anachitira Kaini ndi Mulungu.

Kaini wafika pa mfundo yosabwerera. Atakumbatira ufumu wa Satana m'mene kufunikira kwake kumatsimikizika ndi khama lake ndi zochitika zake, luso lake kuti atsogoleredwe ndi kudzudzulidwa kumawonongeka mofulumira. Kaini akudziwa kuti wachita cholakwa, koma malingaliro a

³¹ Conway, 31

umunthu mosavuta angazinyenge, ndipo m'malo mogonjera mozichepesa kwa Mulungu iye akukwiya. Mokoma Mulungu akufuna kumuthandiza ndi kumukonza iye ndi kumulodzera iye ku mphatso yolonjzedwa ya Mwana Wake, koma Kaini sakutsatira chenjezo. Maganizo ake opanduka akula ndipo ufumu wa mdima pafupifupi wakwanitsa kupambana kuyesera mwa munthu.

Panopa mtima wa Kaini ukulamulidwa kwathuthu ndi maganizo a mphamvu amene Satana anamasula kumwamba. Iye akufuna kuvomerezeka kwa Mulungu koma m'zochitika zake zolakwika. Malingaliro akuperewera kwake achuluka kufika pa mfundo pamene iye anali wokonzeka kuphulika. Iye anagwidwa m'mkhalidwe lonyansa lolakalaka kuvomerezeka kuchokera ku mphamvu zapamwamba kukwaniritsa khumbo lake la kulandiridwa ndi kufunika, pamene pa nthawi yomweyo akufuna kunyalanyaza mfundo yoti chiri chonse ali nacho ncha Mulungu ndipo ayenera kuyamika mozichepetsa chifukwa cha chikondi Chake anapereka kudzera mu nkhosa. Mwamanyazi poyera patsogolo pa Abele, iye wayamba kukangana ndi iye. Abele akumudandaulira Kaini za njira yake ya chipembedzo ndipo akumulimbikitsa kuti abwerere ku dongosolo la Mulungu. Ichi ndichokhacho chimafunika kwa Kaini. Chinachake chinatseguka m'kati mwake. Malingaliro ake a kulepera anam'tsogolera ku mfundo imene tsopano iye samamasamalanso, ndipo pamene nthawiyi yafika, Satana amapatsidwa ufulu onse kulowa ndikumulamulira. Satana akumudzadza Kaini ndi m'kwiyo waukulu kwa m'bale wake, maubale apa banja ayiwalidwa, ndipo ufumu wa Satana tsopano ukudzionetsera mokwanira. Kumwamba konse kumaona pamene kuphedwa koyamba kunachitika, chiwonongeko choyamba cha ubale opatulika ndi wapatali. Choncho ndi chimene chimachitika pamene Malamulo a Mulungu aphwanyidwa! Kumwamba kunaonongeka, ndipo ngakhale Satana ndi angelo ake nayenera kukumana ndi kanthawi ka dzanzi pamene maonekedwe opanda moyo a Abele anasanduliza nthaka kufira ndi mwazi wake.

Satana akuthawamo m'chodabwitsachi, ndipo kuti asataye kapolo wake iye akukhazikitsa malingaliro akupalamula mwakuya kwambiri mwa Kaini kotero kuti iye sangakhulupirirensa kuti Mulungu angamukhululukire iye. Iyi ndiye misala ya Satana. Iye amatilonjeza ife ufulu ndi chimwemwe potsatira ntchito zake zopanduka ndipo pamene talakwa, ndi mau ake ofuula

kwa Mulungu ofuna kuti ife tiwonengeke. Pa nthawi yomweyo ndi mau ake otinong'oneza mu moyo wathu kuti ndife olakwa kwambiri ndi woipa kuti Mulungu angatilandirensa; ndi mau amene amakulitsa malingaliro athu ku mfundo yoti ife timafuna kufa. Nzomvetsa chisoni kuti m'ngelo ongola anasanduka chonchi kukhala woononga watsoka. Tsopano poti Kaini wakhozokera, iye alibe chitetezo cha moyo wake ndipo Satana akutsogolera iye kukulira, "Kulangidwa kwanga nkhwakukuru kosapiririka."³² Awa ndi mau omvetsa chisoni kwambiri osaneneka. Mulungu abwera kwa Kaini, osati kuti amutaye iye, koma kufunafuna kuti amubweze iye. Iye akumufunsa Kaini kuti m'bale wake anali kuti, osati kumutsutsa iye, koma kumupatsa Kaini mwai oti alape ndi kutembenukira kwa Mulungu. Mwachisoni Kaini akutulutsa mau achisoniwa, "Kulangidwa kwanga nkhwakukuru kosapiririka." Iye anakhulupirira mabodza a Satana m'malo mwa mau a Mulungu. Iye anafesa ndipo tsopano iye akolola.

M'Genesis 4:11-12, Mulungu akulengeza temberero. Mbali yotsirizira ya tembererolo, Mulungu akumuuzza Kaini kuti iye adzakhala wothawathawa ndi woyendayenda pa dziko lapansi. Mau akunenedwa kwa munthu amene ndiogwedera ndiozandima; zikupereka malingaliro a munthu opanda chiyembekezo ndi opanda tsogolo. Tembererori sanagwiritse Mulungu poyendetsa zina za m'mwamba, koma kuti chinali chibadidwe chokana ufumu wa banja la Mulungu, chibadidwe mu kukana maubale a pamtima. Moyo wake unazuzidwa chifukwa iye analengedwa chifukwa cha ubwenzi, koma mtima wake wasankha njira yosiyana – nthawi zonse kulakalaka chikondi komabe nthawi zonse kuipidwa ndi amene ali pafupi naye, kufunafuna kukhala nao pafupi komabe osalola anthu kubwera m'chipinda chachinsinsi cha mtima wake m'mene kulephera kwake kukhala, kufana kukhala ndi abwenzi koma nthawi zonse kuchenjera ndi opikisana ndi luso lake. Pano pagona mwambi oti: "Kulibe mpumulo kwa munthu woipa."³³

Baibulo limatiuza kuti Kaini anaturuka pamaso pa Yehova.³⁴ Iye tsopano anakhala opanda malingaliro oti Mulungu ali pafupi ndi iye. Pokhulupirira kuti tchimo lake lamutsekera kwa Mulungu, kwenikweni iye anatekera

³² Genesis 4:13

³³ Yesaya 57:20

³⁴ Genesis 4:16

Mulungu kuchokera kwa iye mwini. Tsopano ndikufuna kwakukulu kuposa poyamba kuvomerezeka ndi kufunika, anayamba kumanga mizinda. Iye ankasonkhanisa anthu kumuzungulira ndikukhala m'tsogoleri wao. Iye ankamanga nyumba zazikuluzikulu ndikupeza kufunikira kwake kuchokera ku zinthu anakwaniritsa. Iye anadzidzinga ndi zintchito za manja ake kuzitsekera kuchokera kukutsitsimuka, ngakhale akanayetsetsa akanathera, umboni wa mau a Mulungu. Iye anali wotanganidwa kwambiri kufika pa mlingo oti analibe nthawi yozifunsa za khalidwe la moyo wake.

Ndipo choncho Kaini anali njira yokhazikitsira ufumu wa Satana pa dziko lapansi. Kudzera mwa iye mtundu wa anthu unakhazikika umene unaonetsera zidzindiro zonse za kusatetezeka ndi kulephera. Iwo anali ofunafuna mphamvu ndi udindo, kukhazikitsa mzimu wolamulira umene unali nsanje ndi wina aliyense otsutana nawo, mukuthamangitsana kosalekeza kufuna kudziwika kopanda Mulungu amene analenga kumwamba ndi dziko lapansi. Ngati Satana angaasunge anthu kufunafuna mtengo / phindu mwa iwo okha m'malo mwa m'manja a ubale waukulu ndi umunthu wa Mulungu, atha kulamulira iwo. Ndipo iye wachita. Kuchokera ku nthawi ya mibadwo yakale Satana wagwira gulu la anthu pansi pa ulamuliro wake, kuwamanga iwo mukulephera, kusatetezeka kwa moyo kwa iye mwini ndi kufuna kulamulira dziko.

Taphunzira mtima wa Babulo, mtima wozunzika ofuna kudziwika ndi mtengo ndi zimene umachita, kufuna kuvomerezeka chifukwa cha mantha ake, ndikuyesa kupezerera zochitika kuti usawopsezedwe. M'chaputala chinachi tiona zotsatira zochitika za mtimau kuonekera kudzera mu mbiri ya anthu.

Gawo Lachiwiri. Tsogolo Limodzi

-Kudziwika Kubwezeretsedwa

10. Kudula Nsinga za Mtengo Wa Batire Lolimba

Panali ndithu nthawi ya chete atakumbatirana. Maganizo akuthamanga mwakuya, koma Iwo awiri anadziwa kuti nthawi yakwana. Kuchokera masiku a muyaya Atate ndi Mwana nthawi zonse anali limodzi awiri, koma tsopano posachedwapa asiyana. Mwana wa Mulungu tsopano ayamba utumiki wobwezeretsa ana amuna ndi akazi a anthu. Awiri Atate ndi Mwana akumvetsa kuopsa ndi mtengo okhuzidwa, koma chikondi chikuwatsogolera iwo kutero.

Kwa kathawi pang'ono, Atate ndi Mwana akuyang'ana mtsogolo ndi maso a uneneri akuona utumiki ukutambasuka. Kunyozedwa, kukanidwa, kudedwa, kulavulidwa, kumenyedwa, kududidwa ndi misomali sizinafanane kuyerekeza ndi nthawi yovuta pamene kumwamba kunali chete ndi kuona kusiyana kwa Atate ndi Mwana. Mwana anaona zaka za kupalamula, kuvutika, kupanduka ndi kulephera koikidwa pa Iye ndipo akuyang'ana kudziona Iye akugwedezeke ngati tsamba, kung'ambidwa ndi malingaliro oti nkhope ya Atate yibisika chifukwa cha tchimo. Atate ali ndi Mwana Wake

m'mdima koma ndi Mwana amene ali ndi malingaliro oti amusiya m'mavuto a imfa.³⁵

Kukumbatirana kulimbika – nchifukwa chani Atate akumupereka Iye ku tsogololi? Pa mlingo wakuya Iwo awiri akulimbana ndi kuthekera kwa kulephera ndi kutayika mpaka m'yaya ku mphamvu ya tchimo. Mwana wa Mulungu atenga khalidwe la munthu pa Iye kupereka danga la mwai kwa mdani Wake, Satana, kuti amupitirire mphamvu Iye. Panalibe kutsimikizira kwa kupambana. Chifukwa ninji Iwo akuputa chiopsezo choopsachi? Nchifukwa chanji akutenga dongosolo lotenga mpweyali? Komabe chikondi chopanda malire chakuya (Agape) chikuwakakamizabe.

Nthawi ya chete ija imene inaoneka ngati m'yaya kenako inafika kumapeto; Iwo awiri anagwirizana kuchita dongosolo lija. Mwana wa Mulungu mphepete mwa kumwamba, akuyang'ana komaliza nkhope yokonda ya Atate Ake ndipo kenako Iye wapita.

M'chaputala cha chisanu ndi chimodzi tinaona m'ndanda wautali wa zobechera zomwe Mulungu anafuna kuchita ngati Iye amafuna kupulumutsa ana Ake amuna ndi akazi pa dziko. M'chaputala cha chisanu ndi chinai tinaona kukhazikika kwa ufumu wa Satana m'mtima wa munthu ndi m'mene Satana amatilamulirira kudzera m'malingaliro athu a kulephera. Iye ayenera kutirumikizanso ku malingaliro athu a kudziwika monga ana a Mulungu ndi kugonjetsa kudziwika konyenga kumene kunakhazikika m'Mtengo wa batire lolimba.

Malingaliro akuya a mantha anayenera kumugwira Satana pamene anaona angelo akuyimba nyimbo ya chimwemwe kwa abusa kuti Mesiya/Mpulumutsi wabwera. Nyenyezi yonyezimira imene inatsogolera anzeru akum'mawa ku khola la ng'mbe kunaonjezera kusatonthozeka. Mutha kuganizira m'mene iye amayang'anira pa khanda lolemekezekalo iye anadziwa kuti wabwera kuzamenya nk'hondo. Iye sanatha kuononga mtendere wa chete umene unakhala pa mwana, zimene iye nthawi zonse amachita pa mwana wina aliyense mumbuyomo. Zinali zosamvetsetseka;

³⁵ Ahebrei 2:9

mwana obadwa m'thupi ndi mwazi koma mtendere wakuya unali pa mwana moti iye akulephererathu kuutsokoneza. Satana anadziwa kuti ali m'mavuto.

Mzimu ovutika unakhala m'mtima wa Herodi ndipo tikupatsidwa dzenera kuona chipwirikiti chimene chimayambitsa mzimu wakuda wa dziko. Malingaliro akuya osatetezeka amene analamulira Herodi anamupanga iye mosavuta kukhala nyambo ya 'mantha ndi zochitika za' Satana kulimbana ndi ufumu wa kumwamba. Iye anatha kumutengera kunja Iye kukangana kwenikweni kusanayambe. Koma chidaliro cha mtendere cha khanda Mfumu sikunatsokonekere. Kumwamba kunakonzera Iye njira yopulumukira kuti Iye abvumbulutse choonadi cha Atate Ake, ndi kubvumbula olamulira wa mdima, ndipo m'thupi la munthu kudula nsinga za kusatetezeka kumene kunapanga mtundu wa munthu woonongeka m'ukapolo. Mwachidule moyo wa Yesu ungangofotokozedwe m'mauwa:

Ndipo wondituma Ine ali ndi Ine; sanandisiya Ine pa ndekha;
cifukwa ndicita Ine zimene zimkondweretsa Iye nthawi zonse.
Yohane 8:29

Sizinatanthauze kathu Satana akanachitanji, iye sakanadula malingaliro aja a ulemu ndi kudalira. Kristu anakakamira pa Umwana Wake ndi kupirira kumene ngakale kalonga wa mdima anachita mantha. Satana anayenera kuti anali ndi m'kwiyo pakupanda pake kwa khama lake kumuchimwitsa Kristu. Tsopanono, winano amene atha kukana Satana. Patapita zaka zikwi zinayi ndi kupambana munthu wina aliyense, Satana akumenya khoma la mwala la moyo wa munthu amene akudalira mu Umwana Wake kwa Mulungu. Umwana unali mfungulo ku chigonjetso; Umwana unali mpanda wotsimikizika kulimbana ndi mtsinje uja wa uchabechabe / kulephera kumene kunamiza mtundu wa anthu, ndipo choncho Umwana uyenera kukhala mfuno yapakatikati pa mkangano pakati pa Kristu ndi omuphayo.

Tauni ya Nazareti inali yodzadza ndi zochitika zachisangalalo. Uthenga wa Mubatizi unafalikira mofulumira. Kalambula bwalo wa Mesiya anabwera, ndipo pamene uthenga unafika ku shopu ya olapa matabwa onyozeka, Yesu anadziwa kuti nthawi yolemekeza Atate Ake yafika. Iye akusiya pansi zida, akukumbatira mai ake ndikupita ku Yorodano.

Yesu akudalira Umwana Wake, koma mkangano ukubwera m'chipululu kumuyesa Iye kuposa munthu wina aliyense anayesedwa m'mbuyo. Zipata za matsoka a anthu zimasulidwa pa Iye ngati kuphulika kwa damu. Yesu ayenera kukumana ndi mphamvu zonse za kulephera kwa anthu ndi kukhalabe okhazikika. Ngati Iye angayime kolimba nji, ndiyeno kwa nthawi yoyamba winawake angathe kudula nsinga za Mtengo wa batire lolimba. Zokunkha za chigonjetsochi zidzakhala cholowa cha iwo amene akhulupirira Iye.

Nkhondo m'chipululu anali maziko a ntchito yapa mtanda. Ndi ntchito yanji kupereka chikhululukiro ngati moyo wa munthu sukudula nsinga za kuperewera kwake? Ndi phindu lanji kubvumbulutso lokongola la chikondi ngati palibe mwamuna, mkazi kapena mwana angakhale ndi mphamvu zokumbatira mphatso ija – palibe! Kulephera ndi kuperewera kwa Mtengo wa batire lolimba kuyenera kugonjetsedwe koyamba ndipo zokunkha za chigonjetso kuikidwa m'manja a mtundu wa anthu kuti onse angapatsidwe mphamvu kuti akumbatire mphatso yotsayerekezeke ya mtanda ndi kukhulupirira moonadi kuti Mulungu amakonda ndi kukhululukira iwo.

Mulungu akudziwa chimene chikubwera ndipo Iye azalimbikitsa dzanja la Mwana Wake ku nkhondo, posaonetsera mphamvu, popanda kugwiritsa asirikali a nkhondo ndi zida. Palibe mwa izi zomwe zingakwanire kukumana ndi mdani obwerayo. Mulungu akupereka chida Chake chabwino kwambiri – mphamvu zochokera ku ubale wa wina ndi m'nzake. Pamene Yesu akutuluka m'madzi, ndipo nkhunda ikutsika, kumwamba kukutseguka ndipo Yesu akumva mawu a Atate Ake, **“Uyu ndiye Mwana wanga wokondewda, mwa Iyeyu ndikondwera.”** Mauwa ndi lupanga lakuthwa kwambiri limene akanatha kumupasa Mwana Wake kuchita nalo nkhondo. Otetezeka m'MAU a Atate Ake, Iye apanga nkhondo ndi mdani onyenga ndi kudula maunyolo a tchimo m'malo mwathu amene ife sitikanatha kudula.

Tanthauzo la mauwa limapita mwakuya kwambiri kuposa momwe ambiri angaganizire. Mfundo yoti Mulungu akulandira chiwalo cha mtundu wa anthu kukupereka chiyembekezo chosaneneka kwa ife tonse. Kudzera mwa Yesu, Mulungu akufikira wina aliyense wa ife ndi kutiuzana ife kuti ife ndife ana Ake okondedwa. Ngati ife tiri ndi chiyembekezo cholandira mphatso ya

mtanda ife tiyenera choyamba kumva mau aja a mtengo wapatali, “Iwe ndiwe mwana wanga wokondedwa mwa iwe ndikondwera.” Nkosatheka kulandira mphatso kuchokera kwa mdani popanda kudabwa ngati sinapakidwe ndi poizoni kapena kampeni kumphasa, koma mphatso yochokera ku chiwalo cha banja lokondedwa ingalandiridwe m’mene iriri – mphatso, yoyera ndipo yosavuta. Palibe njira yoyandikira mtanda kusiyana ndi kudusa ulalo wa chikhulupiriro cholimba cha umwana wathu kwa Mulungu amuna kapena akazi. Njira ina iri yonse ititsogolera mwamalamulo kapena chilolezo ku tchimo.

Mau aja ochokera kumwamba ayenera kuti anam’kwiitsa kwambiri Satana. Chikumbutso cha chinachake chimene iye anali koma tsopano tsali – mwana! Chinali chikumbutso cha kuperewera kwake ndi utsiru. Komabe kunyada sikumafa mosavuta, kotero Satana akumasula mayetsero ake onyoza pa Yesu m’chipululu.

Mbiri ya m’Baibulo ikunena kuti Yesu “anakhala m’cipululu masiku makumi anai woyesedwa ndi Satana.”³⁶ Ine ndikuganiza kuti anthu ambiri angapeze mphindi khumi zonse zoyesedwa nkugonjetsedwa nanga bwanji masiku makumi anai! Satana anali ndi zaka zikwi zinai zokonzekera kuyetsa kuti apambane ndipo inu mukhoza kutsimikizika kuti Yesu anapangidwa chidzikiro cha chida chiri chonse chaku gehena. Ndani angamvetsetse kuya kwa nkhoodoyi? Chirengedwe chonse chinagwira mpweya wao umodzi pamene Satana amaponya chida ndi chida pa Mwana wa Mulungu. Pamene ife, tinali mtulo tofa nato, tingatsutse kuima kwa ngwazi kumene anachita Yesu kutimasula ife. Ngati Yesu akanalephera pano ife tonse tikanasweka ndi maunyolo a kulephera kwathu. Yesu anali m’modzi yekha chiyembekezo chathu kupyoza mdima. Ine ndikafika pa mfundo ngati imeneyi ndipo ine ndimangoyenera kuima ndikuganizira za Iye. Ine ndinganene chani? Mtima wanga umatsefukira ndi chimwemwe chachiyamikiro pa khama lotsimikizika losalekeza la Karonga wamphamvu kutithandiza ife m’makhalidwe amavuto. Ziri monga bambo kapena mai amene athamangira m’nyumba yoyaka moto kupulumutsa mwana wake. Iye pafupifupi anali osweka m’maganizo ndi Satana, koma Iye sanataye Umwana Wake. Munthuyu akupangitsa chinachake chakuya mkati mwanga kufuula – “Ine

³⁶ Marko 1:13

ndiyenera kukhala chinachake chofunika. Palibe wina wake akanachita ichi kupatula iwo amasamaliradi.” Ine ndikukuuzani chikondichi chikundikokera m’njira ndikupeza ndiyotamandika. Ine ndimam’kana Iye, koma ndikuthokoza Mulungu Iye ndiwotsimikizika kusiyana ndi ine!

Pamene Yesu anali pa nthawi yotsatetezeka – kutopa, njala, ndipo yekhayekha, zinthu zonse zimene zimamupanga munthu kulorera – Satana akubwera pa nkhani yofunikira kwambiri. “Ngati Iwe ndiwe Mwana wa Mulungu, uza miyalayi yisanduke mkate.”³⁷ Yeso likanakhalanso lotani kupatula za Umwana? Yesu sanauzidwe kuti akhala m’chipululu Iye akhalamo nthawi yayitali bwanji, mbiri sikutiuzwa kuti Iye anauzidwa kuti m’masiku makumi anai mayeso onse akhala atatha. Yesu anali kunjako, ndipo akhungubwi sanabwere kuzamudyetsa Iye, popanda mana kugwa kuchokera kumwamba. Mwina Iye analakwitsa za mau ochokera kumwamba? “Atate ako sangafune Iwe kukhalabe m’khalidweri. Panga chinachake za ichi,” Satana akumunong’oneza.

Satana anagwiritsa ntchito chilakolako kuyesa kupwanya chikhulupiriro cha Yesu m’mau a Atate Ake. Masiku makumi anai m’mbuyomu, Mulungu anati “Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa, mwa Iyeyu ndikondwera.” Ngati Yesu asandusa miyala kukhala mkate ndiyeno Iye akayika mau a Mulungu, ndipo kukayikako kukwanira kusokoneza kudziwika Kwake. Kupitirira apa Yesu akufunsidwa kuchita chinachake kutsimikizira kudziwika Kwake. Kufunsa Yesu kusandusa miyala kukhala mkate kutsimikizira kuti Iye ndani linali khomo lachindunji m’ufumu wa Satana – kudziwika chifukwa cha ntchito ndi kupambana.

Ndiangati a ife amene sitinagweremo m’msapha otsimikizira kufunika kwathu chifukwa cha zomwe tapeza? Kutengeka ndikuonetsa kuti inu muli nazo zokutengerani kufika pamwamba, kunyalanyaza kugona ndi kupuma ndiponso koposazonse nthawi ya pemphero ndi kuphunzira Baibulo, kukhala ku ntchito mpaka nthawi yotaika ndi kusowa nthawi yopambana ya m’banja – kungofuna kukwera pa ntchito ndi bonasi. Chifukwa chani timazivutisa? M’nthawi zambiri timayankha ku chobechera: “Ngati iwe

³⁷ Mateyu 4:3

ndiwe mwana, wamwamuna kapena mkazi, wa Mulungu, panga chinachake chachikulu chotsimikizira.”

M'mapeza izi pamene mwadzuka m'mawa ndipo inu mukufuna kuti mukhale ndi nthawi yina yosinkhasinkha ndi kukhala ndi Mulungu kuti mutu wanu wagoyamba kudzadza ndi zinthu zonse zofunika kuchita tsikulo, mpaka inu simungatengenso zina ndipo mungololera kukhala ndi mphindi zisanu zokha za pemphero ndipo kenako mukupita m'tsikulo. Ichi chimakuchitikirani inu? Nchifukwa chani? Ngati inu mwafika kumapeto a tsikulo ndi kupeza kuti inu simunakwanitse zambiri, m'makhutisidwabe ndi kukondwera, kapena m'makhumudwa ndikukhala ndi nkhawa? Inu m'makwiya “potaya nthawi” pa kama mutadwala, pamene mukanakhala mukupungula “zochita “pa m'ndanda wa zochitika? Zinthu zonsezi zikulozera ku mfundo yakuti popanda kupatulapo tonsefe timagwa m'mayesero a Satana kuti titsimikizire kudziwika kwathu ndi kufunikira kwathu ndi zimene tachita. Chifukwa cha mfundo yoti mwakuya pansi mkati ife tanyamula kusatetezeka kumene kunapatsidwa kwa ife kuchokera kwa Adamu ndi Eva, ife ndife mipherezero yofuna kupanga masamba a nkuyu auzimu ndi maganizo kuti tiziphimbe tokha. Munthu osatetezeka nthawi zonse amayankha ku chobechera cha kudziwika kwao, pamene munthu otetezeka savutika nazo. Zikundikumbutsa ine nthawi imene ndimayenda ndi m'nzanga amene anali ndi galu wamphamvu wamkulu. Timadusa pa malo a m'nasi amene anali ndi ka galu kakang'ono. Ka galu kakang'ono kamalira ndi kuuwa kuzungulirazungulira kuti kadzutse chidwi cha galu wamkulu. Galu wamkulu sanatembenuze mutu wake kuti ayang'ane ka galu kakang'ono. Ndimamverera ngati ka galu kakang'ono kamanena kuti, “Bwera kuno Galu wamkulu, ine ndirimbana nawe ndipo nditsimikizira mbuyanga kuti ndithu ndigonjetsa galu wamkulu ngati iwe,” koma galu wamkulu modalira m'mene iye aliri ndipo sanayankhe ku chobecheracho. Kukanaonjezera chani kukufunikira kwake?

Ndi chifukwachi Yesu anayenera kulowa m'chipululu cha kuyesedwa. Banja la munthu limafuna munthu amene akanawonetsa kuti iye akukhulupirira kuti ndi mwana wa Mulungu pa chifukwa chokha choti Mulungu ananena, m'malo modzera kutsimikizira ichi m'zomwe wachita iye. Dziko likufunika Davide kulimbana ndi Goliyati olephera wooneka ngali osagonjetseka amene amatimanga ife m'machimo athu ndikutipanga akapolo a

m'dierekezi. Nzoonadi nkhani ya mayesero a Kristu m'chipululu ali ndi zofanana zambiri ndi nkhani ya Davide ndi Goliyati:

1. Satana, monga pokhala m'mzimu, anali ndi mwai waukulu pa Yesu amene anavala khalidwe la umunthu. 1 Samueli 17:33
2. Yesu amayimira mtundu wonse wa munthu ndipo chigonjetso cha Kristu chimatanthauza ufulu kwa ife, monganso Satana amayimira mphamvu zoipa zonse ndipo chigonjetso cha iye zimatanthauza kuti ife nthawi zonse tizakhala akapolo a mphamvu yaku mdima. 1 Samueli 17:9
3. Yesu anali mcipululu masiku makumi anai kukumana ndi kunyoza ndi mayesero a Satana monganso Goliyati akutonza Israyeli kwa masiku makumi anai. 1 Samueli 17:16
4. Satana / Goliyati anabwera m'mphamvu zake koma Yesu / Davide anabwera m'dzina la Ambuye kubvumbulutsa Atate Ake ndi kubvumbula iye amene ananyoza asirikali a Mulungu wamoyo. 1 Samueli 17:45
5. Zida zimene Yesu anagwiritsa ntchito zimaoneka zofooka ndi m'yezo wa dziko – Iye anadalira m'mau a Mulungu ndipo Iye anagwiritsa ntchito mauwo mogometsa pobvumbulutsa maganizo a Satana.

Kufanana nkofunika kwambiri. Ine sindingathe kuthandiza koma kudziika ndekha monga m'modzi wa asirikaliwo a Israyeli ayima m'mphepete mwa phiri, kumvutsera Goliyati akunyoza Mulungu wanga, chipembedzo changa, ndiponso ine pandekha. “Mulungu wako ali kuti? Osamenyana ndi ine bwanji ngati Iye uli ndi mphamvu kwambiri? Inu ndinu ofoka ndi opanda ntchito ndiochititsa manyazi kwa Mulungu wanu?” Kumvetsera ku m'nyozo wotere kwa masiku makumi anai kukanapereka nkhwana. Tagoonani thunthu lake! Zida zake zikunyezimira m'kuwala kwa dzuwa pamene mau ake achirombo onyoza akumveka m'chigwa. Zochitika zikuoneka zopanda chiyembekedzo, ndipo pakumveka mtima obwerera ku ukapolo. Kodi zikusiyana ndi masiku ano? Ife tiri ndi kutonza kwa Satana za kulephera kwathu ndi kufooka kwathu. Mayesero ake akuoneka a mphamvu ndi anthumanzi, ndipo ife timagwa nthawi ndi nthawi, ndipo tiri ndi maganizo akugwa obwerera ku ukapolo. Ngakhalebe palinso iwo amene akulalikira kuti ukapolo wathu sungatheke kugonjetsedwa ndikuti tchimo nthawi zonse

lizatigongetsa ife; chisoni chotere kugonjera kuukapolo wa tchimo. Mwana wa Davide ali m' msasa wathu, ndipo Iye watimasula ife ku maunyolo a m' dierekezi. Chigonjetso Chake m' chipululu cha mayesero ndichigonjetso cha babja lonse la munthu. Mungathe kusankha kuganiza kuti inu muyenera kukumana ndi Goliyati wanu, kapena inu mungathe kuona mwamantha m' mphepete mwa phiri pamene Yesu akuteteza mutu wa yesero lanu. Ngati inu mungakhulupirire kuti inu muli ndi chigonjetso kale chifukwa cha Yesu, m' malo moyembekezera Iye kuti azakupulumutsani inu ndiyeno inu mwapeza chikhulupiriro chenicheni.

Ine ndiri wosangalala kwambiri kuti Mwana wa Davide wandimasula ku mphamvu ya kulephera. Iye wachotsa mtima wanga opanduka ndi onyada. Iye waika mapazi anga pa mwala okhala odziwika monga mwana wa Mulungu. Iye payekha wakumana ndi makayiko m' malo mwanga ndipo anagonjetsa iwo ndi chikhulupiriro m' Mau a Atate athu. Imbani ndikukondwera ndi ine inu ana amuna ndi akazi a Mulungu. Yesu anaphwanya maunyolo a Mtengo wa batire lolimba kwambiri ndikutipanga ife ovomerezeka mwa Okondedwa.

11. Kutsegula Zipata Za Kumwamba

Malazi a kuwala kupyola m’mdima kusonyeza kuti mbandakucha wayandikira. Kumasonyezanso nthawi ya ntchito iyambe. Kugunda kukufulumira, kupuma mpweya kukufupikira, pamene kukonzekera ulendo kukuchitika. Pamene akutuluka m’mbandakucha, malingaliro a Abrahamu akusefukira ndi zikumbukiro. Akukumbukira akumugwira Isake m’nthawi yake yoyamba ndi malingaliro a chimwemwe chachikulu chimene chinatuluka patapita nthawi yayitali yodikirira. Chikumbukiro cha mwana wang’ono akulumphalumphu pa kama wa Bambo ndi kukhala pafupi momasuka pamene akumvera mwachidwi nkhani za Adamu ndi Eva, Nowa ndi zina zambiri, zinali zolemetsa kwambiri pa mapewa ake pamene akuganizira ntchito iri patsogolo pake, pamene Mulungu anati:

“Ndipo anati, Tengatu mwana wako, wamwamuna wayekhayo, Isake, amene ukondana naye, numuke ku dziko la Moriya; numpereke iye kumeneko nsembe yopsereza pa limodzi la mapiri lomwe ndidzakuuza iwe.” Genesis 22:2

Mulungu ananena ndipo Abrahamu akusonkhanisa mphamvu zake zonse kumvera lamulo. Palibe kufotokozeru, palibe chifukwa choperekedwa, lamulo lokha basi. Zaka zambiri zimene Abrahamu anayenda ndi Mulungu, iye anaphunzira kusakana malamulo Ake. Iye anafika pokhulupirira kuti Mulungu amadziwa bwino kwambiri ndipo Yake yinali njira yokhayo yoitsatira. Koma njira inali yovuta, yovuta kuyiganizira!

Ndani angathe kumvetsetsa kulimbana kumachitika m'malingaliro a Abrahamu? Mokondwera iye akanasankha kuzipereka nsembe m'malo mwa mwana wake. Palibe chimene akanalephera kuchita kupulumutsa mwana wake ku tsoka lake. Abrahamu akupuma zolimba pamene iye akulimbana kubisa ululu wake kwa Isake. Ichi chiyenera kukhala chilubwelubwe chimene posachedwa chichoka. Zenizeni zikuchitika pamene Isake akufunsa, "Atate, nkhuni tatenga ndi moto, koma nsembe iri kuti?" Muvi ukulasa mtima wa Abrahamu. Iye ayankha bwanji? Pemphero lachangu likukwera kwa Mulungu lopempha nzeru ndipo kenako Abrahamu akuyankha, "Mulungu adzapereka nsembe mwana wanga."³⁸

Pa mwamba pa phiri, Abrahamu mopwetekedwa akuulula kwa Isake kumvetsera kwake ku lamulo la Mulungu. Isake ndi wachinyamata ndipo mosavuta atha kuwapitirira mphamvu atate ake ndi kuthawa, koma Isake anaphunzira kumvera ndi kulolera zilakolako zake ku nzeru za atate ake. Kumwamba konse kukuyang'ana pamene Abrahamu akukonzetsera mwana wake, mwana wake wapatali ku nthawi yomaliza. Kulingalira kwa munthu kukumasula zida za mikangano kulimbana ndi chikhulupiriro, koma Abrahamu kuima monga mtengo wautali wa mkungudza ku mphepo za mkuntho, akuwerama koma sakupereka chitsimikizo chake kukwaniritsa kumvetsetsa kwake kupempho linaperekedwa kwa iye.³⁹

Chinachirichonse nchokonzeka ndipo Abrahamu akuyang'ana pansu pa mwana wake. Ululu kung'amba kupyola mtima wake ndipo mphamvu zake zayamba kuperevera, koma iye ukugwiritsitsabe. Akupereka pemphero iye akukonza malingaliro ake kuti abaye mpeni umene umalize moyo wa mwana wake wamtengo wapatali kwambiri.

Pa nthawiyi mau akumveka, "Abrahamu! Usaike dzanja lako pa mwana, chifukwa tsopano ndidziwa kuti iwe umaopa Mulungu."

Pamene ine ndikusinkhasinkha za nkhanayi, ine sindingathandize koma kuziika ndekha m'malo mwa Abrahamu ndi mwana wanga m'malo mwa Isake. Ine ndikumvetsa m'mene iye amamvera kupsinjika, koma chithunzi

³⁸ Genesis 22:7, 8

³⁹ Onani buku *la Agape* chaputala 24 – Abrahamu ndi zonyansa zopangitsa bwinja pa fatheroflove.info

pomwepo chikuimitsidwa. Chinachake mkati mwakuya chikutuluka ndipo chikuletsa kuti chithunzichi chimalizike. Mwamaganizo m'malingaliro anga sangathe kufikapo pa chochitika monga ichi.

Kumvetsa kuopsya ndi nsembe ya Yesu pa mtanda ife tifune chithunzithunzi chakuya cha ubale pakati pa Atate ndi Mwana. Chenicheni cha ufumu Wao chikufanizidwa pakati Pao; ngale ya njira Yao ku moyo yikubvulitsidwa m'chikondi chimene Iwo ali nacho kwa wina ndi m'nzake. Ngati ife sitingaphatikizepo mfundozi ya ubale ku mtanda ndiye kuti taphonya mfundo yofunikira kwambiri.

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yensewakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha. Yohane 3:16

Kusiyana pa ubale wakuya kwambiri ndi chinthu chopweteka kwambiri chimene munthu angakumane nacho. Ganizo losiyana ndi amene ife timaakonda ndi mantha amene amabisika m'kati mwa mtima m'moyo wa munthu aliyense. Ine ndimazona pamene ndachokapo kusiyana ndi banja langa kwa sabata imodzi yokha kukalalikira, mtima wanga umalalakala ku nyumba kukhala ndi amene ndimaakonda. Palibe chinachiri chonse pa dziko lapansi chimene ndingasinthanitse ndi ubale wa banja langa. Ngakhale ganizo lonkhalo limandiipira, komabe pamene ife tikuona m'mtima wa Mulungu, monga zabvumbulitsidwira m'Baibulo, ife tikupeza kuti Mulungu Atate wathu ndi Mwana Wake anali olola kusiyana ubale wao wa wina ndi m'nzake, kungoti inu ndi ine tithe kupyola zipata za kumwamba ndi kulumikizikanso ndi Mlengi wathu ndi Mwana wake.

Winawake angayankhe, "Inde, koma Yesu amadziwa kuti Iye aukanso ndi kulumikizanso ndi Atate ake, choncho sizinali zoipa ndithu." Ngati mwalola maganizowa, ndiyeno ine ndikuti inu mutamufunsa Yesu m'mene amamvera Iye pamene anafuula, "Mulungu wanga, Mulungu wanga mwandisiilanji ine?" Pamene kupalamula kopanduka kwa dziko lapansi kunali pa Iye ndi chikondi cha Atate ake chinaphimbidwa ndi kusakhulupirira kwa umunthu wathu m'chikhululukiro cha Mulungu kwa machimo athu, Yesu anafunafuna m'mdima kuti apeze nkhope ya chikondi imene nthawi zonse inali chimwemwe Chake kupyolera m'yaya, koma

tchimo linabisa nkhope ya Atate Ake kotero kuti Iye amamva kuti wasiyana kotheratu ndi Iye. Chiyembekezo Chake chinamedwa, imfa yokhayo ndiimene yimamuyembekezera Iye; Iye analingalira kuti Iye wachotsedwa kotheratu kwa Iye amene amam'konda choncho analira mofuula, "Mulungu wanga, Mulungu wanga mwandisiyiranji ine?" Tangoganizani kwa phindi; nzochitsa mantha!

Mulungu sanamusiye Mwana Wake, koma kulemera kwa machimo athu pa Yesu anam'pangitsa Iye amve zimene ochima amamva chifukwa cha kupalamula. M'chaputala cha chisanu ndi chinai tinawerenga za Kaini amene analira mofuula, "Kulangidwa kwanga nkwakukuru kosapiririka." Kristu ananyamula ichi pa mtanda m'malo mwathu. Machimo athu amatipanga ife timve kuti Mulungu ngotsutsana nafe ndipo akulakalaka ndithu kutipha chifukwa cha machimo athu, koma Mulungu anayamikira chikondi chake kwa ife ndi kulola Mwana Wake kupyola muzochitikazi m'malo mwathu kuti ife tikakhulupirire kuti tingakhululukidwe.

Zonsezi zingabweretse funso, kodi Mulungu ngofunitsitsa bwanji kuphwasula zotchinga pakati pa Iye ndi ife? M'nkhani ya Abrahamu ndi Isake tikuona chithunzi cha Mulungu ndi Mwana Wake. Ndichikhalidwe chathu, monganso ndi Abrahamu, kuganiza kuti Mulungu amafuna Abrahamu aphe mwana wake. Mulungu anamuuza Abrahamu apereke mwana wake, ndipo Abrahamu anamva ichi kutanthauza kuti amuphe iye chifukwa ichi chimaonetsera kudzikira kwathu za chilungamo cha tchimo. Pakutitu Mulungu anamuletsa Abrahamu zikusonyeza kuti ichi sichinali chilakolako Chake, komabe m'ndondomekoyi Abrahamu akuulula chikhulupiriro chakuti anali olola kupereka ziyembekezo zonse zomusangalatsa kwa Mulungu. Pamene Mulungu anapereka nkhoa kwa Abrahamu ngati cholowa m'malo, ife tikuona kuti Mulungu akupereka cholowa m'malo mwa kudzikira kwa munthu za chilungamo. Mulungu analola Mwana Wake kulekanitsidwa kuchokera kwa Iye m'malo moti tikhulupirire kuti ife takhululukidwa ku machimo athu.

M'chivomerezi ndi mdima wa tsiku loopsa lija pamene chikondi chachikulu chomwe nthawi zonse chinakhalako chinalekanitsidwa chifukwa cha machimo athu, Ine ndikumva kulira kwa Atate, "Mwana wanga, Mwana wanga, Ine ndikupereka Iwe bwanji? Ine ndikulola kuti upite bwanji?" Iri

ndi Gehena pom'pano. Awiriwa Atate ndi Mwana anakumana ndi Gehena mwakulekanitsidwa kwa ubale wao m'malo mwathu. Iwo analipira dipo limene ife tinalimvetseta liyenera kulipiridwa. Nanga chingakhalenso chani chenicheni cha Gehena koma kusiyana kwenikweni kuimira kwa ufumu wa Mulungu – kukonda, ubale weniweni?

Choncho izi zikutanthauza chani kwa ife? Zikutanthauza kuti Mwana wa Mulungu analawa kuopsa kwa kulekanitsidwa kuchokera ku chikondi cha umulungu m'malo mwathu, choncho ife kuti tisayenera kukumana nacho. “Imfawe, cigonjetso cako ciri kuti? Imfawe, mbola yako iri kuti?”⁴⁰ Tsopano palibe chingatirekanitse ife kuchokera ku chikondi cha Mulungu chifukwa cha zimene Yesu ndi Atate Ake atichitira ife. Nsembe ndi zopereka sidzinafunike ndi Mulungu, koma m'malo moti ife tidziwe kuti titha kukhululukidwa Mulungu analipira dipo mtheradi.

Chipata cha kumwamba nchochinjika kwa ife chifukwa Mwana wa Mulungu anakumana ndi kulemera kopera kwa Gehena kutseka chipata chake. Ife sityeneranso kulowa ndi kukumana ndi kulira ndi kukuta mano, monga zidzachtikire kwa iwo amene akukana zimene Yesu watichitira ife ndipo azadzirekanitsa okha kwa m'yaya kuchokera ku chikondi cha umulungu.

Chobechera chimene chatsala kwa ife tsopano nchopanga ulendo m'malingaliro athu kuchokera ku makhalidwe amene ife timva uchabechabe, zamwano ndi kutsimikizika, (kusema kudziwika ndi zimene ife timachita), ndikubwerera ku gwero la moyo, kumene chikondi chikuyembekezera ife ndipo ife tikudziwa kuti ndife ana Ake okonedwa. Ngakhalebe Yesu watsegulira ife zipata za kumwamba, ife tipange ulendo kuchokera ku ufumu wa Mtengo wa batire lolimba kunka ku ufumu wa Mulungu, kuchokera ku kudziwika chifukwa cha zimene takwaniritsa kunka ku kudziwika chifukwa cha umwana wa ana amuna ndi akazi, kapena mwa mau ena, kuchokera ku chipulumutso cha ntchito kunka ku chipulumutso cha chikhulupiriro. Kotsalira kwa bukuli tidzipereka ku zobechera ndi mwai / phindu la ulendou.

⁴⁰ 1 Akorinto 15:55

Gawo La Chitatu-Ulendo Obwerera Ku Umwana

12. Moyo Oyendetsedwa Ndi Mtengo Wa Batire Lolimba

Mpweya wachiyembekezo ukudzadza m'chipinda. Ine ndakhala ndi ophunzira anzanga mu holo ndi kulakalaka kumva dzina lolidziwa. Ine ndinalimbikira kwambiri pa maphunziro anga chaka chimenecho ndipo pamene ndimaziuza ndekha kuti ziribe kanthu, ndi pamene m'kati mwanga mwakuya chilakolako chimakula.

Sukulu imapereka mphoto kwa ophunzira osiyanasiyana chifukwa cha zimene anakwaniritsa m'chakacho. M'nthawiyi, ine ndikusewera kasewero kakang'ono ka m'malingaliro. "Iwe walimbikira kwambiri chakachi, utha kulandira mphoto ikubwerayi.....iyayi, wina wake apambana....koma uli ndi mwai." Pamene nthawi ikubwera pamene dzina liziulutsidwa, mtima wanga ukugunda mothamanga poyembekezera ndipo kenako ndikumva dzina, siranga koma la m'modzi wa anzanga. Apa ndi pamene pakusangalalatsa. Kunja kwanga, ine ndikuombera manja anzanga pa kupambana kwao, koma m'kati mwanga nzosiyana: "Chifukwa chani wapambana? Ine ndinalimbikira kwambiri kuposa iye, ine sindikuhulupirira akumpatsa iye. Aa, ine ndikuganiza ndikudziwa chifukwa. Iye ndi wachibale ndi m'modzi wa aphunzitsi, ndipo ndichifukwa chake amusankha iye. Zotsatira nzachinyengo! Sizimene iwe ukudziwa,

ndiamene ukudziwa.” Nthawi yonse ndiombera manja, kumwetulira, ndi kuyesa kuoneka okhazikika. Mitambo ikuyamba kusonkhana ndipo maola ochepa akubwera ine ndikumva nkhwana ndiponso kukwiyo pang’ono. Ndi tiku lina chabe la moyo oyendetsedwa ndi mphamvu za Mtengo wa batire lolimba.

Sizitengeranso nthawi yayitali kuti mwana akawone kuti ngati akufuna kuwengeredwa ndi kuvomeredwa, choyamba ayenera kukhala pa gulu la anzake wofanana naye. Mwalandiridwa ku dziko la kufananitsa. Munagwapo m’msampha oti mwagulira mwana wanu mphatso yakubadwa ndipo m’bale wake osam’gulira? Nthawi zambiri pamakhala mavuto kwa amene sanaguliridwe akuyankhula mau. “Sichirungamo,” misonzi ndi kulira mofuula ndiponso kuvutitsa kwambiri. Ndiyeno pali mpikisano wa “Onani ine” ku malo osewera ku paki. Inu mukuona m’modzi wa ana pa chotsetsereka ndipo m’kumwetulira pamene iwo akutsetsereka pansi. Kumbuyo kwanu mukumva mau kuitana “Onani ine,” ndipo inu mukutembenuka kuti muone mwana wanu wina akuzunguzidwa pa lende. Inu m’kutembenuka ndi chidwi ku chinachake ndipo mwana wanu wazindikira ndipo akulira, “Onani ine” ndipo kenako m’kukhuzidwa ndi mau ambirimбири woti “Onani ine” monga m’mene mfuti ya zipolopolo zambiri imawomberera, aliyense “onani ine” akuonjezekera. Ndiyeno mwakhala pansi pa nkhomaliro ndipo pamene m’kungoyamba kudya, mukumva kamungoli kakang’ono kachikondi, “Iye watenga zambiri kuposa ine, Ine ndikufuna zambiri.” Ichi ndi chenicheni cha moyo woyendetsedwa ndi Mtengo wa batire lolimba. Pamene tikumakula timayetsera kukhala oyengeka kwambiri, koma kufuna kufananitsa ndi chidwi zimapanga kukhala pakatikati pa chikhalidwe cha munthu.

Maphunziro a masukulu ambiri amamvetsensa kufunikaku kwa kufunafuna kufananitsa ndi chidwi. Pokhala pamodzi ndi gulu la anzanu kutali ndi zokonda za kunyumba zimapereka khalidwe lenireni lophatikizika ku dongosolo la Mtengo wa batire lolimba. Zaka khumi ndi ziwiri zizakhala zothamangitsa kuti apambane m’chochitika chimodzi kapena zingapo ndichoncho kupeza tsogolo lowala ndi lokondwa. Zikhalidwe zambiri zimakondera anzeru. Nzeru zoposa ndi chida chimene chingakupititse patali. Kodi inu munayamba mwadabwapo chifukwa chiyani ana amene amasunga ndi kuchitulusanso chidziwitso amapatsidwa mphoto kwambiri

kusiyana ndi mwana amene ali ndi mphatso kwambiri ya luso la manja awo?⁴¹ Kodi inu mungaganizire kupeza malo ku sukulu ya ukachenjede chifukwa inu m' madziwa kwambiri kusamalira munda kapena kukonza ma injini a galimoto? Kuli malo a anthu okhala ndi malusowo, koma mwayi umakonda kuyika amaphunziro pamwamba pa gulu.

Chaka ndi chaka mwana wanu akabweretsa zotsatira za ku sukulu, ndipo iwo amakhala ndi kuzindikirika kwao malingana m'mene zotsatira zao za ku sukulu ziriri. Ine ndakumana nazo nthawi zambiri pamene munthu ali ndi luso la manja koma kuvutika ndi maphunziro. Choncho zotsatira zake inu mupeza iwo akuzichepetsa okha ndi mau oti, "Izi nzopitirira ine," kapena "Ine sindingapange zimenezo." Kapena zoonekeratu "Ine ndiribe chonena pa chimenecho."

Koma osachita mantha pali njira zina zopambanira. Sukulu iriyonse imakhala ndi dongosolo la ndondomeko ya masewero imene imawalola kukulitsa tsogolo lawo la masewero. Ana amaononga maola ambiri kukulitsa luso la sewero zimene mwachiyembekezo tsiku lina zizawabweretsa iwo mphamvu ndi ulemero umene iwo amalakalaka. Ife tonse timadziwa kuti sewero ndi masewero basi momwemo eti? Nenani izi kwa onse okonda mpira wa miyendo a Chingerezi amene amafalikira m' misewu yaku Ulaya nthawi ya Chikho cha Dziko lonse. Bwanji za munthu amene amawonerera gulu lake lokonedwa la mpira omenyera ndodo ikugonja pa Chikho cha Dziko lonse? Zotsatira iye mtima wake ukulephera ndi kufa masewero asanathe. Ndipo nchifukwa chani amasewero osiyanasiyana amalandira makobiri ankhankhani pa chaka kungomenya chikopa chozungulira, kuyesa kudusisa pakati pa mitengo iwiri? Masewero ndi malonda aakulu kwabasi chifukwa amampasa wina njira yosavuta kupeza ulemu ndi kupambana ndikupeza chidwi chonse chimene munthu angaganizire. Ndi imodzi mwa ndondomeko zabwino kwambiri zodyetsera Mtengo wa batire lolimba ndi kupha chikhulupiro chimene ife tingakhale a phindu ndi ubale m' malo mwa kupambana.

⁴¹ Chikhalidwe chaku Maiko aku Madzulo ndichokhazikika kwambiri pa chikhalidwe cha a Herene chimene chimakhala cha maphunziro kwambiri kuposa luso la manja. Simwangozi kuti chirombo chamu Chibvumbulutso 13 amachifotokoza ngati chotsogolera dziko lonse lapansi poyamba kambuku oyimira ufumu wa a Herene.

Chimodzi mwa zinthu zosangalatsa kwambiri za masewero ndichoti ngakhale ungasewero bwino bwanji, koma ngati wabwera pachiwiri, palibe angazakumbukire dzina lako. Maganizo ovuta olephera angakhale owononga. Ine ndikukumbukira ndinaona osewera mpira wa miyendo angodziguwera m'bwalo la mpira akulira ngati mwana wakhanda chifukwa analephera kugoletsa chigoli chopambanitsa chikho gulu lake m'mapenote. Ine ndikukumbukira mphunzitsi wake akumuthandiza kutuluka m'bwalo la mpira ndi kudabwa m'mene iye amadzimvera kuti ndiwaphindu pa nthawi. Koma zoona kuti awa ndi masewero basi. Inde, koma ndi masewero amene ndi kulimbana kwa moyo ndi imfa a phindu ndi kulandiridwa.

Ife titha kuika m'ndanda wa milungu ina imene ife timayembekezera kuti ingationetse ife kukonedwa ndi kutipatsa ife chipambano ndi chimwemwe ife timalakalaka. Pali gawo la zinthu zooneka zokongola. Dziko la mpikisano m'mene kutchuka kupezeka kapena kutaika malingana ndi mphamvu zako. Ndi achitsikana angati mumaadziwa amene amalira kulephera kugona usiku ndi usiku chifukwa akumva kulephera kufikira pamene amafuna? Posachedwa taona kuchuluka kwa mavuto a madyedwe amene apangisa makamaka azimai kuzimana kudya, kuti matupi awo achepe.

Bwanji mu gawo lopeza chuma, udindo pa ntchito kapenanso udindo ku malo okhala. Ine ndagwirapo ntchito ya m'ofesi zaka zambiri ndipo nzosangalatsa kwambiri kuona udindo wolowezana. Ukhoza kunena za udindo wa munthu poona maonekedwe a ofesi yake. Bwana wamkulu ali ndi ofesi yapadera yokhala ndi dzenera lotha kuyang'anira msewu pansu. Ali ndi mpando waukulu wachikopa wokhala ndi popumitsira manja. Iye ali ndi tebulo lalikulu labwino pokhalanso kompyuta yamakono. Wachiwiri wake osiyana ofesi, dzenera, mpando, tebulo ndi kompyuta yosathamanga. Wachitatuso zosiyana ndi wachiwiri, osakhalanso ndi foni yabwino komanso sangathe kuona kunja kwa dzenera. Nzoseketsa pamene ukuganizira za izi, koma nzochitika ndithu m'makampani pa dziko. Ziwiya za m'ofesi ndi mbali yofunikira kwambiri yosiyansira maudindo pakati pa anthu.

M'ndanda wakusiyana mwayi ndi wosalekeza m'dziko la Mtengo wa batire lolimba, koma nthawi zambiri zimagwera muguluwa:

1. Kukwera kwa Maphunziro
2. Luso la Masewero
3. Luso la Kuyimba
4. Udindo wa Ntchito / Kukwera kwa Malipiro
5. Maonekedwe
6. Katundu / Chuma
7. Unzika

Iyi ndi milungu imene dziko limapembedza ndi chiyembekedzo choti iwo akonderedwa. Iwo amakhazikitsa a kapitawo ndipo nthawi zambiri amafuna kugonjera kwathunthu ngati uli ndi chiyembekedzo choti akukondere. Iwo nthawi zambiri amafuna nsembe ya banja ndi abwenzi ndipo ngati muli ndi mwai, mungathe kukhala ndi nthawi yanu ya ulemerero musanasuluke ndi kukhala opanda ntchito. Tonsefe timakhala akapolo kwa milungu imeneyi kudzera ku mphamvu ya Mtengo wa batire lolilmba, ndipo ndikuchokera kwa milungu imenei Mulungu akufuna kutipulumutsa ife.

13. Makwerero Opita Kumwamba

Usana unanka nachepa ndipo kudzidzira kunayamba, nthawi yodzidzira ikubwera. Inali nthawi yotolera ndi kupanga milu ya nkhuni kukonzekera kuyatsa moto nthawi yodzidzira yomwe yikubwera pakati pa chigwa kakang'ono kachimwemwe. Mwamuna wa m'nyumba anali onjinjirika kudula nkhuni pamene anaona pambali panali tinsapato tiwiri. Iye anaweramuka nayang'ana m'mwamba ndipo anaona kam'nyamata kakuona chiri chonse iye amachita. “Bambo anga angadule nkhuni mwam'nsanga kuposa apa.” “Ndichoncho?” anayankha mwamunayo modabwa kulimba mtima kwa kam'nyamatako. “Zoonadi angathe! Bambo anga angathe kupanga chinachiri chonse. Iwo ali bwino kwambiri palibenso wina.” “Chabwino iwe uli ndi mwai kukhala ndi Bambo wachonchi.”

Chonchi ndim'mene unaliri ubwana wanga. Panali masiku pamene Mai ndi Bambo sakanatha kulakwitsa ndipo anali anthu ozodzizwitsa kwambiri kuwaganizira. Mwa njira zina kunali bwino kukhala m'chikhalidwe chachibwana, koma sizikanakhala choncho. Patapita kanthawi pong'ono ku sukulu ine ndinayamba kusintha ndi kufananitsa, kuyesa kupeza malo pakati pa gulu la ana anzanga amene ndimagawana nawo zochitika za maphunziro. M'lingo wofananitsa sunali wakuya kwambiri m'makalasi oyambirira kusukulu masiku oyamba, ndipo zambiri ndimakumbukira monyadira zochitika za nthawi yoyambirira ku sukulu. Kunali zambiri zamanja ndi masewero ndi zintchito, kungoti zinali zosangalatsa. Koma kunali nthawi zimene tsogolo limaonetsedwa ndipo ine ndimakumana ndi mavuto kulawa za ufumu wa Mtengo wa batire lolimba.

Pamene ine ndinali zaka zisanu ndi ziwiri banja langa linasamukira ku sukulu yatsopano ndipo posachedwa ndinamva kuti ndiri pakati pa gulu la ana anzanga achirendo. Ndinapanga abwenzi mwachangu koma ndinakumananso ndi ena ovuta. Ndinali obadwa bwino olimba monga mwana ndipo tianyamata tina timafuna kutengerapo mwai panfundo yoti ndinali wamakhalidwe abwino kusiyana ndi iwo.

“Duntu,” “Albert wonenepa” ndi “Waulesi” ndi maina ena amene ndimakumbukira. Zinali zochitika zovuta zimene ambiri a ife takumana nazo pa chibwana chathu. Izi zimachitika tsiku ndi tsiku. M’dani wa miyoyo amagwiritsa ntchito anyamatawa kuti aononge malingaliro akufunika kwanga. M’wawa wina popita ku sukulu ine ndinaganiza m’nyozo wakwana. “Amayi, ine sindituluka m’galimoto. Ine sindipita ku sukulu.” “Zoono ndiwe mwana wanga.” “Ai sindine!” Pamene timalowa, ine ndinaona kuti awiri amaganizo woipa monga miimba kuti igwire nyama. Amai anatsegula chitseko ndipo anayesa kunditulutsa. M’phindi zochepe zotsatira zinali zovuta. Ine ndinamenya, kukana ndi kukalipa, ndi kukakamira ku mpando wanga. Kodi izi ndi zenizeni za mwana wamakhalidwe woipa? Mwina, koma pamene malingaliro akudziwika kwanga kukuonongeka, ine ndinayenera kupanga zina zake kuzipulumutsa. Ine sindikukumbukira chenicheni chinachitika patsogolo pake koma ndikukumbukira kuti kuopsezana kunasiya. Uku kunali kulawa zomwe ziri mtsogolo.

Nkhanza zoonetsedwa mwa ana ndi zinthu, zotsatira zosadziretsa za mfundo za ufumu woyerekeza wa Satana m’zochitika. Ife nthawi zambiri tingayime ndi kudabwa dyera ndi kusayamika kumene ana amaonetsa. Kodi ife michikhalidwe timakula kuchokera m’makhalidwewa? Iyai. Monga m’mene taphunzirira kuti palibe m’modzi angasiye ufumu popanda chithandizo cha Mwana wa Davide. Ife tikamakula timangokhala ochenjera ndi osinthika.

Pa nthawi imene ndimafika pakatikati pa sukulu yapamwamba ndinali okonzekeratu. Ine ndimaphunzira kupembedza mulungu wa maphunziro, mulungu wa masewero ndiponso mulungu wa maonekedwe a thupi. Ndimafunanso kupembedza mulungu wa makobiri koma sindinali pa ntchito! Zonse zondizungulira ine zimandiuza kuti ndiyenera kuyetsetsa kukhala oyamba; kuyetsetsa kupambana. Ine ndinaphunzira kuti opambana okha ndi amene amalandiridwa, ndipo olephereka sawerengedwa. Nthawi

zambiri zondirimbikitsa kuchita ku sukulu zimandichitisa kwambiri kuthekera kupeza mphoto yoyamba kuposana kungosangalitsidwa ndi zimene ndimaphunzira. Ndimaonera kanema amene amandirimbikitsa chikhulupirirochi. Otsogola osewera a amuna amaonetsedwa kupeza chinachake chopambana chimene chingakope mtima wa achitsikana. Ichi chinandipunzitsa ine kuti ubale chinali china chimene ungachipeze ndikuti ntsikana anali ngati mphoto kuposa bwenzi. Osati unganene m'njirai, koma izi ndi zonse zimachitika m'mtima.

Iyi inali nthawi ya kulota. Nthawi zambiri ndikagona pa kama ndi kulota za kumenya komaliza pothamanga kowinira mu mpira wa ndodo wa gulu la dziko la Australia, kapena kugoletsa chigoli chomaliza chopambanira, kapenanso kuyika moyo pa chiopsezo kupulumutsa buthu limene liri m'msautso. Malotowa ndiamene anapanga dongosolo la phindu langa.

Ndikamalota kwambiri, kwambirinso ine ndimatsimikizika kukwaniritsa zolingazo. Mbali yovuta kwambiri ndiyoti ine sindikanatha kukwaniritsa zolingazozo popanda kanthu. Ndikanayenera kupambana anthu ena. Ine ndimafuna abwenzi koma ndimafuna maloto anga koyamba. Ndikanakhala pachiweniweni pamene maloto anga sakuopsezewa, koma pamene ndikulingalira kuti maloto anga akutsutsidwa, inali nkondo!

Ine ndimalimbikira kwambiri kukwaniritsa zolinga zanga. Ndimachita bwino pamasewero ndi pama phunzironso; awiri pa atatu sipolakwika. Ndiyeno ndimalowa gawo lina. Ndikangofika pamwamba, ndimayetsesa kukhalabe pamwambapo. Ndimakhala chewuchewu kuyang'ana m'mbuyo kuteteza udindo wanga wapamwamba. Ndiyeno pali kuyembekezera mbiri. Ndikangopanga mbiri, ndimazifunsa kuti nanga bwanji ngati ndinapanga molakwika? Zimenezi zikhoza kukhala zonyansa, choncho ndimatsimikiza kwambiri kuti ndisagwe.

Nkhondoyi yimapitirira kwakanthawi kufikira ine ndinayamba kudzindikira kuti kufikira zolinga zanga zonse sikungakhale kotheka. Izi zifikira ku mkwiyo! Ine ndimaganiza kuti ndaputsitsidwa. Ine ndinatamikira ambuye ambiri bwino, ndipo tsopano iwo akundinyogodola. Ndimaphunzitsidwa m'dongosolo limene sirikanandipatsa ine malingaliro okhalitsa a phindu ndipo ndinali wokwiya.

Anthu ambiri amavutika kudzindikira kusakhazikika ndi kuonongeka nthawi zambiri kumaonetsedwa ndi achinyamata ndi chifukwa ambiri a iwo amazipha kapena kulowa m'makhalidwe woipa oledzera ndi mankhwala ozunguza bongo. Ine ndakkulupirira kuti nthawi zambiri iwo akazindikira chifukwa kuti sangakwaniritse maloto awo kudzera mu njira zimene anaphunzitsidwa. Iwo sazakhala amphamvu pa maso a anzawo, ndipo iwo amazionga okha.

Ine ndikukumbukira tsiku lina tikusewera mpira wamanja. Masewero anavuta kwambiri. M'nyamata wambali yina amene ndimasewera naye anayesa mwadzidzi kuponya mpira ndipo ndinamulanda bwino kwambiri m'manja mwake. Mosakhulupirira ndinamva wenzuro kuchokera kwa oyimbira mpira liu loti "walakwisa!" Ndinadziwa kuti sindinamukhudze, ndipo mwadzidzi m'kwiyo unatuluka m'kati mwanga; m'kwiyo oti dongosololi limene linandironjeza zabwino m'dziko sirinandipatse chiri chonse. Ndinam'kwiwira oyimbirayo ndikuyima pafupi pa maso pake ndikumulalatra mokweza. Chinachake chinandisuntha m'kati mwanga ndipo sinabwerere mbuyo. Mwamsanga ananditulutsa m'bwalo la mpira ndipo anandiretsa kuti ndisasewerense mpikisano. Pamene ndimatuluka, ine ndinakhulupirira kuti Mulungu anandiyankhula. Ine ndinazifunsa ndekha, "Chavuta ndi chani munthuwe? Iwe walephereratu pamene paja, sukudzilamulira!" Inali nthawi yoyamba ine ndinaziyang'ana kwambiri ndekha ndikuzifunsa kuti ndikulowera kuti. Mulungu amandikoka ine kuti ndipeze chinachake chabwino. Ine ndinayamba kumva kuti payenera kukhala njira yabwino.

M'dani wa moyo wanga nayenso anazindikira ichi ndipo anayesa kundikakamiza mwakuya kuti ndizitsimikizire ndekha, monga m'mene amachitira osuta amene walingalira kuti nthawi yake yosiya yafika ndipo amayambanso kusuta kawiri mowirikiza ndudu. Ndinayamba kuzibweza pamene maloto anga anachoka, ndipo ndinakhala osakondwa. Tsiku lina mai anga anabwera muchipinda mwanga ndipo anayamba kudandaula za khalidwe langa lotsakondwa. Ndim'mene zimakhallira m'zipinda za achinyamata amene zaka zawo sizinafike makumi awiri. Ine ndinakhala okwiya kuti iwo anabwera m'chinda mwanga kuzandiramulira. Ndinayankhula mau ambirimбири kuwauza kuti andisiye ndekha. Ndizosangalatsa kuona njira zosiyanasiyana zimene Mulungu amam'fikira

munthu. Anzanga ambiri amatchula kwa mai awo ndi chiyankhulo chonyoza. Mwinamwake bambo anga anakwanitsa kundiphunzitsa malingaliro ena olemkeza makolo, ndipo ndinalonjeza kuti sindizayankhula mai anga monga momwe anzanga amachitira. Pamene ndinayankhula mau za amai anga zinali ngati chotsalira cha ulemu wanga chandichokera. Ndinakhumudwa kuti ndinayakhula choncho, ndipo nkhawa yinali yakuya. Ndinafika pa m'lingo osatsamalanso, ndikuti anali malo woopsa okhalapo. Ndinali ndi malingaliro oti ndafika pogwira njakata. Njira yotakata imandikodola yotakata ya mowa, akazi ndi nyimbo. Mbali ina kunali njira yopapatiza monga zinanenedwa m'Baibulo. Kodi nditsatire chipembedzo makolo anga anandiphunzitsa ine kapena ndipite monga nyenyezi yowala yoyenda njira yotakata? Sindinaone choyenera kuyerekezanso kukhala M'kristu. Zinaonekerathu poyera kuti sindinali M'kristu ndipo m'mbuyomo sindinali, ngakhale ndinakulira m'Chikristu. Zinali Kristu kapena Satana. Mothokoza, Ine ndinasankha kuyesa ndi kupeza Yesu weniweni wa m'Baibulo.

Ine ndinaganiza kuwerenga buku limene linakhala zaka zambiri m'nyumba mwathu. Linali lotchedwa "Mapazi wopita kwa Krsitu". Tsopano mutuo unali oyenera pa zofuna zanga. Ndinayamba kuwerenga ndi njala ndi mosimidwa kum'peza Iye. Ndinayenera kupeza khwerero lopita kumwamba, chifukwa sindingakwanitse kugwiranso ufumu wa Satana.

Poyamba m'bukumo olemba anafotokoza kuti Yesu anabwera kuchotsa maboza amene anthu anali nao okhuza Mulungu, ndi m'mene Iye anabwerera kudzaonetsa m'mene Mulungu amatikondera ife. Ndinaalandira mau monga nthaka youma yimachitira ndi mvula ya chirimwe. Olemba anandiyitanira ine kuganizira za Yesu m'munda wa Getsemane ndi kum'tsatira Iye pa mtanda.

Pamene ndimalingalira za zochitikazo, mwadzidzi ndinamva ngati ndayimirira ndikumuona Iye. Chithunzi pa mtanda chinaoneka kwenikweni, ndipo ndinalandira maganizo mwamphamvu kuti Iye anakhomeredwa pa mtanda chifukwa choti Iye amadikonda ine ndipo ndinamvetsetsa mosimidwa kwanga kufuna kuthawa ufumu wa Satana. Ndinalandira ganizo loti ine ndiyenera kumukhulupirira Iye ngati m'nzanga weniweni ndikuti Iye anditsogolere ine ku ufumu wakumwamba. Pamene

ine ndinamuona popaja , ine ndimva malingaliro a akulu othokoza kuti Iye anali olola kundipulumutsa ine ndipo ndinamva kulemera kwa kupalamula, nkhawa, kukhumudwa ndi mantha zimene ndinazinyamula kwa zaka zambiri zikuchoka kumsana kwanga. Mtendere unalowa m' mtima mwanga umene sindinaumvepo ndi kale lomwe, ndipo kenako ine ndinalira ndikulira chifukwa cha chimwemwe. Mwana wa Davide anathyola kupyola m' mdima wanga ndi kuupyozza ndi kuwala kwa tsiku.

14. Milungu Yofanana, Maina Osiyana

Chipinda chinali chodzadza ndi zochitika, kuseka, nyimbo, ndi chisangalalo chachinyamata. Chakutsogolo kwa chipinda kunali zimasikpika ziwiri zadzikulu zikusinja nyimbo mokweza za oyimba atsopano a Rock. Ine ndinakonza phwando kuti ndisangalale ndi gulu la anzanga – zoonadi ndinayetsesa kutero. Ndinapita pa ngodya ina yachipinda pamene wachiyamata wina amafotokoza nkani yina musewero latsopano. Ndinakhala pansu ndipo ndinayesa kulingalira za zochitikazo, koma chinachake sichinakhale bwino basi. Ndinazambatuka ndikupita kunja kuseri kwa khonde ndikulumikizana ndi achinyamata “Achikondi” amene amakambirana njira zawo zatsopano zokopera achitsikana a maloto awo. Iyai, Ine sizinandisangalatsenso. M’nyamata, vuto langa ndi chani? Nyimbonso zinayamba kusandikhalira bwino m’malingaliro anga, ndipo ndinasudzumira m’chipinda ndinaona kanema poyimba amene ndinapeza kuti ndiwonyansa. Ganizo linamenya ngati sitima yakatundu, ine ndimadana nazo zinthuzi!

Malingaliro anga anathamanga ndizochitikazo. Kufikira nthawi yimeneyo izi zinali zondipatsa chisangalalo, koma tsopano sindimazifunanso. China chake chinagwira mtima wanga ndipo chinapanga kuti ndisatsangalalanso. Kuchokera kwinkwaka kunabwera ganizo loopsa loti moyo wanga wachitsangalalo unatha ndikuti ine sindizathanso kuzalsangalalanso. Ndinathamangira kunja kutsogolo kwa nyumba ndikukhala pa udzu ndipo ndinagwedeza nkhonya yanga m’mwamba nalira mokweza. “Iwe waonga moyo wanga!”

Panali patangopita masabata angapo kuchokera pa ‘Zochitika za njira yanga ya Damasiko’ ndi Yesu. Moyo wanga unatembenezika dodolido. Sindinamvereponso mtendere wochuluka pa moyo wanga, ndipo Baibulo linayamba kukhala la moyo. Ine ndimamwa zonse ndi kukumana ndi ufulu umene sindinawudziwenso konse. Pamene Yesu anafika m’moyo wanga, kusintha kunali pompo. Mwadzidzi, ndinakhala odziwa kuti mayankhulidwe anga ena sanali abwino, ndikuti nthabwala zanga zina zinali zolakwika, ndiponso kuti mbali zina za moyo wanga zinali zosagwirizana ndi njira yatsopano imene ndinalingamo tsopano. Ine ndinali pa ulendo opita ku ufumu watsopano. Zinali ngati ndikupita ku dziko lachirendo kwambiri ndikuphunzira chiyankhulo ndi miyambo kuchokera popanda kathu. Ndimafuna kuphunzira chifukwa ndimam’konda Ambuye wa ufumuwo, koma ndinali nditaphunzitsidwa m’ufumu osiyana, ndipo ziyenera kutenga nthawi ndithu kuti ndisinthike kwenikweni.

Zinali kufikira usiku uja wa phwando pamene ndinadzindikira kusintha kwenikweni kumachitika. Kuchokera pamene Yesu analanda mtima wanga ndi chikondi Chake, sindinam’kanizenso Iye pamene Iye andiyitana. Choncho usiku uja wa phwando pamene ine ndimapanga zimene ndimaganiza nzabwino; ine ndinatha kulingalira kuti Iye akundiyyitana ine kuchoka ku moyo wa tunduwo. Chifukwa sindimadziwa chinachiri chonse, ndinali ndi mantha kuti chimene chingalowe m’ malo mwake sichingakhale chabwino. Mwamwai ine ndinasankha kukhulupirira kuti Yesu andisamalira ndipo kunali bwino kukhulupirira Iye koposa maganizo anga.

Pamene ndinamulandira Yesu ngati Mpulumutsi wanga ine ndinali otsangalala kwa masabata angapo. Ine ndinalingalira ubwenzi wapedera ndi Iye umene unakhalabe ndi ine kufikira tsiku la lero. Yesu ananditsegulira zipata za kumwamba, koma tsopano Iye andithandiza kuchotsa mbeu ya Mtengo wa batire lolimba. Iye anayamba kundithandiza kuzula nzeru ya moyo umene umapanga ntchito ndi kupambana kukhala pakati pa dongosolo la phindu langa. Ndiulendo umene mwana aliyense wa Adamu ayenera kutenga. Njira yokhaya ife tingapange ndi kusunga maso kuyang’anitsa pa kuwala kwa mtanda ndi mozichepesa kutsata mapazi a mpulumutsi wathu m’ndondomeko za ufumu watsopano.

Ndinayamba kupezeka m'misonkhano ndi anzanga. Pa usiku oyamba pamene tinagwada tonse ine ndinamva Mzimu wokoma wa Mulungu otizungulira tonse, koma panali mzimu wina kuchokera ku moyo wanga wakale umene umandivutitsa ine. Pamene ife timapemphera titakhala mzere mozungulira, ganizo linandimenya: "Ine sindingathe kupemphera monga anthuwa akupempherera, akupemphera momveka bwino." Malingaliro anga anamangika m'maganizowa pamene mapemphero amasunthira pafupi ndi ine mtima wanga unayamba kuthamanga. Posachedwapa ndikhala ine ndipo aliyense amvera ine. Koma dikirani kamphindi; uwu unali msonkhano wa mapemphero a Yesu, osati ine!

Pano pali temberero la Mtengo wa batire lolimba. Ngakhale ndinapereka mtima wanga kwa Yesu ndipo ndimafuna kumutsatira Iye, mfundo za moyo wanga wakale zinali zokonzekabe ndi kulola kundikokera m'mbuyo kundipanga kukhala pakati pa chirichonse, kupanga zochita zanga m'pemphero kukhala nkhani, kutsutsana ndi ubale wanga ndi Mulungu m'pemphero.

Ine pamene ndinayamba kuphunzira Baibulo koyamba, nthawi zambiri ndimamva kuperewera chifukwa, ngakhale ndinakulira m'Chikristu, ndinadzindikira kuti mau a m'Baibulo sinamalize ku sukulu ya mkaka. Ine ndimakonda kumvetsera ku zimene amandiphunzitsa koma kumbuyo kwa malingaliro anga china chake chindidandaulitsa ndikunena, "Two akupeza mavesiwo mosavuta bwanji, ine sindimatha kutero." Ndimavutika kupeza buku lolondola ndi vesi, ndipo ndimangopemphera kuti ndisakhale omaliza ndikuti aliyense adzidikirira ine. Zochititsa manyazi! Zaka za maphunziro ndinalandira ozifananiza ine ndi anzanga anayamba kutumphuka m'ulendo wanga watsopano wa Chikristu. Zinali zosavuta Mzimu wa Kristu kundipeza olakwa za malankhulidwe anga ndi kakhalidwe ka moyo wanga, koma zitha kunditengera nthawi kuti ndidzindikire m'mene ziriri kuya kwa ziyangoyango za Mtengo wa batire lolimba zikuthamangira.

Pamene ndimapitiriza ulendo wanga ndinakhala ndi chikondi chakuya cha Baibulo. Inali imodzi mwa njira zophunzirira za ngwazi yanga imene inapereka moyo Wake chifukwa cha ine. Ndimangokonda kuphunzira za Yesu ndipo linali dalitso, koma moyo wanga wakale limandibisalira, kukonzekera kukhala msampha wanga. Ine ndinayamba kudzindikira kuti

anthu ondizungulira anali ndi chidziwitso chochepa kuposa ine ndimachitira ndi zinthu za m’Baibulo. Kukula kwanga kwa chidziwitso cha Baibulo kunandipatsa chidaliro choyankhula ndipo posachedwa ndimatenga timagulu tating’ono kenako magulu aakulu kupangisa maphunziro a Baibulo. Kachiwirinso, iri linali dalitso kwa ine ndi amene anandizungulira, koma zinali pang’ono ndi pang’ono, mokhazikika zimabwerera m’mbuyo pa nsanja ya phindu chifukwa cha ntchito m’malo mwa phindu m’ubale. Zimachitika pang’onopang’ono mosazindikirika, koma zimachitika. Poganzira zimene zimachitika ine ndimaona kuti ambiri a ife, tiri ndi milungu yofanana koma maina wosiyana.

Ngati mungayang’ane m’bokosi liri pansipa, mutha kuona m’mene ziri zosavuta kukhulupirira m’Baibulo koma kukhala monga a dziko. Sindikutanthauza kuti kukhala wamakhalidwe ngati wosapemphera, ndikutanthauza kukhala ndi phindu chifukwa cha ntchito.

Mu Dziko	Mu Tchalichi / m’Mpingo
Maphunziro	Chidziwitso cha Baibulo
Luso la Masewero	Luso loyakhula pa gulu
Luso lopanga zopanga zinthu	Luso la utumiki wa nyimbo
Udindo wa ntchito	Udindo m’tchalichi / mpingo
Katundu	Mphatso za Uzimu
Mawonekedwe a thupi	Perete wa fashoni m’tchalichi
Unzika	Kukana kusintha / Ololera kusintha

Kwa ambiri a ife kuyenda ndi Yesu kumasokonekera ndi mphamvu yonyenga ya Mtengo wa batire lolimba. Ndikamayang’ana m’tchalichi lero ndimaona kuti milungu ife timafuna kuyisiya m’dziko yimatipeza m’tchalichimo. Iyo yimazibveka yokha ndi zovala zoyera ndipo timazikumbatira ngati abwenzi abwino. Mosalephereka zostsatira zake ndi m’kwiyo, kuwawidwa, ndi kumenyana m’tchalichi. Nkosavuta kuoneka a uzimu m’tchalichi, koma nanga bwanji munthu okhala mbali yina ya tchalichi amene sangakuyankhuleni chifukwa m’namunenera zoipa kumbali ndipo anamva? Nanga bwanji oyimba limba amene anakalowa mpingo wina

chifukwa munamunyoza kuti sayimba bwino? Nanga bwanji kulondanalondana m'mpingo kuti mupeze wina oswa mbendera za mpingo kuti m'mugwetse? Nanga bwanji “wofuna kusintha” amene afuna kulanda mphamvu za oyendetsa chipembezo ndikukakamiza mapembezodwe atsopano pa aliyense, ndipo zosakhala bwino kwa amene safuna? Pali zambiri ndikuti m'ndandanda ndiwosatha ndipo m'dani wamkulu wa miyoyo yathu akudziwa kuti nangati tikuyendera zimenezi ngakhale tiri m'mpingo, tiribe m'ufumu wake.

Umboni wakulu oti tikuwonongekabe ndi mfundo za ufumu wa Satana ndi kukwera kwa chiwerengero cha kusagwirizana ndi kusoweka kwa chikondi cha Chikristu m'mpingo. Ubale wathu ukanakhala monga Mulungu amachitira nafe, mukanakhala chikondi chochuluka m'mpingo ndikusamalirana kwambiri pamene tikuchitirana wina ndi mnzake.

Nzochititsa chidwi kuti milungu ya m'dziko mochenjera yalowa m'mpingo muzochitika zathu ndikuti zikuchitikanso muzochitika za mpingo wonse. Mzaka zam'mbuyomo, pamene mfumu Constantine “analandira” Chikristu, panali zinthu zambiri zosinthika zimene zinachitika m'mpingo wa Chikristu. Mfundo imodzi yopatsa chidwi ndiyo mafano ambiri a milungu yachikunja amene anali mu Pantheon (mpingo wa milungu yonse) anayisamusira m'mpingo wa Chikristu ndipo maina awo anasinthidwa m'makhalidwe a m'Baibulo monga Mose, Davide, ndi Petulo. Milungu yofanana, maina osiyana! Sinkhaniyi kuti inu mukuyibveka bwanji, ndichikunja basi, ndipo lero tingathe kunena chani? Ndi chinthu chimodzi kudzudzula mpingo wonse chifukwa chopatuka ku choonadi cha atumwi. Ndi chinthu china kuona mfundo zofanana zikugwira ntchito m'miyoyo yathu. Tionetsetse kuti ife tachotsa mtengo m'diso mwathu tisanachotse chitsotso m'diso la m'bale wathu.

Ndzopasa chidwi kuphunzira ulendo wa ambiri omutsatira ozipereka kwa Kristu – wophunzira Ake. Nkhani ya mphamvu ndi udindo zimakambidwakambidwa. Tiyeni tione ndime zochepa M'malemba:

Nthawi yomweyo ophunzira anadza kwa Yesu, nanena, Ndani kodi ali wopambana mu Ufumu wa Kumwamba? Mateyu 18:1

Pali chifukwa chimodzi ndipo ndi chifukwa chimodzi basi chifukwa ophunzira amamufunsira funsolo – kudzikonda. Ophunzira amakhulupirira Yesu kuti ndi Mesiya, Kristu. Iwo anali okondwa ndi kukhudzidwa za chikhulupiriro chawo mwa Iye; ena amathanso ngakhale kulola kufa chifukwa cha Iye, komanso monga ine pamene ndimakonzekera kuti ndipemphere ndipo malingaliro anga anatembenukira kuchokera ku ubale wanga kunka ku ntchito zanga mu pemphero, ophunzira anasuntha kuchokera ku ubale wao ndi Mesiya kunka ku udindo wao mu ufumu Wake watsopano.

Ndipo anadza kwa Iye Yakobo ndi Yohane, ana a Zebedayo, nanena naye, Mphunzitsi, tifuna kuti mudzaticitire cimene ciri conse tidzapempha kwa Inu. Ndipo Iye anati kwa iwo, Mufuna kuti ndidzakucitireni inu ciani? Ndipo iwo anati kwa Iye, Mutipatse ife kuti tikhale m’modzi ku dzanja lanu lamanja, ndi wina kulamanzere, m’ulemerero wanu. Marko 10:35–37

Mulungu wa udindo ndi mpando anapitirira mfundo za ufumu watsopano ndikuti Yakobo ndi Yohane amaphunzira, kuti iwo anamfunsa Yesu ngati iwo angathe kukhala kumanja Kwake ndi kumanzere m’ufumu Wake. Mwamwai Yesu sanatope ndi kulepheralephera kwao kuti asiye za mfundo za ufumu wakale. Iye anamvetsetsa kuti zimatenga nthawi kuti ife tione kuya kwa mfundo za ufumu wa Satana m’mene ziriri. Vuto ife timakumana nalo ndi loti pamene talola mfundo zakale kutipitirira chotsatirachi chimachitika:

Ndipo pamene khumiwo anamva, anayamba kupsa mtima chifukwa cha Yakobo ndi Yohane. Marko 10:41

Pamene ife talola mfundo za ufumu wakale kuti zitamulire, mikangano nthawi zonse yimatsatira. Zimene Yakobo ndi Yohane anachita zinapangitsa ophunzira ena kukwiya. Chifukwa chani? Chifukwa iwo amapereka uthenga woti, “Ifé tiri bwino kuposa inu.” Mwina iwo samafuna kupanga chocho koma nthawi zonse zimatsatira choncho. Yesu anatengerapo mwai owadzindikiritsa m’mene ufumu wa Mulungu uliri osiyana ndi umene iwo anakuliramo. Iwo ayenera kuphunzira kuganizira mosiyana.

Ndipo Yesu anawaitana, nanena nao, Mudziwa kuti iwo amene ayasedwa ambuye a mitundu ya anthu amacita ufumu pa iwo;

ndipo akuru ao amacita ulamuliro pa iwo. Koma mwa inu sikutero ai; koma amene ali yense afuna kukhala wamkuru mwa inu adzakhala mtumiki wanu; Ndipo amene ali yense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse. Pakuti ndithu, Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo Wace dipo la kwa anthu ambiri. Marko 10:42–45

Lolani mauwa kumveka kosatha m'makutu mwanu! Ngati ndikukhumba kwanu kukhala wamkulu mu ufumu wa Mulungu ndiyeno phunzirani kutsangalala kutumikira ena koposa m'malo molamulira ndi kunyenga iwo. Yesu akutiya ife kuti achikunja (amitundu) amalumulira ena ndi kutsangalala kugwiritsa mphamvu zawo ndikuonetsa bwana ndani. Mwachirendo kwambiri, mzimu omwewo nthawi zambiri umalamulira mpingo ndi ziwalo zosiyanasiyana kufunafuna kukhazikisa zofuna zawo ndi ulamuliro pa mpingo. Zaka zikwi ziwiri kuchokera pa mtanda komabe ambiri a ife sitikumvetsetsa mfundo zake.

Nchifukwa ninji m'dani wa miyoyo yathu sapeza mavuto kutibwezera m'mbuyo ku njira zathu zakale za maganizidwe? Monga tanenera poyamba, ndikuchokera ku malingaliro athu akuya wa osatetezeka kumene kumapangitsa Satana kusavutika kutiyetsa ife kuzitsimikizira tokha. Mpokhapokha ife tikakumbukira m'mene ife timapezera phindu lathu tizapeza chovuta kukaniza kuyesa kutembenuza miyala kukhala mkate kuzitsimikizira kuti ndife ofunikira.

Pali chinthu chimodzi ine ndimachipeza chodetsa nkhawa za mfundo ya Mtengo wa batire lolimba imene imatitsatirabe motikakamira ife. Yesu anali mphunzitsi wabwino kwambiri dzikoli sirinaonenso. Iye anakhala zaka zitanu ndi theka ndi ophunzira, kuwaphunzitsa iwo m'mene akanathera za ufumu wakumwamba, ndipo ngakhale pa zonsezi tikupeza kuti pa usiku weniwenio wa kupachikidwa Kwake ophunzira anali kulumulidwabe ndi mfundo za moyo wakale.

Ndipo coteronso cikho, atatha mgonero, nanena, Cikho ichi ndi pangano latsopano m'mwazi Wanga wothiridwa chifukwa cha inu. Koma onani, dzanja lace la iye amene adzandipereka

ali pagome pano pamodzi ndi Ine. Pakuti Mwana wa munthu amukatu, monga kunaikidwiratu; Koma tsoka munthuyo amene ampereka! Ndipo anayamba kufunsana mwa iwo okha, ndiye yani mwa iwo amene adzacita ici. Ndipo kunakhala kutsutsana mwa iwo, ndani wa iwo ayesedwe wamkuru. Luka 22:22-24

Pa madzulo penipenipo a tsikulo loonetsera chikondi chachikulu chirengedwe sichinaonenso, iwo amene anali pafupi ndi Yesu, amene amadziwa zambiri za ufumu Wake kuposa wina aliyense, amakangana kuti ndani wa iwo ndi wam’kulu. Chisoni chimene Yesu anakumana nacho pa nthawiyo chinayenera kukhala chachikulu kwambiri! Nkutheka iwo a ife amene timaziyesa om’tsatira Yesu tikubwereza zophophonya zofanana monga ophunzirawo – om’tsatira enieni a Yesu, komabe kulimbana pakati pa ife tokha kuti ndani amene ali wamkulu?

Pali chinthu chimodzi choipa kwambiri kuposa kulamulidwa ndi mfundo za Mtengo wa batire lolimba m’dziko, ndiko kulamulidwa ndi iwo m’mpingo. Mulungu atithandize kuti timasulidwe kuchoka ku mfundo zozifunira tokhazi kuti ife tikumane ndi chimwemwe cha ufumu Wake!

15. Mukuwerenga Bwanji?

Lero likhala tsiku lapadera. Inu muli wodzadza ndi chiyembekezo ndi chitsangalalo ndi kuthekera zimene mukuyembekezera patsogolo. Bwana wa kampani yaikulu yopanga zinthu ali ndi chidwi ndi chifanifani chapadera chimene inu munachikonza ndipo akufunitsitsa kuti achipange ndikuchigulitsa ku dziko lonse lansi. Inu mwaganiza kuti mukumane pa nkhomaliro ku malo odyera abwino m’deralo. Chifukwa simunayambe mwaonanapo, inu m’maonekedwe onjenjemera mukuyesa kuti mum’dzindikire munthuyo amene asinthe maloto anu kukhala zenizeni. Otsachedwa wabwera ndipo mukugwirana chanza mwamphamvu, kenako nonse awiri mukulowa m’kati modyera ndikupeza malo. Kuti mudziwane, amene mudye naye bwanayo akukufunsani pan’ono za banja lanu ndi kumene m’makhala ndi m’mene ana anu akuchitira ku sukulu. Zonse zikuyenda bwino ndithu kupatula chifukwa choti kumbuyo kwanu kuli m’kulu wina amene akupanga phokoso pakumwa m’suzi. Poyamba mwangodzisiya, koma popita nthawi zikufika posatsangalatsa. “Anthu ena akufunika kuphunzitsidwa ulemu pang’ono” inu mukuganiza mwa inu nokha, koma mwangodzisiya kuti asakusokonezeni. Kukambirana kukuyenda bwino ndi wamalonda m’nzanu, ndipo muli pakatikati kukambirana za phindu lowonjezera pa chifanifani chanu pamene mwadzidzi m’kulu wakumbuyo kwanu uja anageya moopsa kwambiri moti pa tebulo panu panakhuzidwa kwambiri. Maso onse modyeramo anamuyang’ana m’kulu wachirendoyo amene anaoneka kuti alibe ulemu ndithu. Chipinda chonsecho chinadzadza ndi kunong’ona ndi kuseka kophatikiza kudabwa ndi kunyansidwa. Potsiriza mwini malo odyera

anatulukira ndikumufunsa m'kuluyo adzipita, ndikunena kuti makhalidwe a mtundu umenewo ngosaloledwa modyeramo.

Chinthu chimene chiri chodabwitsa ndichoti ngati m'kuluyo anali m'malo wodjera amene amaonetsa makhalidwe achi Tchaina, palibe amene akanamudabwa. Ndipotu anyamata ndi atsikana ogwira ntchito m'menemo akankhumudwa ngati inu simunaonetse kukhuzidwa. Muchi khalidwe chachi Tchainanso simupatsana moni wapamanja ndi munthu wina amene simunakumanepo ndi kale lomwe kapena kukambirana za m'banja pa nkhomaliro inu mutengedwa amwano kwambiri.⁴²

Nzodabwitsa m'mene zochitika zomwezo zikhoza kutanthauzidwa mosiyana malingana ndi m'khalidwe kapena dziko limene mukuchokera. Mfundoyi ndiyosasiyana pamene ife tikuyang'ana makhalidwe awiri osiyana a ufumu wa Mulungu molimbana ndi ufumu wa Satana.

Chikhulupiriro cha Chikristu chiri ndi maziko amodzi, Yesu Kristu, tikaona kunyanzira kuonjezekera kwa magulu amene amatenga dzina la Yesu sitimvetsa kupeza kuti pangakhale zotsutsana zambiri pa maziko amodzi. Ulendo opita m'ufumu wa Mulungu kumafuna kusiya makhalidwe ndinso kusiya maonekedwe a dziko. M'chaputala chapitachi tinafotokoza za vuto limene timakumana nalo pophonzira kuganiza m'njira za Mulungu.

Mavuto a akulu akuyenda m'Chkristu amakhudza njira m'mene timafikira Mau a Mulungu, Baibulo. Ife tikutuluka m'dziko m'mene ife taphunzitsidwa mu kupambana ndi udindo, koma pamene ife tikulowa m'ufumu wa Mulungu nzofunika zedi kusiya maganizo athu ndikulola Mzimu wa Mulungu atiphunzitse m'mene ife tingawerengere Mau a Mulungu. Mwachisoni nthawi zambiri izi siziri choncho, ndipo zotsutsana zambiri, mipatuko ndi mikangano zopezeka m'chikhulupiriro cha Chikristu ndi mbiri zachokera powerenga Baibulo ndi Mtengo wa batire lolimba m'malo mwa chimango cha kumwamba, chimene chimalunjika pa ubale ovomerezeka ndiponso wapamtima.

Yesu akupereka mfundo pakukambirana Iye ndi wachiramulo mu Luka 10. Wachiramulo akufunsa Yesu, “Mpulumutsi, ndidzalowa moyo wosatha ndi

⁴² <http://www.chinawestexchange.com/Chinese/Culture/customs.htm>

kucita ciani?” Yesu anayankha, “M’ciramulo mulembedwa cani?” Kufuna kupeza nkhani mwakuya Iye akufunsa, “Uwerenga bwanji?”⁴³ Yesu sakufunsa iwe ukuwerenga “Chani”; Iye akufunsa ukuwerenga “Bwanji”, kapena kuti ukutanthauzira bwanji zimene ukuwerenga? Iri ndifunso kwa aliyense amene akufuna kutenga njira yochoka ku dziko la Mtengo wa batire lolimba kunka ku ubale wakumwamba – Iwe ukuwerenga bwanji?

Funso lokhudzana ndi moyo wosatha limene wachiramulo anamufunsa Yesu ndi limodzi mwa mafunso ofunikira kwambiri pa ulendo wa Chikristu. Udindo wumene uli nawo ndi anthu umayanjana nawo ndi chisonyedzo champhamvu cha phindu m’dzikoli. Posiyanitsa, m’ufumu wakumwamba munthu aliyense ndi mwana wa Mulungu ndipo ayenera kulemekezedwa ndi ulemu. Tikasatira kukambirana kwao ife tikuona kuti wachiramulo akufuna kutanthauzira Malemba m’njira yakale kuposa yatsopano. Iye akumpatsa Yesu yankho lolondola pomena, “Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, ndi mphamvu yako yonse, ndi nzeru zako zonse ndi mnansi wako monga iwe mwini.”⁴⁴ Yesu akunena potsatira, “Wayankha bwino; cita ici, ndipo udzakhala ndi moyo,” koma wachiramulo podzindikira kufunikira kwakuya kokhudza nkhanayi iye akufuna kukhotetsa tanthauzo pofunsa, “M’nansi wanga ndani?” Kutanthauza kwa Malemba nkosavuta koma mtima wa munthu olamulidwa ndi Mtengo wa batire lolimba amachita ngati nzovuta kumvetisa, chifukwa sulola kusiya za kale ndikulandira kwambiri zatsopano. Apa ndipo pagona chifukwa cha Akristu ambiri opanda moyo, iwo amakhulupirira m’ufumu wa Kristu koma akukhala ogwirizana ndi ufumu wa Satana ndipo zotsatira ndi chisokonekero, kukhumudwa, ndi zoipa.

Chikhulupiriro cha Chikristu chonse nchosokonekera pa nkhani ya chipulumutso chifukwa Baibulo likuphunzitsa momveka bwino kuti Chikristu nchopatsidwa mphamvu ndi chisomo kukhala mogwirizana ndi Malamulo Khumi. Komabe, ambiri a ife timafikira Malamulo Khumi m’zochitika za Mtengo wa batire lolimba; ife timafuna tiwasunge iwo ndicholinga chopeza chipulumutso, m’ malo moona Malamulo Khumi

⁴³ Luka 10:25, 26

⁴⁴ Luka 10:27

monga malongosoledwe a ubale olonjzedwa uzachitike pakati pa Mulungu ndi ana Ake.

Tikawonetsetsa, ndipo zachulukira kuti ife tiri ndi khamu lonse limene limaona kusatheka kuchita zofunikira za lamulo, komabe m'malo molowa ndi chikhulupiriro cha ubale, iwo amanena kuti nkosatheka kusunga Malamulo a Mulungu ndichoncho sangatsangalale ufulu wachipambano mwa Kristu. Kaya inu mufuna kuchita kapena mufuna kusachita, nkhani ndiyotibe ntchito m'malo mwa ubale. Palibe pa maguluwa amene angalowe m'ufumu wakumwamba kupatula atasunga Malamulo Khumi m'nkhani ya chikhulupiriro chokhazikika pa ubale ndi Iye amene anafa chifukwa cha ife.

Kwa gulu la Chikristu limene limayika kuti sangachite ndikuti nkosatheka kupambana m'ulendo wa Chikristu, posachedwa chotsatira nchoti mulungu amene iwo amamutumikira iyenso sangathe kuchita. Kuphatikiza chizolowezi ndi chilakolako cha dziko chofuna kudziwika ndipo nzosadabwitsa kupeza ophunzira, aziphunzitsi, ndi okhulupirira a Chikristu amene amakana kuthekera kwa Mulungu kulenga dziko m'masiku asanu ndi limodzi enieni. Monganso wachiramulo akupereka yankho loti iye azikonda m'nansi wake koma kenako akufunsa, "M'nansi wanga ndani?" choncho ophunzira ambiri lero amati, "Inde ife timakhulupirira m'masiku asanu ndi limodzi achiregedwe, koma ndi masiku wotani?" Zoipa nthawi zonse zimafuna njira yosokonezera Malemba kuti aziyenere okha; kukhulupirira Kristu komabe akukhala ogwirizana ndi dziko.

Munthu akango taya chikhulupiriro mwa Mulungu amene angalenge mtima watsopano ndipo waphunzira kufunsa mafunso osokonekera za mau omveka bwinobwino a m'Malemba, ndiyeno nkosavuta kulola ndi kuvomera kugonana amuna kapena akazi okhaokha ngati khalidwe la m'Kristu pamodzi ndikukana maudindo a amuna ndi akazi, m'nyumba ndi ku mpingo, zimene Baibulo limandandalika bwino kwa ife. Malingalirowa ndi achilendo ku ufumu wa kumwamba. Phindu nthawi zonse limazera m'ubale osati m'udindo.

Titha kundandalika phunziro ndi phunziro m'Baibulo zimene zasokonekera ndi kutembenuza kugwirizana ndi mfundo za mphamvu, udindo, ndi ntchito, koma ine ndikuganiza mfundo yapangidwa bwino kuti ngati ife

tizitcha otsatira a Yesu ndiyeno ife tizafuna kutanthauzira Malembo mogwirizana ndi mfundo za ufumu Wake m'malo mwa ufumu kumene ife tonse tachokera.

16. Osakhalanso Kapolo

Inali imodzi mwa nthawi zapadera. Mwana wanga wa zaka zisanu ndi chimodzi ndi ine timayenda tonse pa galimoto. Tinali kukambirana zakuya ndi zofunikira, chabwino, zakuya monga zochitika mwana wanga wapa mtima akanalola kuzitsatira. Ine ndinatha kuona maganizo anzeru akuyenda m'mutu mwake. Ine ndinazindikira kuti iye anali pafupi ndi chinachake chofunikira kwambiri, ndipo kenako anachinena. “Mudziwa Abambo, ine ndikuganiza kuti zinthu zitha kuyenda bwino kwambiri ngati inu munali bwana nthawi zina, ndipo ndinali bwana nthawi zina.” “Chabwino mwana wanga, ndithudi ilo ndiganizo losangalatsa kwambiri,” ine ndinayankha pa maganizo ake. Panali kanthawi ka chete chifukwa ine ndimayesa kuganzira chifukwa chabwino choti ganizo lake linali loperewera, ndipo ngati sindingathe kuganiza za chimodzi tonse tingathe kuthera muvuto. “Chabwino, ndithu sim'mene Baibulo limatiuzira ife m'mene tingachitire, mwana wanga.” “Koma nchifukwa chani inu m'mandiuza ine zoti ndichite nthawi zonse?” “Chabwino mwana wanga, Yesu wandifunsa ine kuti ndikuphunzitse m'mene ungakhalire wachinyamata wamphamvu chifukwa Chake, ndipo chifukwa Iye ndi bwana wanga ine ndiyenera kuchita zimene Iye wandiuza ine kuchita.”

Kulera ana ndikuphunzira kovuta kwenikweni. “Mwana wanga, chonde khala pansu pamene ukudya.” “Aa, sichirungamo!” “Okonedwa, chonde tenga zidole zako ukasunge.” “Aa amai, ine ndikufuna ndipite panja ndikasewere.” “Mwana wanga ndi nthawi yopita kukagona.” Kulira,

kudandaula mosatsangalatsa kapena m’khalidwe obwerezabwereza, kukuwa, “Koma inu simukupita kukagona tspano. Chifukwa chani ine ndipite?”

Malamulo ndi malangizo onsewa! Mutha kuganiza kuti makolo ndi ankhanza nthawi zonse. Chifukwa chani ana sangathe kumvetsa kuti inu mukufuna iwo akhale chete ndi kudya pang’onopang’ono pa gome kuti iwo asansanze? Kapena mukufuna iwo aphunzire osamalika ndi a ukhondo kuti aphunzire kulongosoka ndi luso pamene iwo akakula? Ndipo ndichifukwa chani ana safuna kuyamika kuti inu mukufuna muwateteze kuti asadwale pokhala ndi nthawi yambiri yogona? Chifukwa chani? Chifukwa iwo sadziwa mbuna ndi zoopsa za moyo.

Mtumwi Paulo akutenga fanizoli mwachitsanzo ulendo wathu m’moyo wa Chikristu.

Koma ndinena kuti, pokhala wolowa nyumba ali wakhanda, sasiyana ndi kapolo, angakhale ali mwini zonse. Agalatiya 4:1

Paulo akufotokoza ubale wa mwana kwa makolo ake ngati osasiyana ndi kapolo kwa mbuye ake. Abambo ayenera kuphunzitsa mwana wake m’mfundo za ufumu wa Mulungu, koma mwana ndi khalidwe lake la Mtengo wa batire lolimba samvetsa chifukwa cha kuphunzirako. Maphunziro ambiri bambo ake azamphunzitsa iye ali osiyana ndi khalidwe lake ndipo nthawi zambiri ndi ntchito yovuta yimene yimaoneka yosasiyana ndikukhala kapolo. M’nyamata sangavutike kudabwa, “Chifukwa chani bambo anga amandiretsa ine kupanga zinthu zimene ndimafuna? Ine ndimadzimva ngati kapolo. ‘Mwana wanga, panga ichi, mwana wanga, usapange icho,’ Sichioneka chirungamo!”

M’khalidweu umafotokoza mwangwiro zochita za Mulungu ndi ife pamene Iye akufuna kutikonzetsera ife m’ufumu wa Mulungu. Ambiri amaona malangizo a Mulungu ngati ovuta ndi okakamiza ndipo nthawi zambiri amafunsa, “Chifukwa chani analola kuti izi zichitike kwa ine kapena chifukwa chani moyo wa Chikristu umaoneka okhwimitsa?” Palinso ambiri amene anayamba mpingo amene amaoneka okhutira kukhala monga ana ndi kungokhala akapolo basi, kugwira ntchito za moyo wa Chikristu ndi kuyembekezera kuti azapatsidwa mphoto chifukwa cha ntchito zawo, anthu

otere ali m'chiopsezo chokutidwa ndi maganizo a mwana wam'kulu mu nkhani ya mwana olowerera.

Paulo akufotokoza kwa ife m'mene ife tingamasulidwe ku zovuta zambiri za moyo ndi kufunsa zochita za Mulungu ndi ife. Pamene ife tingamvetsetse kuti Mulungu ndi Atate athu ndikuti akutikonzetsera ife kulowa mu ufumu Wake ndikuti Iye amatikonda kwambiri, ndiyeno ubale wathu ndi Mulungu uyamba kukhala ndi nzeru. Malamulo ndi malangizo sakhalanso chipsinjo ndi malire otiretsa kutsangalala; m'malo mwake iwo akhala makomo a ufulu aulula nkhani yachifundo ya Mulungu kwa ife ndi khumbo la chilakolako Chake kuti ife tirandire cholowa chatu chodzadza monga ana a Mulungu . Paulo akufotokoza m'njirayi:

Koteronso ife, pamene tinali akhanda, tinali akapolo akumvera miyambo ya dziko lapansi; koma pokwaniridwa nthawi, Mulungu anatuma Mwana Wace, wobadwa ndi mkazi, wobadwa wakumvera lamulo, kuti akaombole akumvera lamulo, kuti ife tikalandire umwana. Ndipo popeza muli ana, Mulungu anatomiza Mzimu wa Mwana wace alowe m'mitima yathu, wopfuula Abba, Atate. Kotero kuti sulinso kapolo, koma mwana; koma ngati mwana, wolowa nyumbanso mwa Mulungu. Komatu pajapo, posadziwa Mulungu inu, munacitira ukapolo iyo yosakhala milungu m'cibadwidwe cao. Agalatiya 4:3-8

Awa ndi mau ena okongola kwambiri m'Malemba. Pamene ife tikudzindikira nsembe ya Yesu kutipezera kutikhazikitsira ife monga ana a Mulungu, ife tamasulidwa kuchokera ku ukaolo wa ufumu wa Satana. Ife timasuka a ufulu kuchokera ku ulamuliro wa nkhanza wa Mtengo wa batire lolimba ndipo timaima olimba ndi olemekwezeka monga ana a amuna ndi akazi a Mulungu, kudziwa kuti chifukwa cha Yesu ife nthawi zonse tizakhala ana okonedwa Ake. Kodi Mzimu wa Mulungu wapfuula m'mtima mwanu "Abba Atate," Abambo, Abambo?" Kodi m'mamva kukhazikika m'chikondi Chake kuti inu mungathamangire m'manja Ake ndi kudziwa inu kuti simwangolandiridwa kokha koma okhumbidwa mwakuya ndi Iye? Kodi inu mwabwereranso ku chibwana cholemekezeka ndi Atate anu chimene chimawala pamene Iwo ali pafupi? Kufikira inu mtakumana nao ufuluwu,

inu muzakhalabe nthawi zonse kapolo amene amakhala wosalandirika amene mawa muzapatsidwa chirango chanu chokhwima.

Monga ana a Mulungu, cholowa chathu nchotsimikizika. Ife molimba mtima tingathe kubwera kwa Iye ndi kupereka zofuna zathu; ife tingathe kudalira motsimikizika kuti Iye amadziwa zabwino zofunikira ife. Chiri chonse chochitika kwa ife m'moyo nchotithandiza ife kukula m'kumvetseta mwakuya za phindu la ufumu wa Mulungu ndi kuthyola ukapolo wa Mtengo wa batire lolimba. Inu m'kukumbukira m'chaputala cha chisanu ndi chimodzi kuti tinakambirana ntchito yofunikira kwambiri ya Mulungu anakumana nayo pofunafuna kubwezera mtundu wa anthu m'kukumbatira kwa chikondi Chake. Pano pali mfundo zakenso:

1. Njira yompatsa munthu ufulu odzindikira m'khalidwe wao otsimidwa, pamodzinso njira kwa iwo kuti akopeke ku njira yabwino kopanda kuphwanya ufulu wao osankha.
2. Njira yowatsonyeza iwo kuti anali ndi maganizo olakwika za khalidwe la Mulungu ndi ufumu ndiponso kuwaonetsera iwo kuti Iye amaakonda iwo ndi m'mene Iye aliridi.
3. Njira yochotsera kupalamula wao ndi kusatetezeka, kubwezeretsa kudziwika kwao ndi phindu monga ana a Mulungu.
4. Njira yobwezeretsa malingaliro a cholinga chawo, chifukwa chao chokhalirako, kapena tsogolo lawo.
5. Zonse ziri pamwambapa zima funika nthawi. Adamu ndi Eva anataya moyo wao, choncho iwo amafunika dongosolo la moyo ogwirizitsa powapatsa iwo nthawi kuti asankhe ndi kusimikiza.
6. Pamene akupanga zonsezi, Mulungu ayenera kukhalabe ndi malingaliro a chirungamo. Iye sanganyalanyaze kupanduka kwao ndikuti ziri bwino. Pamene Mulungu m'chifundo chake sakulola zotsatira zozadza za chisankho chao kuwagwera iwo. Adamu ndi Eva adakalibe kuyenera kulawa zochitika za zotsatira za chisankho chao kuti iwo ayambe kuyamikira zolakwa zimene iwo anasankha kuchita.

Ntchito ya Yesu mu utumiki Wake, kufa ndi kuuka zapereka yankho ku mfundo zonse zisunu ndi chimodzi. Ndani angamvetsetse mphamvu ya

mtanda wa Yesu? Ichi ndi chakuya kwambiri kuposa kungochotsa ntchito zathu zolakwika; ndizakuya kwambiri.

Kodi simungagwade inu ndikuyang'ana pa mtanda pompano ndi kuona kumasuka kwanu kuchokera ku Mtengo wa batire lolimba? Inu mukutha kumva mau ochokera kumwamba kunena kuti inu ndinu mwana Wake okondedwa amene Iye amakondwera? Kodi inu simungathe kusiya kupalamula kwanu konse, kuipidwa, kunyada ndi m'kwiyo pa Iye? M'ngolola chidzalo cha chimwemwe Chake chitsefukire moyo wanu pompano. Inu mungathe kupanga choncho ngati simunatero kale. Chinsinsi chothawa Mtengo wa batire lolimba ndikusalolanso kukhala kapolo, koma mwana wamwamuna kapena mkazi.

17. Kugwa Kwa Babulo

Inakantha ngati mphenzi. Magulu a galimoto za nkondo a German anathamangira m'minda ya Holland ndi France, ndipo m'usiku umodzi maikowa anali pa nkondo yaikulu ya akasinja a Nazi. Kukhala m'dziko lotanganidwa nkofoketsa kwambiri. Abambo anga amakhala m'nthawiyi m'mzinda wa Assen kum'poto kwa Holland.

Amuna anapanikizidwa m'kutumikira m'akasinja ankhondo a German. Obvumbula nkhanu za chinsinsi anali tcheru kuwaulula iwo kwa apolisi woopsa a chinsinsi, ndipo pa ola lililonse mwina angamve kugogoda pa khomo ndipo okonedwa awo angatengedwa, osadzaonedwanso. Ulamuliro wa Nazi unaonetsa zidzindikiro zonse za Mtengo wa batire lolimba, mzimu wakulamulira umene utha kuchotsa onse owatsutsa, kulumulira kudzera m'mantha ndi kuonetsa mphamvu ndi kukhutira m'nkhanza.

Kulandidwa ndi kutha kwa chuma chake, olema kuchokera ku singa zowapsinja zimene zinaamanga, Holland sanakonzekere nyengo yachisanu ya 1944. Iwo sanathe kusiya nyumba zawo chifukwa cha mantha kuti pamene iwo akubwera sakanapezanso, atalandidwa nkhuu zawo. Zikwi zikwi m'mizinda anaonongeka chifukwa cha njala ndi kudzidzira. Kutenga nthawi yayitali bwanji kupirira mavutowa?

Potsiriza ma German anabwerera kwao, kuphwasula maulalo, kuononga zida ndi kusiya kuononga kwakukulu m'mene akanathera. Abambo anga akukumbukira aliyense amavina m'misewu ndipo atsirikali am'gwirizano

kugawa chakudya. Chinali chinthu chovuta kukhulupirira kuti nkondo yatha, ufulu pamapeto!

Mzimu wa Kaini ulibe ndi moyo, ndipo buku la Chibvumbulutso likubvumbulutsa kuti Yesu asanabwerenso ulamuliro, osatetezeka, nsanje ndi mzimu wachabechabe uzakhala ndi chionetsero chomalidza cha mphamvu iwo usanaonongedwe. Yohane akufotokoza iwo monga chirombo cha mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi chimene chikutuluka m'nyanja.

Ndipo ndinaimirira pa mcenga wa nyanja. Ndipo ndinaona chirombo cirikuturuka m'nyanja, cakukhala nazo nyanga khumi, ndi mitu isanu ndi iwiri, ndi pa nyanga zace nduwira zacifumu khumi, ndi pamitu pace maina a mwano. Cibvumbulutso 13:1

Chirombochi chipatsidwa mphamvu zazikulu ndi ulamuliro pa amitundu onse pa dziko, ndipo dziko lonse likupembedza ndi kugonjera iwo okha ku mphamvu ya chirombo.⁴⁵ Mphamvu za chirombochi zikuima kutsutsana ndi ubale wathu ndi Mulungu amene analenga kumwamba ndi dziko lapansi. Chikufuna chipembezo kwa ichochokha.

Chifukwa chimene chirombochi nkosavuta kutembenuza dziko lonse kuchitsatira ndi chifukwa chimayenda pa Mtengo wa batire lolimba. Chimayankhula chiyankhulo chimene ife tonse timayankhula. Chimatirimbikitsa kupeza chidzindikiro chathu ndi zimene ife takwanitsa ndiponso tachita, ndiponso

chimatirimbikitsa ife kukumana ndi Mulungu pa mfundo zathu, kubweretsa nsembe ya ife eni yopanda mwazi ndi kuyembekezera Mulungu kutsatira ndi kulandira kupembedza kwathu. Mbali yayikulu ya dziko iri kale pansu pa mphamvu ya chirombochi koma osadzindikira ichi. Pamene dziko likana mfundo za ufulu ndi kubwerera ku ulamuliro wa dziko lonse kupyolera m'mantha ndi mphamvu, izi zidzangokhala chionetsero chakunja za zomwe zabisika mwakuya m'mtima mwa aliyense wa ife. Mulungu sikuti wangokhala osachita kanthu. Iye akutumiza utenga omaliza osuntha kuchenjeza dziko lonse kuti asagonjere ku mphamvu ya chirombochi.

⁴⁵ Chibvumbulutso 13:2, 7

Uthenga ukubwera m'njira ya mauthenga atatu. Uthenga oyamba ukuitana mtundu wa munthu kukhala tcheru ndi kutikumbutsa ife kupembedza Mulungu amene analenga kumwamba ndi dziko lansi. Ukutirodzera ife ku nsembe ya Yesu ndi kutikumbutsa ife kuti nsembe ya Kaini siingathe kulandiridwa ndi Mulungu. Ife sitingathe kupeza kukonderedwa ndi Mulungu, chifukwa chipulumutso chathu chinagulidwa kudzera m'mwazi mwa Nkhosa.⁴⁶

Mulungu ndiyeno akutikumbutsa ife za choonadi chofunikira kwambiri. Iye akufotokoza m'chirankhulo ichi:

Ndipo anatsata mngelo wina mnzace ndi kunena, Wagwa, wagwa, Babulo waukuru umene unamwetsako mitundu yonse ku vinyo wa mkwiyo wa cigololo cace. Cibvumbulutso 14:8

Chifukwa chani Mulungu akugwiritsa ntchito liwu loti Babulo? Ife tikamayang'ana mu Baibulo tikupeza kuti Nimrode ndi amene anamanga mzinda wa Babulo. Nimrode anali ndi khalidwe lochititsa chidwi kwambiri. Baibulo limatiuza ife, "Ndipo kuyamba kwace kwa ufumu wace kunali Babele, ndi Ezeke, ndi Akadi, ndi Kaline, m'dziko la Sinara."⁴⁷ Nimrode ndi munthu oyamba olembedwa kukhazikitsa ufumu wa iye mwini. Nzochitsa chidwi kuona Nimrode pa nthawi ina yake anakwatira mai ake – banja losokonekera ndithu! Palinso maganizo ena kuti Nimrode anapha bambo ake kuti akwatire mai ake. Mulimonse, nyumba ya Nimrode sinakhazikike pa mfundo za ufumu wa Mulungu, m'mene maubale a banja ali opatulika.

Kotero kuti kupanda chitetezo kwa Nimrode kwakukulu kwambiri m'moyo wa m'nyumba mwake moti iye anayamba kukhala odziwika ndi zimene iye anapanga, m'malo mwa amene anamlenga. M'Genesis chaputala 10, Baibulo likundandalika mibadwo ya mtundu wa anthu. Munthu aliyense amadziwika ndi dambo ake. Kudziwika kwao kunakhazikitsidwa ndi maubale a mabanja awo. Iyi ndi njira imene ufumu wa Mulungu umayendera. Nimrode komabe, anakhala odziwika chifukwa chokhala osaka wamphamvu ndi olamulira wa mphamvu.

⁴⁶ Chibvumbulutso 14:6, 7

⁴⁷ Genesis 10:10

Lye ndiye mpalu wamphamvu pamaso⁴⁸ pa Yehova: cifukwa cake kunanenedwa, monga Nimrode mpalu wamphamvu pamaso pa Yehova. Ndipo kuyamba kwace kwa ufumu wake Kunali Babele, ndi Ezeke, ndi Akadi, ndi Kaline, m'dziko la Sanara. M'dziko momwenso iye anaturuka kunka ku Ashuri, namanga Nineve, ndi mudzi wa Rehoboti, ndi Kala, ndi Resene pakati pa Nineve ndi Kala: umenewo ndi mudzi waukuru. Genesis 10:9-12

Nimrode, wokakamidzidwa ndi kusatetezeka kwake, anamva kufunikira kuziyetsa yekha. Kotero anayamba kumanga mizinda ndiyeno iye anayamba kupanga magulu a nkondo kuti agonjetse mabanja a mafuko oyandikana nawo. Olemba mbiri odzindikira akulemba motere:

Ulamuliro wa olamulira oyambirira umakhazikika pa maganizo a abale, ndipo kukwera pa ufumu kunali chithunzi cha kulamulira kwa makolo. Nimrode m'malomwake, anali m'gawo layekhayekha, ndipo anthu akangokhala ali m'chigawocho potsawerengera za ubale wawo. M'mbuyomu kunali kukula kwa mafuko – mabanja – Anthu; tsopano kuli mtundu, gulu la Ndale – Dziko.⁴⁹

Pafupifupi dziko lonse lapansi lero likutsatira m'mapazi a Nimrode. Maboma lero ali a ndale ndi gawo, osati a mafuko ndi osamukasamuka.

Ndizochitsa chidwi kuona dongosolo Nimrode anatsata kuti amange dziko la ndale. Mulungu anayamba kunena za dongosololi ndi mzinda oyamba kumanga, umene umatchedwa Babulo. Dzindikirani phata la m'mene Babulo anakulira m'mitima ya anthu:

1. Zimayamba ndi ana amene sanakonedwe ndi azibambo awo.
2. Ndiyeno, chifukwa cha zotsatira za kusatetezeka, mowirikiza amafuna kuvomerezeka.

⁴⁸ Liu loti “pamaso” lingathanthauzenso “motsutsa”

⁴⁹ AT Jones, Empires of the Bible, (Review and Herald Publishing, 1904) p 51

3. Chilakolako chofuna kuvomerezeka nthawi zambiri chimaakakamiza motsimimidwa kupeza njira zochotsera kuperewera ndi uchabechabe wao.

Ichi ndi chinsinsi chimene chimapanga vinyo wa Babulo kukhala wachibaba. Ndi angati a ife amene tinakhomedwapo ndi maganizo opanda pake, kapena kutsimikiza kuonetsa ena kuti tiri nazo zotiyenereza? Ndi angati a ife tamvapo kuti khama lathu lomusangalatsa Mulungu lakhala lolephereka ndithu, ndipo palibenso mfundo yoti tingayesenso? Ndi angati a ife amene tagwidwapo kulimbirana mphamvu ku ntchito, ku sukulu, kapena ku mpingo ndi kumva kapena kuyankhula mokwiya kapena mau okhazula ngati njira yozitetezera kapena kuyesa kukulitsa tima ufumu tathu? Kodi dziko lonse silikumwa ku chikhochi? Ngati tikuchita mwa njirayi ndiyeno sitiri akapolo enieni a Babulo?

Kotero kugwa kwa Babulo kukutanthauzanji? Mau oti, “Babulo wagwa,” akuchokera ku Yeremiya 51:8 ndipo nkhani yake iri pa Yeremiya 50 ndi 51.

Mu Yeremiya 50, Mulungu akufotokoza anthu Ake monga nkhoa zotayika amene asocheretsedwa ndi amene ayiwala malo awo odikha. Anthu a Mulungu kwenikweni agwidwa ukapolo ndi Babulo ndipo ambiri a iwo ayiwala kwao koono, malo awo odikha.

Koma Mulungu sanaiwale ana Ake. Iye akupereka lonjezo lokongola lotsatirali:

Yehova wa makamu atero: Ana a Israyeli ndi ana a Yuda atsautsidwa pamodzi; ndipo onse amene anawagwira ndende awagwiritsitsa; akana kuwamasula. Mombolo wao ngwa mphamvu; dzina lace Yehova wamakamu: adzawanenera mlandu wao ndithu; kuti apumitse dziko lapansi, nadzidzimutsa okhala m’Babulo. Yeremiya 50:33, 34

Ndiyeno m’chaputala 51 ife tikuwerenga zotsatirazi:

Thawani pakati pa Babulo, yemwe apulumuke moyo wace; musathedwe m’coipa cace; pakuti ndi nthawi yakubwezera cilango; Yehova adzambwezera iye mphoto yace. Babulo

wakhala cikho ca Golidi m'dzanja la Yehova, amene amaledzeretsa dziko lonse lapansi; amitundu amwa vinyo wace; cifukwa cace amitundu ali ndi misala. Babulo wagwa dzidzidzi naonongedwa; mumkuwire iye; mutengere zowawa zace bvunguti, kapena angacire. Tikadaciritsa Babulo koma sanacire; mumsiye iye, tipite tonse yense ku dziko lace; pakuti ciweruziro cace cifikira kumwamba, cinyamulidwa mpaka kuthambo. Yehova waturutsa cilungamo cathu; tiyeni tilalikire m'Ziyoni nchito ya Yehova Mulungu wathu. Yeremiya 51:6-10

M'nkani ya chaputalachi, anthu a Mulungu agwidwa ndende ndi Babulo. Iwo atsocheretsedwa, koma Mulungu awapulumsa iwo, osati chifukwa iwo ali oyenera, koma chifukwa ndi ana Ake. Pamene mau, "Babulo wagwa," ndi mau a chiweruzo ndi kutsutsika, nthawi yomweyo ndi a lonjezo la ufulu kwa Israyeli, chifukwa Babulo anagwira Israyeli ndende.

Kugwa kwa Babulo kuli m'uthenga wa M'ngelo Wachiwiri kukumasula Israyeli wa uzimu kuchokera ku kusatetezeka, ku uchabechabe, ndi ku mzimu wolamulira kutikakamiza ife ku uchimo. Pamene ife tadzindikira kuti ndife olandiridwa mwa Okonedwa, kuti ndifedi ana a Mulungu kupyolera mu nsembe ya Yesu, kusatetezeka kwathu konse ndi uchabechabe zimatsedwa, ndipo ife timaima a ufulu monga ana a Mulungu.

Mauthenga a Angelo Atatu amatchedwanso Uthenga wa Eliya, ndipo simwangozi kuti mbali yomaliza m'Malaki 4:6 akunena kuti Mulungu adzabwezera mitima ya atate kwa ana, ndi mitima ya ana kwa atate ao. Mu mwau ena, mphamvu ya uthengau yidzamasulidwa pamene ife takhulupiriradi kuti ife ndife ana a Mulungu, osati chifukwa cha zimene tachita, koma zimene Yesu yekha watichitira ife. Choka Babulo ndi mfundo zako za Mtengo wa batire lolimba. Osakhalanso kapolo, koma kupfuula "Abba Atate" ndikudziwa kuti inu ndinu mwana Wake okonedwa. Kupyolera mwa Yesu, ife ndife mfulu.

Nkhondo za Kudziwika ndi ulendo wa kuzipeza wekha. Uku ndi kuyitanira ku kuphunzira phindu lanu mu nkhani za ubale.

Miyoyo yathu yimavutitsidwa ndi mauthenga ambiri wotiuza ife kuti kupambana kumabwera kuchokera podzitsimikizira ife tokha ndi dziko kuti tiri nazo zotiyenerenza, kuti tiri ndi zinthu zoyenera. Ndi dongosolo lotiphunzitsa ife kuzimva a phindu ndi ofunika pamene takwanitsa ndi kuchita kufika pa mlingo wina wake. Zotsatira za dongosololi ziripo ndipo umboni wake siwabwino. Zikwizikwi za anthu amataya mtima ndipo mazanamazana a anthu pa tsiku amachotsa miyoyo yawo chifukwa chokhumudwa.

Ndikukuyitanirani kukuphunzira choonadi cha khalidwe la nkondo tirimo – nkondo za kudziwika ya zomwe zimathandauzira phindu ndi kufunika kwathu. Chiopsezo nchachikulu chifukwa ichi ndi moyo kapena imfa. Bukuli liri ndi ulendo wanga ndi mfundo ndinaphunzira pa njirayi. Ufulu ndi chinthu cha chibale koma bukuli likulemba msewu wanga ku ufulu.

**Adrian Ebens
Tatewachikondi.com**